


KWAWO KWAMTSOGOLO KWA MKWATI WA KUMWAMBA NDI MKWATIBWI WAPADZIKO LAPANSI

 Tiyeni ife tikhale chiyimire kamphindi, pamene tikuweramitsa mitima yathu tsopano pamaso pa Mulungu.

² Atate athu Akumwamba, ife ndithudi ndi oyamikira chifukwa cha mwayi wokhala pano lero, kusunkhana pamodzi mu Dzina la Ambuye Yesu. Ife tikupemphera kuti Inu mutikhululukire machimo athu, ndipo pamene ife tiri pano kuti tidzatembenezire tcheru chatu ku zinthu Zamuyaya ndi Moyo umene uli kudutsa chivundi ichi. Tsopano tikupemphera kuti Inu mutipatse ife malangizo Anu, a momwe tikuyenera kutembenekira, chimene tikuyenera kudzachita m'tsogolomu, ndipo ngakhale mu kukhalapo tsopano, kuti tipeze malo amene ife tiri. . . tinalonjezedwa.

³ Pali ambiri amene akudwala ndi osowa mdziko, ndipo sanamalize ulendo wawo. Ndipo mdani wathu wamkulu, osati mdani wathu kokha, koma mdani Wanu, wabwera kudzawafooketsa iwo ndi ku—ndi kudzaimitsa moyo wawo, ndi kuwatumiza iwo ku—manda mwachangu. Ndipo ife tikuwapemphera iwo, lero, kuti Inu ndi chifundo Chanu ndi chisomo, Ambuye, muwonjezere masiku awo mpaka ku nthawi yoikika.

⁴ Zaikidwa pa nsanja, kapena pa guwa, apa pali mipango ndi maphukusi. Ndipo kunjira mmaholo ndi kuzungulira malowa, kuli iwo amene ali pamachira, mzikuku, odwala ndi osautsika, ayima pakati pa omvetsera opanda nkomwe mphamvu zokwanira kuti aimirire.

⁵ O Mulungu Wamuyaya, Wodalitsika Uyo, Inu mumve pemphero lathu mmawa uno, kudzera mu Magazi a Ambuye Yesu; osati kuyang'ana pa mphulupulu zathu, koma podziwa kuti Iye anayima m'malo mwathu, ndipo Iye ndi Mmodzi amene akutiyimirira ife ku pemphero ili. Mulole wina aliyense achiritsidwe kwa ulemelero Wanu, Ambuye.

⁶ Dalitsani mipango iyi. Pamene iyo iti ikaikidwe pa odwala, mulole iwo akachire.

⁷ Ndipo tsopano, Atate, kufikira titayembekezera msonkhano wawukulu wa machiritso, ife tikukhulupirira kuti utsatira, muswere kwa ife njira ya Moyo, Ambuye, kuti ife tikhoze

kudziwa kudzera mu Mawu Anu chimene ife tikuyenera kuchita. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

⁸ Monga nthawizonse, uwu ukutengedwa kuti ndi umodzi wa mwayi wanga wapamwamba kwambiri, ndi kudzakhala mnyumba ya Mulungu ndi kudzayankhula kwa anthu Ake. Ndipo tsopano ndikudziwa kuti mwadzadza kwambiri, ndipo ndiri ndi phunziro lalitali kwambiri. Chotero ndine. . . Ine—ine ndikudalira kuti—kuti mukhala omasuka, momwe mungathere, mpaka ife timalize Uthengawu.

⁹ Tsopano, kwatentha, koma ndife othokoza chifukwa cha choziziritsa mpweyachi. Koma, gulu la kukula uku, sipangakhale choziziritsa mpweya chimene chingathe kusamalira izo, mwaona, chifukwa thupi lanu lomwe ndi chopukusa, pafupifupi madigiri nainte-eyiti, ndipo ilo mowirikiza likumatulutsa kutentha, ndi kukhala moyandikana pamodzi. Koma ine—ine ndikudalira kuti Mulungu akupangani inu kuti mukhale momasuka basi monga Iye angathere.

¹⁰ Ndipo pamene ife tiri muno, misonkhano yolipira monga chonchi, ine—ine sindikanati inu mubwere kuno, mwa njira iliyonse, ngati sindimaganiza kuti izo ndi zoti zikuthandizeni inu, ngati sindimaganiza kuti izo zikuchitirani inu ubwino, ndi kuti inu mudzapindula nazo, pobwera. Ndiyeno, podziwanso kuti tiribe nthawi yochulukirapo kuti tichite izi, kuti ndife—ife tikufika ku—maora otsekera amene, ndi ine—ine ndikufuna kuipanga mphindi iliyonse iwerengeke, yomwe ine ndingathe, kwa Ufumu Wake. Ndipo tsopano ine ndikudalira kuti Ambuye Mulungu atidalitsa ife pamene ife tikusonkhana.

¹¹ Ndipo ndikufuna kuti ndichitire ndemanga, kuti, dzulo ndimapita kumalo osiyanasiyana, uko kukawona ena a odwala ndi osautsika, mu mamotelo, ndipo ine ndikuyenera kukumana ndi ena a mamanejala sabata ino, malo ena odyera. Monga, ine ndinali ku Ranch House sabata ino, kuno, ndipo amanenjala amandigwira chanza pamene ife timanyamuka. Ndipo anati, iye ananditchula ine, “M’bale Branham.” Ndinadabwa kuti iye wandidziwa bwanji ine. Ndipo iye anati. . .

Ine ndinati, “Kodi ndinu amanenjala?”

¹² Iye anati, “Ndine mwini.” Ndiyeno anati, “Eya, anthu anu akumabwera kuno kudzadya, kuchokera kumusi uko.” Anati, “Iwo. . .”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndikuganiza iwo amakuchulukirani inu.”

¹³ Iye anati, “Bwana, limenelo ndi limodzi la gulu labwino kwambiri la anthu limene ndinaliwonapo.” Iye anati, “Iwo ndi abwino kwenikweni.”

¹⁴ Ine ndinapita ku motelo dzulo, kukamuwona mtsikana amene ndimafuna kuyankhula naye, bambo ake ndi amayi

ake anali komweko, ndipo ndimayenera kuti ndipite kwa amanenjala kuti ndidziwe kumene—a- . . . chipinda chimene iwo anali.

15 Iye anati, “Ndipo ndinu M’bale Branham?” Kumeneko ndi kumtunda ku Oaks.

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

16 Iye anati, “Ndikufuna kugwira chanza chanu.” Iye anati . . . Anandidziwitsa ine kwa mkazi wake; banja labwino kwambiri. Iwo anati, “Munthu aliyense mu motelo iyi wabwerera misonkhano yanu. Ife tinawasungira iwowo.” Ndipo anati, “Makasitomala athu ena onse tinawakana.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndikukuthokozani inu chifukwa cha zimenezo.”

17 Iye anati, “M’bale Branham, limodzi la gulu labwino kwambiri la anthu amene ine ndinayamba ndawawonapo, ndi anthu amene amabwera kuno, amene amakhala pa misonkhano yanu.”

18 Ine ndinapita usiku watha kwa mzanga, Bambo Becker kumusi kuno, ndipo ine nthawizonse ndinkakonda masangweji ake. Iye ndi wotero . . . Iye, ine ndinamudziwa iye pamene ine ndinali mnyamata; ndinamudziwa iye moyo wanga wonse. Panali awiri atakhala pamenepo ochokera kumusi ku—malo akale, kumusi ku Riverside Hotel kumusi uko. Chotero iwo . . . Bambo Becker anati, “Billy?”

19 Ine ndinati, “Ndi chiyani icho, Homer?” Ife timadziwana bwino lomwe.

Iye anati, “Ine ndimawadyetsa anthu anu onse kumtunda uko.”

20 Thuu handirede ena, kapena chinachake, Lamlungu lirilonse, amadya ku Blue Boar. Ndipo kulikonse kumene ndimapita, ndimamva ndemanga za momwe inu muliri abwino.

21 Bambo uyu anati, “Kumusi ku—Riverview kumusi uko,” anati, “malo onsewo atengedwa ndi anthu amene abwerera msonkhano.” Anati, “Pakhala mazana omwe alephera kuti adzalowe.”

22 Chotero, kuti mukhale chimenecho, kwa ine ndinu mchere wa dziko lapansi. Ine—ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti ndiri ndi mwayi wolalikira kwa anthu amene ngakhale ochimwa ndi anthu . . . Ine sindikunena kuti anthu awa ndi ochimwa, koma ine ndikutanthauza anthu amene, amalonda ndi ena otero, amene anganene kuti ndinu anthu abwino, ndipo iwo amakuyamikirani mu bizinesi yawo, pozungulira malo awo. Inu mukudziwa, ndiko kukhala amchere. Ine ndikuyamikira zimenezo, khalidwe lanu, momwe mumasamalira zinthu.

23 Ine nthawizonse ndimati, “Ngati wina abwera ndipo alibe, alibe ndalama zolipirira bilu yake, mungondiyimbira ine.” Mukuona? Ine ndinati, “Ife tidzachita chinachake pa izo.” Ndipo ine ndinati, “Nthawizonse muziwadyetsa iwo, kaya iwo ali ndi ndalama kapena ayi.” Mwaona, chirichonse chikhoza kuchitidwa.

24 Ine ndikumverera kuti ndinu ana anga. Ndinu—ndinu nyenyezi zimene ine... Ngati ndingadzakhale nayo imodzi ndikadzafika kumeneko, inu mudzakhala ngale imeneyo, gawo lowala kwambiri, mu—mu korona wa utumiki wanga. Pamene iwo udzavekedwa korona, inu mudzakhala ngale imeneyo.

25 Ndipo ine ndakhala ndikukuuzani inu, mu nthawi zapitazo, za Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, Mibadwo ya Mpingo, ndi zinthu zimene—zimene zakhala zikuchitika.

26 Ndipo tsopano, mmawa uno, ine ndiri ndi phunziro lofunika kwambiri. Kwa ine, ilo ndi lodalitsa kwambiri. Ine ndikuyembekeza ilo likukhudzani inu mwanjira yomweyo. Ndipo ngati ine ndingalipereke ilo mu kudzodza kumene ndinalandirira ilo, zingakhale zodabwitsa, koma izo zikhala kwa Mulungu kuti achite izo.

27 Ndakhala ndikukuuzani inu za *kumene* ndi *chimene* chikuchitika, ndipo tikuwona zinthu zonsezi zikuchitika.

28 Tsopano ndikuyankhula, mmawa uno, pa: *Kwawo Kwamtsogolo Kwa Mkwati Wa Kumwamba Ndi Mkwatibwi Wapadziko Lapansi*, kumene iwo ati adzakakhale. Ndipo, pakuti, ine ndikudalira kuti mwa chisomo cha Mulungu ndife tonse gawo la chuma chachikulu cha Mulungu chimenecho.

29 Ndipo tsopano ine—ine ndikudalira kuti mupirira nane, mukhale ndi Mabaibulo anu, mapensulo anu, kapena chirichonse chimene inu mungachite kuti muwerenge ndi ine, chifukwa ine ndilozera ku Malemba ambiri. Kuyesetsa kuti ndimalizitse mu nthawi yokwanira kuti tikhale ndi pemphero kwa odwala; ndipo ine ndinalonjeza zimenezo. Kubwera, kupempherera kwa kanthawi kakang’ono kotsiriza, mzipinda ndi pozungulira, kwa iwo amene ali pafupifupi opanda thandizo ndi opanda chiyembekezo.

30 Ndipo, Ambuye akalola, ine mwinamwake ndidzakhala ndi msonkhano wina pa sikisitini, basi mwina pemphero la odwala.

31 Ndiyamba tchuthi changa tsopano. Kuyambira Januwale wathayu, ndakhala ndikuyendayenda, ndipo ndikubwerera kuno. Ine ndingokhala, ndikuyenera kutengera banja langa ku Tucson mmawa, ndipo kenako ndidzabwerera kuti ndidzakhale ndi nthawi kumusi kuno ku Kentucky, ndi ena a zimzanga, kusaka, ndi kusaka agologolo, kwa masabata angapo, kapena mwinamwake seveni kapena eyiti, masiku teni, chirichonse chimene icho chiri, pokhapokha ngati Ambuye atanditsogolera ine kwinakwake. Ine sindimadziwa nkomwe, basi kumene inu

muti mudzakakhale; ife sitimadziwa konse zimenezo, chifukwa izo ziri mmanja a Mulungu, Mulungu yekha.

³² Tsopano pa phunziro lalikulu ili, ife—ife. . . Ine ndikuganiza, ngati ine ndingatenge nthawi yanga pa izi, chifukwa inu muyenera kubweretsamo zinthu zambiri, izo zingatenge masabata. Koma ndalemba Malemba ena, zolemba zina, kuti ndingomenya mfundo zazikulu za izo, kufika pamene izo zingakupangeni inu kuwerenga.

³³ Ndiye posachedwapa, mwinamwake, Ambuye akalola, mu Okutobala, ine sindikudziwa kuti ndi liti, koma pamene Iye adzapereke, ine ndikufuna kuti ndidzakhale ndi—masiku pang’ono, basi a msonkhano wowirikiza, pa mutu wa 12 wa Chivumbulutso, kuti zidzagwirizane ndi izi apa. Oh, ine ndikukhulupirira izo zingadzakhale zazikulu. Izo zingadzakhale basi. Zingadzakhale zopambana kudzawona momwe Iye anachitira.

³⁴ Ndiye, ife kubwera pamodzi tsopano, ndinanena usiku wathawu, ine ndinati, “Inu mukudziwa, pamene ine. . .” Mmawa, monga mmawa uliwonse, ine ndimaganiza, “Pamene ine ndibwera kuno, ine ndikamuzindikira aliyense wa abwenzi anga amene ali kumeneko.” Tsopano ine ndizichita motani zimenezo?

³⁵ Kukhala ndi ine pano, monga mzanga wabwino, Dokotala Lee Vayle wakhala kumbuyo kuno, mkazi wake wokondedwa ndi mwana wamkazi. Ndi M’bale Roy Borders, ndipo, ine ndikuganiza, M’bale Ruddell, M’bale Beeler, ndi M’bale Palmer, ndi M’bale Jackson. Ndipo, oh, mai, a—a. . . Abale okondedwa amenewo ochokera ku madera onse osiyanasiyana! M’bale Anthony Milano, ndipo, oh, paliponse pamene iwe ungayang’ane, iwe umamuwona m’bale wina! Kuchokera kumusi mu Arkansas, ine sindikuganzira za dzina lawo; M’bale John, M’bale Earl Martin, ndi M’bale Blair. Ndipo, oh, alipo basi. . . inu. . . Ndi zopanda malire basi, inu mwaona. Ndine wokondwa kukhala ndi gulu ngati limenelo litasonkana mondizungulira ine pamene ndikuphunzitsa Mawu a Mulungu, amuna amene ine ndikuganiza kuti ndi amuna ochilimika, amuna enieni a Mulungu.

³⁶ Ndine wothokoza chifukwa cha kachisi wamng’ono uyu. Ndine wothokoza chifukwa cha zitseko zake zisanu zotseguka kwa anthu. Khomo lililonse. . . Ife tiri ndi madikoni anayi pano, amuna odzadzidwa-Mzimu; matrastii anayi, amuna odzadzidwa-Mzimu. Zimenezo ndi awiri pakhomo lililonse. Ndipo iye ali ndi zitseko ziwiri kutsogolo, za abusa awiriwo, alishi.

³⁷ Ndife okondwa kukhala nanu inu; woyamikira kwa Mulungu chifukwa cha izi. Iye akudalitseni inu nthawizonse.

³⁸ Tsopano tikufuna kuti tiyime mphindi yokha, pamene ife tikuwerenga kuchokera ku Petro Wachiwiri mutu wa 3, ndiponso kuchokera mu Bukhu la Chivumbulutso 21.

³⁹ Pamene ife tikuyima, O Ambuye, dzadzani mitima yathu ndi chisangalalo chifukwa cha kuwerenga kwa Mawu Anu, podziwa kuti Yesu ananena, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzalephera konse.” Mudziwenso kuti Iye anati, “Malemba onse akuyenera kukwaniritsidwa.” Ndipo pamene ife tikuwerenga zinthu izi, mulole ife tikhale ndi kumvetsa kuchokera kwa Inu, ora limene ife tikukhalamo. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mlembi wa Bukhulo. Amenii.

⁴⁰ Petro Wachiwiri 3.

Kalata yachiwiri iyi, okonedwa, tsopano ndikulemba inu; mu zonse ziwiri zimene ndikutsitsimutsa mtima wanu woyera mwa njira yokumbutsa:

Kuti inu mukumbukire mawu amene ananenedwa kale ndi aneneri oyer, ndi a malamulo a ife atumwi a Ambuye ndi Mpulumutsi:

Podziwa ichi poyamba, kuti mmasiku otsiriza kudzabwera onyoza, akuyenda monga mwa zilakolako zawo,

Ndi kunena, Liri kuti lonjezo la kudza kwake? (Ngati izo sizikumana ndi mkazi wachikunja uyu...)... popeza makolo anagona, zinthu zonse zikupitirira monga momwe iwo anali pachiyambi cha chirengedwe.

Pakuti ichi iwo ndi osadziwa mwadala, kuti ndi mawu a Mulungu miyamba inali yakale, ndipo dziko lapansi linayima kunja kwa madzi ndi mmadzi:

Momwemo dziko limene linali nthawi imeneyo, pomizidwa ndi madzi, linawonongeka:

Koma miyamba ndi dziko lapansi, zimene tsopano ziripo, ndi mawu omwewo zasungidwa, zasungidwira ku moto kufikira tsiku la chiweruzo ndi chiwonongeko cha anthu opanda umulungu.

Koma, okonedwa, musakhale osadziwa chinthu chimodzi ichi, kuti tsiku limodzi liri kwa Ambuye ngati zaka sauzande, ndipo zaka sauzande ngati tsiku limodzi.

Tsopano, Ambuye sazengereza zokhudza lonjezo lake, monga ena amachiyesa kuzengereza; koma ndi kuleza mtima kwa ife, osafuna kuti wina awonongeke, koma kuti onse akhoze kubwera ku kulapa.

Koma tsiku la Ambuye lidzabwera ngati mbala mu usiku; mu...mmene miyamba ndi dziko lapansi, ndi

phokoso lalikulu. . . zidzapita ndi phokoso lalikulu, ndipo zammwamba zidzasungunuka ndi kutentha kwakukulu, ndipo dziko lapansi ndi ntchito ziri momwemo zidzathethedwa.

Powona ndiye kuti zinthu zonsezi zidzathetsedwa, tikuyenera kukhala munthu wotani ife mu kayankhulidwe koyera konse ndi umulungu,

Kuyembekezera kufulumira kwa kudza kwa tsiku la Mulungu, mmene miyamba poyaka moto idzathetsedwa, ndipo zammwamba zidzasungunuka ndi kutentha kwakukulu?

Komabe ife, monga mwa lonjezo lake, tikuyembekezera miyamba yatsopano ndi dziko latsopano, momwe mukhalitsa chirungamo.

Chifukwa chake, okonedwa, poona kuti ife tikufunafuna zinthu zotere, chitani changu kuti musapezeke. . . mupezeke ndi iye mu mtendere, opanda banga, ndi opanda chilema.

Ndipo kuwerengera kuti kuleza mtima kwa Ambuye ndiko chipulumutso; ngakhale monga wokonedwa wathu. . . Paulo. . . malingana ndi nzeru yopatsidwa kwa iye walemba kwa inu;

Monganso. . . makalata ake onse, akuyankhula m'menemo za zinthuzo; . . . zomwe nthawi zina ndi zovuta kuzimvetsetsa, zimene iwo amene ali osaphunzira ndi osakhazikika alimbana nazo, alimbana, monga—monga iwo achitiranso ndi malemba ena, ku chiwonongeko chawo chomwe.

Inu chotero, okonedwa, powona kuti mukudziwa zinthu izi kale, chenjerani kuti inunso, potsogozedwa. . . kulakwa kwa oyipa, kungagwere kwa inu. . . kukhazikika.

Koma mukule mu chisomo, . . . mu chidziwitso cha Ambuye ndi Mpulumutsi Yesu Khristu. Kwa Iye kukhale ulemelero kuyambira tsopano ndi ku nthawi zonse. Amen.

⁴¹ Tsopano mu—Chivumbulutso cha Khristu, mu mutu wa 21, ine ndikuwerenga Mawu awa.

Ndipo ine ndinawona kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano: pakuti kumwamba koyamba ndi dziko loyamba zinachoka; ndipo panalibenso nyanja.

Ndipo ine Yohane ndinawona mzinda woyera, Yerusalemu watsopano, ukutsika kuchokera kwa Mulungu kuchokera kumwamba, wokonzedwa ngati mkwatibwi wokongoletsedwera mwamuna wake.

Ndipo ndinamva phokoso lalikulu likuchokera kumwamba likuti, Taonani, kachisi wa Mulungu ali ndi anthu, ndipo iye adzakhala ndi iwo, ndipo iwo adzakhala anthu ake, ndipo Mulungu mwiniwake adzakhala ndi iwo, ndi kudzakhala Mulungu wawo.

Ndipo Mulungu adzapukuta misozi yonse mmaso mwawo; ndipo sipadzakhalanso imfa, kapena kudandaula, kapena kulira, ngakhalenso sikudzakhala zowawa: pakuti zinthu zakale izo zapita.

Ndipo iye amene anakhala pa mpando wachifumu anati, Taonani, ndikupanga zinthu zonse zikhale zatsopano! . . . iye anati kwa ine, Lemba: pakuti mawu awa ndi owona ndi okhulupirika.

Ndipo iye anati kwa ine, Zatha. Ine ndi Alfa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza. Ndipo ndidzampatsa iye wakumva ludzu akasupe a madzi a moyo kwaulere.

Iye amene agonjetsa adzalandira zinthu zonse; ndipo ndidzakhala Mulungu wake, ndipo iye adzakhala mwana wanga.

Tiyeni tipempherenso.

⁴² Ambuye Yesu, ndi lonjezo loterolo ndi kuyankhula kolimba ngati mmene Yesu Mwiniwake ndi mtumwi watipatsira ife za ora limene ife tikuliyandikira, tipatseni ife, O Ambuye, za chitsogozo Chanu, kuti ife tithe kudziwa momwe tingayandikire ilo mu njira yolondola. Chifukwa, ilo likubwera, ife tikudziwa. Malemba akuyenera kukwaniritsidwa, ndipo izo zidzakhala chomwecho. Ndipo tsopano, Ambuye, ife tikupempha chifundo Chanu kachiwiri pa ife tonse, pamene ife tikuphunzira Mawu Anu. Mukhale nafe ndipo muwafutukule Iwo kwa ife, Ambuye, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

Mukhoza kukhala pansii.

⁴³ Tsopano, ine ndikudabwa ngati pangakhale njira yoti mwina, mwinamwake iwo akhoza kuzimitsa magetsi a mu holo yayikulu, ndi kungowasiya iwo pa nsanja pano, zomwe mwina zingakhale zabwinoko, ndi kutenga mphamvu ya magetsi yinayo. Ife tinatsala pang'ono kuwotcha tharansifoma, usiku wina. Ndipo ngati woyang'anira angachite izo kwa ife, ife tingayamikire kuzimitsa nyali zapansi, nyali zazikulu zamu holo, kuzizimitsa. Ndiyeno ine ndikuganiza kuti mukhala ndi malo ambiri oti mudziwonera, kuti muzilemba.

⁴⁴ Tsopano, phunziro kachiwiri, kuti tilengeze ilo, limene tikuliyandikira—phunziro la: *Kwawo Kwamtsoyolo Kwa Mkwati Wa Kumwamba Ndi Mkwatibwi Wapadziko Lapansi.*

⁴⁵ Tsopano monga izo zakhala zikukhalira. . . Ine ndikungoyenera kuti ndichite izi. Kwatentha kwambiri kuno, mwaona. Inde, bwana. Monga ife. . . Ndikudziwa kuti

mkazi wanga samakonda kuti ine ndizichita zimenezo; koma, kuti, kuvula chikhotho changa. Basi kwatentha kwambiri kuno. Mwaona, inu muli ndi mpweya kunja uko, ndipo iwo wangodulidwa mu kakhola kakang'ono kuno, mwaona. Tsopano, mu—m'tsogolo, kapena . . .

⁴⁶ M'mbuyomu, kani, ife timaphunzira *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, Mipingo Isanu Ndi Iwiri*. M'bale Vayle ndi iwo akugwira ntchito pa izo tsopano, mokhulupirika, kuti aziyike izo mu mawonekedwe a bukhu.

⁴⁷ Ndipo powona zinthu zachinsinsi zonsezi zimene ife taziwona zikuchitika, ndiye ine ndikuganiza, nditatha kumvetisa izo, mu ora limene ife tikukhalamo, ndi udindo; palibe mmodzi amene angafune kuti akhale pansu mwanzeru ndi kuwunika chimene chanenedwa, ndi chimene chinalonjezedwa kuti chidzachitika, ndi chimene chachitika, koma chimene chikanakhoza kunena kuti zinthu zimenezo zakwaniritsidwa. Mukuona? Ndendende zimene Mulungu ananena kuti Iye akanadzachita, Iye anachita izo ndendende basi mpaka ku chilembo. Mukuona?

⁴⁸ Tsopano, ine ndikuganiza mu izi, kuti, posadziwa nthawi imene Ambuye Yesu angawonekere, ine ndinaganiza kuti izo zikanakhala zabwino, izo zinkawoneka zokondweretsa kwa Mzimu Woyera kuti ife tiyankhule pa izi, ndiye; ndipo mwinamwake kubwereranso kwa izo kachiwiri, kawiri kapena katatu, chifukwa sindidzakhala ndi nthawi yokwanira yotulutsa zonsezi.

⁴⁹ Monga momwe munamenya a—phunziro limene lingakhale lopunthwitsa pang'ono kwa wina, iwe sungapitirire nalo njira yonse kuti ukalipangitse ilo kumveka bwino, kenako nkubwereranso kuti udzawire phunziro lotsatira.

⁵⁰ Ndiyeno patsogolo mwake, mu...ngati Ambuye alola, ife tidzabwera mu Zisindikizo za 12, kapena ayi... Mundikhululukire ine. Mutu wa 12 wa Chivumbulutso, umene uli pakati pa Kudza kwa Ambuye ndi kutha kwa Malipenga, ndi zina zotero. Ife tiyesera kuzibweretsanso izo mmbuyo, kuti tidzawonetsere chimene Satana ali, ndi chimene iye anachita, kumene iye anachokera, chimene cholinga chake chiri, ndi momwe kukongola kwake kwakukulu kumene kunaperekedwa kwa iye kunapangitsa kugwa kwake. Chinyengo chake chinapangitsa izo kugwa; kukongola.

⁵¹ Kenako, momwe kuli kosatheka kwa munthu aliyense amene akufuna kuti aziyang'ana pa izo molondola, “mbewu” ya serpenti ija. Ndingapange chitsutso kwa izo, kwa aliyense, mwaona, amene angafune kuyang'ana pa izo, ndi—ndi mwamtheradi kumvetisa kwa wamba. Mwana akhoza kuziwona izo. Mukuona? Tsopano, ndipo ife tifika kwa izo nthawi ina.

⁵² Tsopano, ife tikumvetsa apa kuti Malemba awiri awa... Chifukwa chimene ine ndinawerengera Petro Wachiwiri mutu wa 3, ndi kufanizitsa izo ndi Chivumbulutso 21, iwo onse awiri apa akuyankhula phunziro lomwelo, koma Yohane sana—sanazilembe konse izo monga Petro anachitira. Mukuona? Ife tikumvetsa kuti Kwawo kwakukulu uku kwa Mkwatibwi kudzakhala kuno pa dziko lapansi.

⁵³ Ndipo tsopano ngati mungawerenge, monga ngati mutu 21, mutu wa 21 wa Chivumbulutso, mtumwi apa ananena, kapena mneneri ananena, kuti, “Ine ndinawona Kumwamba Kwatsopano ndi Dziko Latsopano.” Zikumveka ngati pakubwera chiwonongeko.

⁵⁴ Tsopano, momwe ine nthawizonse ndimapezera Mauthenga anga ndi mwa pemphero. Ine ndimakhala mu pemphero ndipo chinachake chimawulula kwa ine. Ndipo ine ndimadikirira pa icho maminiti pang’ono ndi kuwona ngati icho chiri cholondola, ndiye ine ndimachimverera icho chikuyandikira. Ndiyeno nthawizina ine ndimakhala ndikudikirira mpaka icho chitatulukira mu masomphenya. Koma pamene icho chiyamba kubwera, ndipo ine nkukhutsidwa kuti icho chikuchokera kwa Mulungu, ndiye ine ndimapita ku Lemba. Mwaona, Uko ndiko, chiyenera kukhala kutsimikizirao kwa chinthu chauzimu chirichonse chimene chachitidwa, chifukwa Baibulo ndi vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu; mwaona, Ilo ndi Thupi Lake.

⁵⁵ Ndipo tsopano, mmenemo, mwinamwake ine ndimapeza malo mu Lemba amene samamveka bwino basi, ndipo ine ndimadabwa. Ine ndimabwerera kachiwiri ku pemphero. Iwo amabweranso. Ndiye ine—ndiye ine ndimayamba ku—kufufuza Lemba langa.

⁵⁶ Tsopano, Baibulo lathu linalembedwa mu Chingerezi, ndipo mawu Achingerezi amasintha, nthawi zonse. Mwachitsanzo, monga Yohane Woyera 14, anati, “M’nyumba ya Atate anga muli nyumba zazikulu zambiri,” nyumba yayikulu mu nyumba. Chabwino, ndiye, inu, chimene inu mumachita ndi izo ndiye, ndi kuzibwezeretsa izo ku—ku chiyambi ndi kuwona chimene Yakobo ankanthauza, kapena kubwerera ku Chiheberi, kapena ku Chigriki, kuchokera ku kumasulira koyambirira. Ndipo mmenemo amati, “Mu Ufumu wa Atate anga muli nyumba zachifumu zambiri.” Chabwino, ndiye, inu mubwerere ku nthawi imene omasulira anamasulira King James, *ufumu* unkatchedwa, mu Chingerezi, “nyumba,” ndipo mfumu anali atate wa nthumwi zake. Icho ndi chifukwa chimene iwo anamasulira, “M’nyumba ya Atate Anga muli nyumba zazikulu zambiri.” Mukuona? Ndiyeno ukawatenga mawu amenewo ndipo iwe umayenera kuti uwasake iwo.

⁵⁷ Ndiye, inu mwaona, kuchokera ku kudzodza kumeneko...

Guwa ili mmawa uno, ine ndikuti, palibe nthawi imodzi limene linayamba lakhalapo chirichonse koma molunjika, Lembu. Umo ndi momwe *Mbewu ya Serpenti* ndi zinthu zina zonse izi zimabwerera. Mukuona? Mwa . . .

⁵⁸ Ndipo ndizo, kwenikweni, ngati munthu atangowerenga ndi kuti, “Mnyumba ya Atate anga muli nyumba zazikulu zambiri,” ngati iwe sunaimikire kuti uphunzire, kupemphera, iwe ukhoza kusokonezeka yense. Mukuona? Koma kumangopitirira kupemphera. Mulungu nthawizonse amakonza izo molondola, ngati izo zikuchokera kwa Mulungu.

⁵⁹ Tsopano, Yohane akufotokoza kusintha ndi a- . . . momwe izo zimafikira . . . Iye samafotokoza izo, kani, koma Petro amatero. Yohane anati, “Ine ndinawona Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano; miyamba yoyamba ndi dziko lapansi loyamba zinachoka. Kunalibenso nyanja. Ine Yohane ndinawona Mzinda woyera ukutsika kuchokera kwa Mulungu kuchoka Kumwamba, wokonzeka ngati Mkwatibwi wokongoletsedwera kwa Mwamuna Wake.” Koma, tibwerenso ku Petro Wachiwiri tsopano kuti tipeze, Petro akufotokoza m’mene izi zidzachitikire. Tsopano, ngati inu mungayang’ane pa chimene Yohane ananena, zikumveka ngati, “Pakuti miyamba yoyamba ndi dziko lapansi loyamba zinachokapo,” kuwonongedwa psyiti. Mwaona, ndiye, izo zikumveka zachilendo kwambiri. Chotero icho ndi chimene chinandikhudza ine, ndipo ndinayamba kuyang’ana mawu akuti, “kuchokapo.” Ndipo, tsopano, koma zikuwonekeratu kuti onse awiri awa, mtumwi ndi mneneri, ankayankhula za chinthu chomwe chomwecho.

⁶⁰ Ndipo tsopano, aponso, mu Bukhu la Yesaya, tsopano, kuti inu mukufuna kulemba Malemba awa, mu Yesaya 65:17. Yesaya, akuyankhula za Zakachikwi, zaka sauzande zija za kupumula kwa—kwa anthu a Mulungu. Yesaya anayankhula za izo, ndipo iye anati, “Ine . . . Panali a . . . Zinthu zakale zonse zinali zitapita,” ndi momwe iwo adzamangire nyumba, nkumakhalamo mmenemo. Ngati tikanakhala ndi nthawi . . . Mwinamwake tingotenga nthawi ndi—ndi kuwerenga izi miniti yokha, Yesaya 65, ndipo tiyeni tingowerenga kwa maminiti pang’ono apa. Ndipo ndi izi apa, kulondola, kwa ife. Tsopano, kuti tiyambe, Yesaya 65:17.

ndipo, taonani, *Ine ndilenga mmiyamba mwatsopano*
ndi dziko lapansi latsopano: . . .

⁶¹ Tsopano, Yesaya, mneneri, anali mmodzi wa aneneri amene analemba ndendende Baibulo lonse mu uneneri wake. Iye akuyamba ndi chirengedwe; mkati mwa Bukhu lake, pafupifupi mutu wa 40, akudzabwera pamenepo Yohane M’batizi, Chipangano Chatsopano; ndipo akudzathera apa, mu Bukhu lake, mu Chivumbulutso, mu Zakachikwi. Muli mabukhu

sikisite-sikisi mu Baibulo, ndipo muli mitu sikisite-sikisi mu Yesaya. Iye analemba ndemanga yathunthu.

⁶² Tsopano, ife tikupeza, apa tsopano iye akutenga mutu wa 65, mutu umodzi wowonjezera, ndipo iye akuyankhula za Zakachikwi. Zindikirani izo, kukongola kwake.

...taonani, Ine ndilenga kumwamba kwatsopano ndi...dziko latsopano: ndipo chinthu chakale sichidzakumbukiridwa, kapena kubwera mmaganizo. (Icho chikuyenera kuti "chidzachokepo.")

Koma khala—inukhale okondwa ndipo musangalale...ngakhale mu chimene Ine ndachilenga: pakuti, taonani, Ine ndilenga Yerusalemu wokondwa, ndi anthu ake osangalala.

Ndipo Ine ndidzakondwera mu Yerusalemu, ndipo ndidasangalala mwa anthu anga: ndipo liwu lolira silidzamvekanso mwa iye, pakuti...ngakhalenso liwu la kufuula.

Sipadzakhalanso mmenemo zoterozo...khanda la masiku, ndi...munthu wokalamba amene sanakwanitse masiku ake: pakuti mwana adzafa usinkhu wa zaka handirede; ndipo wochimwa wokhala ndi usinkhu wa zaka handirede adzayimbidwa mlandu. Ndiye adza...

Ndipo iwo adzamanga nyumba, ndi kudzakhalamo; ndipo adzabzala minda yamphesa, ndipo adzadya zipatso zake.

Ndipo iwo sadzamanga, ndi wina nkukhalamo; (ndiko kuti, munda wanu, mwana wanu ndi wolowa m'malo mwake, kapena ena mwa olowa m'malo anu)... iwo sadzabzala, ndipo wina nkudya kumeneko: (iwo akupanga kubzala kwawo kwawo ndipo nkumakhala mmenemo; iwo ali ndi Moyo Wamuyaya)...pakuti monga masiku a mtengo ndi masiku a anthu anga, ndipo anga aatali...osankhidwa anga adzasangalala nthawi yayitali ndi ntchito za manja awo.

Iwo sadzagwira ntchito pachabe, ngakhale kubalira mavuto; pakuti iwo ndi mbewu ya odalitsika a AMBUYE, ndi mphukira zawo limodzi ndi iwo.

⁶³ Tsopano zindikirani, apa ndi pamene ine nditi ndifikepo, pakapita kanthawi.

Ndipo padzakhala, kuti iwo asanayitane, ine ndidzayankha; ndipo pamene iwo ali chiyankhulire, ine ndidzamva.

Ndipo nkhandwe ndi mwanawankhosa zidzadyera limodzi, ndipo mkango udzadya udzu ngati ng'ombe:...fumbi lidzakhala chakudya cha serpenti.

Ndipo *iwu sadzapweteka* kapena *kuwononga mu phiri*
langa lonse lopatulika, atero AMBUYE.

64 Ndi lonjezo lotani, la aneneri awa ndi anzeru akulu, aphunzitsi a Baibulo, kalekale mmasiku aamakedzana, powona Tsiku laulemelero ili labwera!

65 Ndi ndime izi, wina akhoza kuganiza, kapena kutsogozedwa, kani, kukhulupirira kuti pulaneti yonse, ya dziko lapansi ili, idzawonongedwa, “Ine ndikupanga Kumwamba Kwatsopano ndi Dziko Latsopano,” mwaona, kuti miyamba idzachoka ndipo dziko lapansi lidzachoka, kuwonongedwa psyiti. Koma kuphunzira mwatcheru, ndi chithandizo cha Mzimu Woyera, tikhoza kuwona Choonadi cha izi; ndipo ndi zomwe tikulowamo.

66 Ndi mu mlengalenga mokha mozungulira iyo, ndi tchimo limene liri pa dziko lapansi, zimene ziti zidzawonongedwe. Mukuona? Tsopano, ife tikuzindikira kuti *miyamba* imatanthauza “mlengalenga mmwamba.” Mukuona?

67 Chimachita izo ndi chiyani? Izi ndiye, nthula iyi, ndi matenda, ndi imfa, ndi ndale, ndi mwamuna wochimwa, ndi mkazi wochimwa, ndi mizimu yoyipa, zonsezo zidzakhala zitapita ndi kuwonongedwa psyiti. Mukuona? Izo zikuyenera kuchitidwa mwanjira imeneyo, chifukwa ife tidzakhala pompano. Ife titsimikizira izo mwa Baibulo. Pomwe pano ndi pamene titi tidzakhalepo. Tsopano zindikirani, nthula, majeremusi, matenda onse ndi zinthu, zidzachotsedwa kwathunthu. Zonse izi, kukhalapo kwake kumene kuli padziko lapansi tsopano, machitidwe-opangidwa ndi anthu, ndale, tchimo, mitundu yonse ya mizimu yoyipa imene dziko layipitsidwa nayo, ndi mmiyamba monse pamwamba pathu muno, ndi moyipitsidwa ndi mzimu woyipa. Tsopano ife tipita mwakuya ndi motalikitsa, mu izi, mwaona.

68 Zonsezi ziripo mmiyamba, kapena mu mlengalenga, ndi dziko lapansi limene liripo tsopano. Dziko lapansi ili liri ndi zinthu zimenezo, koma ilo silinapangidwe kwa cholinga chimenecho. Tchimo linapangitsa izo kuti zikhale monga choncho. Mukuona? Ilo linapangidwa ndi Mulungu, Mlengi. Koma zonse . . .

69 Ndipo matupi athu onse, amene tikukhalamo tsopano, anayikidwa pa dziko lapansi pamene Mulungu analilenga ilo, chifukwa inu munachokera ku fumbi la dziko lapansi. Izo zonse zinayikidwa apa. Pamene Mulungu Mwiniwake analenga izo, inu munali mu kuganiza Kwake. Ndipo mwa Iye, Wamuyaya Wamkulu, munali lingaliro, limene liri chikhumbo Chake.

70 Ndipo tsopano tchimo linapangitsa zonsezi kuchitika. Ndipo Mulungu, kudutsa mu m’badwo uno, akusonkhanitsa zinthu Zake.

71 Satana akadali kuno. Ndicho chifukwa chimene zinthu zonsezi zimachitika. Iye akanali pano, ndipo mphamvu zake

zonse zoyipa zikanali pano. Zindikirani, ndicho chifukwa chimene dziko lapansi tsopano ndi lonyansa kwambiri. Ndi chifukwa chake nyansi ndi zinthu zopanda pake zomwe zimapitirira; kukhetsa magazi, nkondo, ndale, tchimo, chigololo, mitundu yonse ya zonyansa zimapitirira, ndi chifukwa chakuti Satana ndi wolamulira wa dziko lapansi lino ndi mumlengalenga umu.

Inu mukuti, “Mlenga- . . .?” Inde, bwana!

⁷² Zonse ziwiri miyamba ndi dziko lapansi tsopano zayipitsidwa ndi adierekezi amene angatinenere ife pamaso pa Mulungu. Yesu ali Pamenepo kuti azititetezera ife. Mukuona? Pamene otsutsa akupitirira kumatiloza chala, “iwo anachita *ichi*, iwo anachita *ichi*, iwo anachita *ichi*,” koma Magazi akuphimbabe. Iye anabwera kuti adzawombole Osankhidwa amenewo amene Iye anawawoneratu. Icho ndi chifukwa izo ziri zonyansa lero.

⁷³ Apa, mtumwi, mu Petro Wachiwiri apa, mutu wa 2, ndi ya 5 ndi a . . . ndi ndime ya 5 ndi ya 6. Inde, ndapapeza pamenepo. Iye akulozera ku magawo atatu a dziko lapansi. Mwaona, iye— iye akutenga magawo atatu a izo. Zindikirani momwe iye akuzibweretsera izo.

⁷⁴ “Dziko lakale linatuluka kuchokera mmadzi,” tsopano, limenelo linali dziko la chigumula.

⁷⁵ Tsopano, limene liripo, dziko lapakali pano limene ife tikukhalamo tsopano, analitcha ilo “dziko.”

⁷⁶ “Dziko lakale limene linatuluka mmadzi,” Genesis 1:1. Tsopano ndi “dziko” limene liripo tsopano. Ndiyeno, kachiwiri, iye akulozera kwa lina, “dziko limene lirinkudza,” Dziko Latsopano. Mayiko atatu; magawo atatu a dziko lapansi.

⁷⁷ Ndipo zindikirani momwe Mulungu akufotokozera momveka bwino kwa ife dongosolo Lake la chiwombolo. Oh, izi zinangokondoweza moyo wanga pamene ine ndinaziwona izo, momwe Iye amafotokozera momveka bwino kwa ife pano tsopano dongosolo Lake la chiwombolo. Tsopano tifanizitse zimene tikuziwona ndi maso athu omwe. Chimene Mulungu wachita kuti aliwombole dziko Lake, Iye wachita dongosolo lomwelo kuti awombole anthu Ake, pakuti Mulungu wosasinthika samasintha ayi mu chirichonse cha madongosolo Ake kapena chirichonse. Chinthu chaulemerero chotero!

⁷⁸ Momwe Iye anatitsogolera ife kwa Iyemwini, kuti adzakhale mwa ife, kudzera mu magawo atatu a chisomo; chimodzimodzi monga momwe Iye analitsogolera dziko mu magawo atatu, kuti abwere ku dziko. Monga Mulungu ati adzabwere ku dziko lapansi ilo litatha kudutsa magawo atatu osiyanasiyana a chiyeretso, umo ndi ndendende momwe Iye akubwerera kwa ife kudzera mu magawo atatu a chisomo. Ine ndinaphunzitsa

zimenezo pachiyambi; ine sindinasinthepo, kuyambira pamenezo. Ndi Mawu a Mulungu.

⁷⁹ Inu mukuyenera kusunga ma firii anu pamodzi, ma seveni anu, ma thwelofu anu. Mawerengero a Baibulo akuyenera aziyenda mwangwiro kapena inu mudzasokoneza chithunzi chanu chonse. Ngati simungathe kuzimvetsa izo, muzingopitirira kumapemphera. Inu muzizipenya, izo zidzadulira mkati, ndendende. Mulungu amapangitsidwa wangwiro mu utatu. Mukuona?

⁸⁰ Zindikirani, “dziko lakale,” chigumula; a “dziko lapansi” limene liripo tsopano; ndi Ilo limene lirinkudza.

⁸¹ Tsopano, gawo loyamba limene Iye akutifikitsako ife . . . Mwaona, dongosolo Lake la chiwombolo liri ndendende chimodzimidzi ndi chirichonse. Iye akugwiritsa ntchito njira yomweyo. Iye samasintha. Iye ananena, mu Malaki 3, “Ine ndi Mulungu, ndipo sindisinthayi.” Momwe Iye amachitira izo, chotero, ngati Iye anamupulumutsa munthu woyamba amene Iye anayamba wamupulumutsapo, ndi Magazi okhetsedwa a Mmodzi wosalakwayo, Iye ayenera kudzamupulumutsa wotsatirayo; ndipo aliyense amene Iye angamupulumutse adzayenera kukhala mwanjira yomweyo.

⁸² Ngati Iye anamuchiritsa munthu pa nthawi iliyonse kudutsa mu ulendo wa moyo; kaya ndi mmasiku a Yesu, atumwi, aneneri, nthawi iliyonse imene izo zinali; pamene zofunikira zomwezo zakwaniritsidwa, Iye akuyenera kuti achite izo kachiwiri. Uko nkulondola. Iye samasintha. Munthu amasintha, nthawi imasintha, m’badwo umasintha, nyengo zimasintha, koma Mulungu amakhalabe yemweyo. Iye ndi wangwiro. Ndi chiyembekezo chotani chimene icho chikuyenera kuwapatsa anthu odwala!

⁸³ Ngati Iye anayamba wachiritsapo munthu, Iye akuyenera kuti achite izo kachiwiri pamene zofunikira zomwezo zakwaniritsidwa. Iye anayamba, wapulumutsapo munthu, Iye akuyenera kuchita izo pa maziko omwewo amene Iye anazichita izo nthawi yoyambirira. Ngati Iye anayamba wamudzazapo munthu ndi Mzimu Woyera, Iye akuyenera kuti achite izo pa maziko omwewo amene Iye anachita nthawi yoyambirira. Ngati Iye anayamba wamuukitsapo munthu kuchokera mmanda, Iye akuyenera kuti adzachite izo kachiwiri, ndipo nthawi ina iliyonse, pa mfundo yomweyo.

⁸⁴ Iye samasintha. Oh, ndi chiyembekezo chotani chimene izo zimandipatsa ine! Ndi chiyani chimenecho? Osati mu lingaliro lina lopangidwa ndi anthu, chinachake chimene magulu a anthu abwera pamodzi; koma Mawu Ake osasinthika.

Inu mukuti, “Kodi ndi Choonadi?”

⁸⁵ Iye anati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona.” “Pakuti miyamba ndi dziko lapansi

zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera konse.” “Malemba onse amaperekedwa mwa kudzoza, chotero iwo ndi abwino ndi opindulitsa kwa chiphunzitso.” Ndipo mukumbukire, kuti, “Malemba onse adzakwaniritsidwa,” chidutswa chirichonse cha iwo.

⁸⁶ Zindikirani momwe Mulungu amazipanga izo kukhala zomveka kwa ife. Ndipo ngati izo sizinali a—chitsimikiziro chachikulu, chabwino . . . dalitso lalikulu, lachikondi lochokera kwa Mulungu! Pamene ndiwona ichi, ndimawona icho kuyambira ndiri mwana, nthawi yoyamba imene Khristu anachitapo ndi ine, ndakhala nthawizonse ndikuphunzitsa magawo atatu a chisomo amenewo. Zindikirani ngati izo siziri zoonza tsopano.

⁸⁷ Tsopano, gawo loyamba ndi “kulapa kwa Mulungu.” Ndipo kenako chotsatira pambuyo pake, ndi ubatizo wa mmadzi, “ubatizo wa mmadzi,” “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.” Mwaona, ubatizo wa mmadzi umatsatira, kusonyeza kuti kulapa kunali kwenikweni. Kapena, kuti “kuchotsa” machimo athu akale, izo ziribe kanthu kochita ndi tchimo lamtsogolo. Iwo umangochotsa. “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.” Zachiyani? “Kuchotsa.” Kuchotsa tchimo lakale kulibe chochita ndi lam’tsogolo. Basi, tchimo lanu ladulidwapo, zimene inu munachita.

⁸⁸ Inu simungalape pa zimene Adamu anachita. Inu simunachite zimenezo; Adamu anachita. Inu mumangopeza chikhululukiro pa chimene inu munachita. Chikhalidwe chakale chidakali pamenepo.

⁸⁹ Ndiroleni ine nditenge bolodi ili miniti yokha. [M’bale Branham akujambula zithunzi pa bolodi—Mkonzi]. Tsopano, *apa* pali mtima wa munthu. Tsopano, ine sindine . . . Ndiri kutali kwambiri kuti ndingakhale wojambula. *Apa* pali mtima wa munthu; ndipo *apa* pali mtima wa munthu. Tsopano, uyu cha *apa* ali ndi njoka mmenemo, limenelo ndi tchimo, apa iye ali ndi moyo wake. Uyu cha *apa* ali ndi nkunda mmenemo, umene uli Mzimu Woyera, apa iye ali ndi Moyo. Chabwino, uyu *apa*, iye ali ndi njiru, udani, kaduka; icho ndi chimene chikuyambitsa izo, ndi munthu uyu *apa*. Chabwino, uyu cha *apa* ali ndi chikondi, ndi chisangalalo, ndi kupirira; ndipo Icho ndi chimene chimachita izo, pansu *apa*.

⁹⁰ Tsopano, pamene inu mufunsidwa, kapena mwakhululukidwa machimo anu, inu mumangochita izi, mumachotsa izo. Koma chinthu chimene chinakupangitsani inu kuti muzichita zimenezo chikadali pomwepo. Ndiwo muzu wakale wa zoipa; iwo ukadali pomwepo. Zindikirani, ndiye inu mumalapa ndipo mumabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Iye akukhululukireni inu machimo anu. Zindikirani.

91 Kenako, chachiwiri, pamadzabwera kuyeretsedwa, kumene kumakhazikitsa malingaliro athu mu dongosolo la chiyero, kuti tiziganiza molondola. Kuchotsedwapo . . . kuyeretsedwa ndi liwu lapawiri la Chigriki, limene limatanthauza “kuyeretsedwa, ndi kuyikidwa pambali ku kutumikira.”

92 Kenako, chotsatira, umadzabwera ubatizo wa Moto ndi Mzimu Woyera, kuti Mulungu adzakhoze kukhala mwa ife. Ndipo Moto wa Mulungu umatsuka mitima yathu ku tchimo, ndi kudzaikamo Mzimu Woyera mmenemo. Ndiye ife timabala Moyo womwewo umene *Ichi* chinkachita, chifukwa Icho chiri mwa ife.

93 Zindikirani, mu kubadwa kwachibadwa, pamene mkazi abala mwana. Moyo wachibadwa umaimira moyo wauzimu. Pamene mkazi abala mwana, mwachibadwa, chinthu choyambirira chimene chimachitika ndikutuluka kwa madzi, kenako magazi, ndipo kenako mzimu (moyo). Kumugwira mwana wamng'onoyo ndi kumumenyaiye khosi, ndipo amayamba kulira, akukuwa. [M'bale Branham anawomba manja ake—Mkonzi]. Madzi, magazi, mzimu.

94 Ndipo tsopano pamene mwana wabadwa mu Ufumu wa Mulungu, iye amabwera mwanjira yomweyo: madzi, Magazi, Mzimu.

95 Tsopano zindikirani, kuyeretsedwa, gawo lachitatu . . . gawo lachiwiri la zimenezo, limatsuka malingaliro; limakhazikitsa mtima, malingaliro a mtima, mu dongosolo la chiyero.

96 Munthu akhoza kulapa machimo ndipo iye nkumaganizabe za . . . Chabwino, mwinamwake iye ndi—mwamuna wa makhalidwe oyipa, mkazi aliyense wowoneka mwa makhalidwe oyipa amene iye amamupeza, akadali pamenepo. Mwinamwake iye ndi chidhakhwa; nthawi iliyonse akanunkhiza chakumwacho, chimakhalabe pomwepo. Mukuona?

97 Komano pamene iye ayeretsedwa, izo zimatsuka chikhumbo chimenecho kuchoka mwa iye. Mukuona? Izo zimachotsa kufuna kwa izo. Iye akhoza kumayesedwabe, koma Iye amachotsa kufuna kwa izo. Komabe, iye sali bwinobe.

98 Kenako, iye amabatizidwa ndi Mzimu Woyera ndi Moto. Kutsukidwa, kuwotchedwa, kutsukidwa; ndipo kenako amaikidwa mu utumiki wa Mulungu.

Kuyeretsedwa kumangowayika iwo pambali *ku* utumiki.

99 Ndipo zindikirani chimodzimidzi basi momwe izo zinabwerera, mauthenga akubwera. Martin Luther, kulungamitsidwa; John Wesley, kuyeretsedwa; chipentekoste, ubatizo wa Mzimu Woyera. Mauthenga, ndi pamene sipangakhalenso mibadwo ya izo, mwaona. Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Magawo atatu. Ubatizo umayeretsa mtima ndi Mzimu Woyera.

¹⁰⁰ Ndi zokhudza bwanji tsopano, Iye akutenga malo amene ife titi tidzakhaleko, akuwadutsitsa mu dongosolo lomwelo.

¹⁰¹ Tsopano, Iye anawuyitana Mpingo kudutsa mu kulungamitsidwa, anawuyitana Iwo kudutsa mu kuyeretsedwa, kenako anawudzaza Iwo ndi Mzimu Woyera ndi Moto. Ndipo Iye anawutenga Iwo kudutsa mu dongosolo, kuti Iye Mwiniwake, Mzimu Woyera Mwiniwake, Mwana wa Mulungu, adzakhoze kukhala mu mtima wa munthu. Tsopano, Iwo ukuyenera kudutsa mu zimenezo Iye asanabwere mwa Iwo.

¹⁰² Zindikirani, Iye anachita kwa dziko, kumene Mkwatibwi ameneyo ati adzakhaleko, mwanjira yomweyo, dongosolo Lake lomwe lomwelo—la chipulumutso.

¹⁰³ Zindikirani dziko la chigumula. Iye, ilo litatha kulapa, kudzera mwa Mkwatibwi wa tsiku limenelo, Nowa, Iye analipatsa ilo ubatizo wa mmadzi, analiphimba ilo ndi madzi. Kenako, kulungamitsidwa, kuwonetsera kuti Iye ali pa njira Yake kuti adzayitane dziko lakugwa ili, kuchokera ku Edeni, kubwerera ku kubwezeretsedwa kwake kachiwiri.

¹⁰⁴ Kenako Khristu anabwera ndipo anadzakhetsa Magazi Ake pa ilo, kuliyeretsa ilo ndi kulitenga ilo. Mwaona, limenelo ndi dziko limene ife tikukhalamo tsopano.

¹⁰⁵ Mukuona momwe Satana, apa mu Lemba, anayesera kuti amupangitse Iye kuswa dongosolo la Mulungu kuti alandire ilo, kulipereka ilo kwa Iye pamene iye anamutengera Iye pamwamba pa phiri, ndipo nkukayesera kuti alipereke ilo kwa Iye popanda kugula kwa Magazi?

¹⁰⁶ Kodi inu munazindikira momwe Abrahamu, pamene iwo ankayesera kumupatsa iye dzikolo, iye analigula ilo ndi mashekeli a siliva ambiri, pamaso pa anthu, ngati chizindikiro, ngati umboni? “Zidziwike lero kuti ine ndagula malo a manda awa.” Mwaona, anagula iwo! Ndipo Satana anayesera ku—kuti amupatse Iye ufumu umene uli wake tsopano. Iye anayesetsa kuti awupereke iwo kwa Iye ngati mphatso, koma Iye sanalandire iwo. Chifukwa iwo, mwaona, kenako Satana akanakhoza kukhala ndi chodzinenera pa iwo. Koma, iwo un kayenera kugulidwa. Amen. Iye anali Mawu mu chidzalo chake. Iwo sakanakhoza kumunyenga Iye mu icho.

Kenako, tsopano ndi kuti adzatenge ubatizo wa Moto.

¹⁰⁷ Mwaona, izo zatero tsopano. . . Chinachitika ndi chiyani? Khristu anabwera ndipo anawuitanira Mpingo ku kulapa, ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, kwa chikhululukiro; kuwuyeretsa Mpingo; ndipo ndi Moto wa Mulungu unatsika ndipo unadzawotcha zonyansa zonse, ndi unabwera ndi kudzakhala mu mtima wa munthu.

¹⁰⁸ Tsopano, dziko, kuti lidzawomboledwere munthu wowomboledwa uyu, Iye akugwiritsa ntchito njira Yake

yomweyo. Iye analibatiza ilo mmadzi, chiwonongeko cha chigumula chitachitika. Anakhetsa Magazi Ake pa ilo, kuti aliyeretse ilo ndi kulitenga ilo. Ilo ndi Lake.

Satana anayesetsa kunena kuti, “Ine ndidzalipereka ilo kwa Iwe.”

¹⁰⁹ Iye anati, “Ayi, bwana, Ine ndidzaligula ilo.” Mulole iwo ukhale umboni. Iye anakwezedwa mmwamba, ngati chizindikiro, kuti Iye waligula ilo. Iye anagula ilo.

¹¹⁰ Koma tsopano ilo likuyenera kudutsa mu ubatizo wa Moto, Moto woyera wochokera kwa Mulungu, umene umayeretsa dziko lapansi ndi miyamba yozungulira ilo. Ndiye, ilo lagulidwa kuti owomboledwa adzakhoze kukhala mwa ilo, kudzakhala mwa ilo mwa mtendere. Zindikirani, ubatizo wa Moto ndi woti udzaliyeretse ilo ku tchimo, kuchokera ku matenda, ku majeremusi a matenda, kuchokera kwa ochimwa, kuchokera kwa mdierekezi ndi gulu lake lonse. Iye ndi woti adzaponyedwere kunja, mu Nyanja ya Moto. Moto Woyera wochokera kwa Mulungu, umatsika pansi kuchokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba, ndi kudzaliwotcha ilo, zindikirani, kudzalikonzekeretsa ilo kuti Mulungu adzakhalemo. Pakuti, Mulungu, mu Dziko Latsopano limene liri nkudza, adzakhala pa dziko lapansi. Chifukwa, inu mukuti, “Mulungu, Iye amakhala mu mtima wa munthu.” Koma, Iye ndi Mkwatibwi akudzakhala Mmodzi, ndipo iwo adzapita Kwawo mu Dziko Latsopano. Ndipo dongosolo lomwelo la chiwombolo likugwiritsidwa ntchito kuwombola, ziwiri zonsezo, dziko lapansi ndi anthu amene akudzakhala mmenemo.

¹¹¹ Mwaona, mtima ukuyenera kutsukidwa monga choncho. Mulungu asanabwere pansi mu umunthu wa Mzimu Woyera, amene ali Khristu akubwera pansi ndi kudzakhala mu mtima wa munthu, choyamba iwo ukuyenera kulapa. Iwo ukuyenera kubatizidwa mmadzi, mu Dzina Lake, kuti uwonetse uti iwo ndi wandani.

Kenako iwo ukuyenera kutsukidwa ndi Magazi a Yesu.

¹¹² Ndipo kenako Moto woyera ndi Mzimu Woyera, wochokera kwa Mulungu, umabwera pansi ndi kudzawotcha chikhumbo chonse cha tchimo, chikhalidwe chonse cha mdziko. “Ndipo, chotero, iye amene achimwa mwadala atatha kulandira chidziwitso cha Choonadi. . .” Kenako, kenanso Baibulo linati, “ndi zosatheka. . .” “Kuti, a—munthu wobadwa mwa Mulungu sangakhoze kuchimwa; iye samachimwa.” Palibe njira yoti iye achimwe. Iye angakhale bwanji wochimwa, ndipo wowomboledwa, pa nthawi yomweyo? Kodi ine ndingakhale bwanji mu sitolo ya pinyolo, ndi kunja kwa sitolo ya pinyolo, pa nthawi yomweyo? Mukuona? Oh, Iye anatiwombola ife ndi Magazi Ake; ndi Mzimu Wake iye anatiyeretsa ife; ndipo kenako

nkubwera kudzakhala mwa ife, Mpingo. Osati chipembedzo, tsopano; Mpingo!

113 Zindikirani mwacheru tsopano pamene ife tikutenga izi, malo amene ife titi—tizidzakhalamo. Tsopano, tsopano, a—kulapa kwa chigumula, ndiye, kunabweretsa ubatizo wa mmadzi. Kenako Khristu anabwera ndipo anadzakhetsa Magazi Ake pa ilo, kuti adzayeretse ndi kudzalitenga ilo. Ndipo atatero nkubwera, chotsatira, chiwonongeko cha dziko monga chiriri tsopano.

114 Tchimo lonse limene liri mmiyamba, “iye ndi kalonga wa mphanvu ya mu mlengalenga,” iye amatsekereza (nkhondo) madalitso a Mulungu. Mmenemo mumabwera mphezi za kung’anima ndi kugunda dziko lapansi, ndi chirichonse, kuchokera mmiyamba, mikwamba ya mvula yocheka, ndi mphepo yamkuntho, mku-...mikuntho ndi chirichonse, “zimachokera kumwamba,” amene ali Satana, “kalonga wa mphanvu ya mu mlengalenga.”

115 Zindikirani, onani momwe Satana anayesera kuti alitenge ilo, monga ine ndinanenera maminiti pang’ono apitawo, polipereka ilo kwa Yesu popanda kuligula ilo. Potero, Satana akadali ndi chodzinenera, chifukwa akumayang’anapo, mwaona. Koma Yesu akuligula ilo ndi Magazi Ake okhetsedwa ndipo akulibweretsanso ilo kwa mwiniwake woyenera. Mukuona? Umo ndi momwe Iye anatigulira ife, ndi Magazi Ake, momwe Iye anawugulira Mpingo.

116 Ndipo tsopano ndi ubatizo wa Moto ukuliyeretisa ilo ku majeremusi onse, matenda ake onse, matenda onse, ngakhale zinthu zonse zauzimu; zimene ziri pafupi nafe, nazonso, zikuchita mwanjira yomweyo; kulikonzekeretsa ilo kuti Mulungu adzakhalemo, mu m’badwo waukulu uwu umene uli nkudza, Dziko Latsopano. Mwaona, Iye akuliwombola ilo mwanjira yomweyo imene Iye akuchitira ndi anthu Ake. Iye akuzipanga izo zonse mofanana basi, dongosolo Lake la chiwombolo. Pakuti, Iye ndi Mulungu wosasintha, nthawizonse yemweyo mu madongosolo Ake.

117 Momwe ine ndinakuuzirani inu, kale, ndi kuzidziwitsa izo kwa inu, ndi mwa mibadwo yonse, kuti Mulungu sangathe kusintha; amazidziwitsa izo, mwanjira iliyonse, mofanana.

118 Iye anazidziwitsa izo, uthenga Wake woyamba, mu dziko la chigumula, ndi Nowa mneneri.

119 Ine ndimayankhula ndi m’bale wokonedwa amene wakhala limodzi ndi ine pano. Dzulo, iye anati, “Chinthu chimodzi chimene inu munanena, M’bale Branham, chimene nthawizonse chimandigwedeza ine.”

Ine ndinati, “Ndi chiyani icho, m’bale?”

¹²⁰ Ndipo iye anati, “Ichi ndi chimene inu munanena,” ndipo ndi zoonza, “Apang’ono, momwe kagulu kakang’ono kadzapulumutsidwe mmasiku a Kudza.’ Ndipo ife tinakambirana za momwe Yesu ananenera, ‘Khwalala ndiro chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono pamene adzakhala amene ati adzaizeze iyo.’ Tsopano zindikirani, Baibulo linati, ‘Monga izo zinali m’masiku a Nowa mmene miyoyo eyiti inapulumutsidwa ndi madzi, chomwechonso izo zidzakhala pa Kudza.’”

Ine ndinati, “M’bale, inu mwangopeza . . .”

Iye anati, “Kumbukirani, kunali miyoyo eyiti yokha kumeneko.”

Ine ndinati, “Inu mwangopeza theka la chithunzicho.”

¹²¹ Komabe, Nowa anali choyimira cha otsalira amene adzatengedwere kwinako, osati gulu lodzasanthulidwa. Enoki, mwamuna mmodzi, anapita mu Mkwatulo chigumula chisanadze, kuwonetsera kuti Mpingo sukupita mu chisautso kapena chirichonse chozungulira izo. Enoki anasanthulidwa, mwamuna mmodzi. Oh, mpingo ukhoza kukhala angapo; koma Mkwatibwi adzakhala gulu laling’ono kwambiri limene liti lidzapange Mkwatibwi. Tsopano, mpingo ukhoza kukhala chiwerengero chachikulu; koma, Mkwatibwi, inu mukuona, mufanizire eyiti ndi wani. Ka eyiti kuchepera kwake, adzakhala Mkwatibwi, kuposa mpingo.

¹²² “Ndipo ngati olungama adzapulumutsidwe moperewera, ochimwa ndi osapembenda adzawonekera pati,” iwo amene amadziwa bwinoko, kuti achite izo, ndipo nkumapitirira ndi kumakachita izo mulimonse? Iwo amene amatsatira malamulo a chipembedzo mmalo mwa Mawu, kodi iwo adzawonekera pati, komabe otchedwa Akhristu, kumatenga Dzina la Khristu?

¹²³ Tsopano, mwangwi, Nowa anali choyimira cha iwo amene anatengedwera kumeneko. Kumbukirani, pamene Nowa anatuluka, Hamu anali ndi iye. Tchimo linali likadali mmenemo. Tchimo linapitirirabe, kudutsa mu chombo. Kusakhulupirira, kukayikira, kunakalowa mu chombo, kunyamulidwa pamwamba pa chiweruzo. Koma Enoki anapita pamwamba kuposa chombo, iye anapita mpaka mu Kukhalapo kwa Mulungu. Koma Nowa anadutsa ndipo anatuluka, ndipo tchimo linali liripobe; choyimira cha Zakachikwi, cha chikhalidwe cha dziko.

¹²⁴ Zakachikwi si mathero ake. Padzakhalabe nthawi Zakachikwi zikadzatha. Zakachikwi ndi danga la nthawi; koma, osati Dziko Latsopano. Ayi, ndithudi. Zindikirani, mmenemo, ife tifika kwa izo pakapita kanthawi.

¹²⁵ Mwaona, dziko lapansi, lowomboledwa, likubwerera kwa Mwiniwake wapachiyambi kachiwiri. Ilo linatenga . . . Iye analitenga ilo kuchokera kwa Satana. Iye anakoka, kulichotsa

dziko lapansi kwa Satana, monga momwe Iye anakuchotserani inu kwa Satana, monga Iye anamutengera mkazi wamng'ono pa chitsime kumuchotsa kwa Satana. Apo panayima wansembe, ankaganiza kuti iye anali ndi Mulungu, ndipo iye analibe kalikonse. Mukuona?

¹²⁶ Ndikufuna kuti ndikujambulireni inu izo mphindi chabe. Tsopano, tikufuna kuti tizimvetse izi momveka bwino, chotero tsopano penyani mwatcheru tsopano pa kuphunzitsa uku. [M^bale Branham akujambula zifotokozerera pa bolodi mu ndime zingapo zotsatirazi—Mkonzi].

¹²⁷ Tsopano, *ichi* apa, apa ndi Mulungu. Mulungu, yemwe ali Wamuyaya, wopanda. . . Palibe wina koma Iye. Koma, mwa Mulungu, Iye anali ndi zikhumbo. Tsopano, *ichi* apa chikuimira Mawu, Mawu a Mulungu, amene anadzasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu mu umunthu wa Yesu.

¹²⁸ Tsopano *ichi* apa, munthu apa, ife timupanga iye monga *chonchi*. Tsopano, *uyu* akutchedwa mkazi pa chitsime. *Uyu* ndi wansembe, Mfarisi. Ndipo pamene inu mukuwona *ichi*, bolodi lopanda kanthu, zikutanthauza chisomo ndi chipulumutso.

¹²⁹ Tsopano, “Pachiyambi panali Mawu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Magawo atatu. Icho chinali chikhumbo poyamba, chinali mwa Mulungu, kuti Iye anaganiza za Iyemwini ngati munthu; ndipo izo zinamupititsa Iye pansi kuti akakhale Yesu; ndipo tsopano, ngati inu mudzakakhale konse Kumeneko, inu munali ndi Iye nthawi imeneyo. Pakuti, ulipo mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndiwo Mulungu; ndipo iwe umayenera kukhala gawo la Mulungu pachiyambi, osati chimene wangosankha kuno. Iye anakusankhani inu. “Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera.”

¹³⁰ Tsopano tamuwonani wansembe uyu apa. Ife tikupeza gawo lake la pansi, *apa*, moyo wake wakumbuyo, kumbuyo kwake, kukonzedweratu kwake kumbuyo kuno, ndi wochimwa.

Apa pali gehena, pansi *apa*.

¹³¹ Tsopano, gawo laling'ono ili mkati *umu*, limene likuwoneka ngati bolodi, limenelo likuyimira chiyero chake. Iye anali wansembe. Iye anali munthu wolemekezeka. Icho chinkaimira *ichi*. Iye anali, nayenso, amayenera kukhala munthu wabwino, kapena iye sakanakhala wansembe. Koma inu mukuona momwe iye anawupezera iwo, zinali kuphunzira mwaluntha.

¹³² Tsopano, mkazi wamng'ono uyu, moyo wake woyamba, pamwamba *apa*, iye anali wachiwerewere, iye anali yense atayipitsidwa. Koma pansi pomwe mwa iye, *apa*, munali kumvetsa pang'ono pokha. “Ine ndikudziwa pamene Mesiya adzabwera. . .” Mukuona? Mwaona, izo zinali pamenepe.

133 Zindikirani, pamene Yesu anabwera ndipo nkudzawawonetsera Mawu, chifukwa Mawu anazindikira malingaliro amene anali mu mtima; monga Ahebri 4 amati Iwo adzatero, 4:12, kuti Iye akanadzatero. “Mawu anali ozindikira za malingaliro a mtima,” ndipo Iye anabwera monga Mwana wa munthu, Mneneri. Chinachitika ndi chiyani? Wansembe uyu, ndi kuphunzira chabe kwanzero, anati, “Ndi mdierekezi,” chifukwa ndicho chimene chipembedzo chake chinkachitcha icho. Kodi icho chinachita chiyani? Iye analibe chomuyimira, koteri icho chinamudetsa iye.

134 Koma mkazi wamng’ono uyu analibe chirichonse choti awonetse; iye anali waumve ndi wodetsedwa momwe iye akanakhalira. Koma, zindikirani, pansi pomwe mwa iye, iye ali ndi chomuimirira, mwaona. Ndipo, ndiye, iye ankayembekezera kuti ichi chidzapangidwe thupi.

Ndipo pamene Iye anati, “Pita ukamtenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno.”

Iye anati, “Bwana, ine ndiribe.”

135 Anati, “Iwe wanena zoon, chifukwa uli nawo asanu, ndipo amene iwe uli naye tsopano si wako. Iwe wakhalapo nawo faivi. Izo zikupanga sikisi amene unali nawo.”

136 Iye anati, “Bwana!” (Osati, “Ndinu,” osati, “Belezebule.”) “Ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Tsopano, ife tikudziwa Mesiya, wotchedwa Khristu, adzabwera. Ndipo pamene Iye adzatero, Iye adzachita izi.”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

137 Panalibenso kukaikira. Inu simunayenera kufotokoza izo. Iye anaziwona izo. Iye anakhulupirira izo. Iye anapita! Bwanji? Kodi Iwo anachita chiyani kwa iye? Iwo anamuwombola iye.

138 Tsopano penyani, Iye anabwera kuti adzakhale Muwomboli. Nkulondola uko? Kodi *kuwombola* kumatanthauza chiyani? “Kubwezeretsa.” Nchifukwa chiyani Iye sanamutenge wansembe? Iye kunalibeko nkomwe kumwambako. Mukuona? Mwaona, iye analibe chomuimirira.

139 Iye anabwera kuti adzawombole chimene chinali chitagwa. Mu kugwa, *ichi* chinasokonezeka, ndi mtsikana ameneyo; koma Mulungu anali ndi iye mu kuganiza Kwake maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndipo Iye anabwera kuti adzamuyeretse iye. Mukuona? Kenako Iye. . . Iye anali ndi Moyo Wamuyaya. Mukuona?

140 Kutu, wansembe, kodi izo zinachita chiyani kwa iye? Izo zinamutumiza iye kubwerera kumene iye ankapita. Iye analibe kalikonse, poyamba, kuphunzira kwaluntha kokha.

141 Tsopano mveterani, mzanga, ngati chinthu chokha chimene inu muli nacho ndi kungophunzira mwaluntha, inu muli ndi chinachake chosiyana ndi icho. Ndipo inu simudzakhoza konse

kuchipeza Icho pokhapokha mukanakhala ndi chokuimirirani. Ndi chifukwa chake ine ndikukhulupirira inu mukumabwera kuchokera kummawa ndi kumadzulo, kumpoto ndi kummwera; Mawu, amoyo, akuwonetseredwa mthupi.

¹⁴² Zindikirani tsopano momwe Iye akupangitsira njira Yake kudziwika pogwiritsa ntchito aneneri Ake, pachiyambi. Iye sanayambe wasinthapo konse zimenezo.

¹⁴³ [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]... chipulumutso. Iye anamulungamitsa munthu; anamuyeretsa iye; anatumiza Mzimu Woyera ndi Moto, ndipo anawotcha tchimo mwa iye, ndipo anakhala mwa iye, Iyemwini.

¹⁴⁴ Iye akuchita nalo dziko lapansi, limene Iye ati adzaligwiritse ntchito mu dongosolo la chiwombolo, mwanjira yomweyo. Ilo linalapa ndipo linabatizidwa m'madzi, mu... ndi Nowa. Yesu anabwera ndipo anadzaliyeretsa ilo, pokhetsera Magazi Ake pa ilo, ndipo analitenga ilo. Ndipo mu Dziko Latsopano limene liri nkudza, ilo lidzakhala ndi ubatizo wa Moto woyera, kuti adzalitsuke ilo ku mdierekezi aliyense, jeremusi iliyonse, matenda aliwonse, chirichonse chimene chiripo, ndi kudzalipanga ilo mwatsopano. "Ine ndinawona Kumwamba Kwatsopano ndi Dziko Latsopano."

¹⁴⁵ Inu mumadzakhala munthu watsopano. Amen! Osati kokha wakale woyikidwa zigamba, pojowina mpingo kapena kuyesera kutsegula tsamba latsopano, koma ndinu gawo lathunthu latsopano. Mulungu amamutenga munthu wokalambayo ndi kumuwotha iye kwathunthu, ndi Mzimu Woyera ndi Moto, ndipo amabwera Iyemwini, amadzatumiza chokuimirirani chanu. "Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine." Inu mukuona izo? Dongosolo lomwelo; njira yomweyo.

¹⁴⁶ Satana anali... adzachotsedwa pa dziko lapansi, chimodzimidzi basi momwe Satana anachotsedwa kwa inu. Satana sangavutitse; kapena, iye akhoza kumuyesa, koma iye sangathe kumutenga Mkristu wobadwa mwatsopano. Pakuti, Mulungu, kuchokera ku maziko a dziko lapansi, anamuwoneratu iye, ndipo anatumiza Yesu kuti adzamuwombole iye, ndipo Magazi amamuyankhulira iye. Kodi iye angachimwe bwanji pamene izo sizingawonedwe, ngakhale, ndi Mulungu? Iye alibe ngakhale... Chinthu chokhacho chimene Iye amamva ndi liwu lanu. Iye amawona chokuimirirani chanu. Amen! Izo nzoona. Mukuona?

¹⁴⁷ Mwanjira yomweyo, pakuti dziko ndi chimodzi mwa zikhumbo Zake basi chimodzimidzi momwe inu muliri m'modzi mwa zikhumbo Zake. Dziko limakhala chimodzi cha zikhumbo Zake, chifukwa kunali kuganiza kwa Mulungu, pachiyambi. Kuti adzakhale ndi dziko, kuti adzakhale pa Mpandowachifumu,

kuti adzakhale Mfumu, kuti adzakhale Wowombola, kuti adzakhale Mchiritsi, ndizo zikhumbo Zake.

¹⁴⁸ Chimodzimodzi monga chikhumbo cha inu. Ine sindingati a—a “nsanamira” pokhapokha ngati ndikuganiza za nsanamira. Ine sindingati “munthu” pokhapokha ngati ndikuganiza za munthu. Ndipo pamene ine ndiganiza za munthu, ndiye ndimati “munthu,” kuganizako ndiko chikhumbo changa ndipo kufotokozerako ndi mawu. Mukuona?

¹⁴⁹ Monga Yesaya, iye akanatha bwanji kunena, kuti, “Namwali anali woti adzayima”? Kodi lingaliro ndi chiyani?

¹⁵⁰ Tsopano, ambiri a inu mukudabwa momwe izo, kuzindikira zamumtima kuja, kumabwerera. Ine ndikuuzani inu. Mwaona, ndi mawu amene ine ndimanena. Ndipo si maganizo anga, chifukwa ine sindikudziwa. Sindikudziwa kuganiza kwake. Kodi ndingakuuzeni inu bwanji kuti ndinu ndani komanso kumene mukuchokera, pamene ine sindimakudziwani inu? Kodi ine ndingakuuzeni inu bwanji chimene munachita zaka teni zapitazo, pamene ine sindinakuwonenipo inu mmoyo wanga? Kodi ndingakuuzeni inu bwanji komwe mudzachite ndi chimene mudzachite zaka teni kuchokera pano? Kodi ine ndimadziwa bwanji zamtsogolo? Koma ndi lingaliro la Winawake.

¹⁵¹ “Mulole malingaliro amene anali mwa Khristu akhale mwa inu. Mulole malingaliro amene anali mwa Khristu akhale mwa inu.” Mwaona, ndiye si kulingalira kwanu. Ndi kulingalira Kwake, kupyolera mwa inu. Ndipo simukufotokoza mawu anuanu; inu mukufotokoza Mawu Ake.

¹⁵² Umo ndi momwe abale amasokonezeka nthawi zambiri, pa kutanthauzira kwa malirime, ndi zinthu. Mwaona, iwo amanena zinthu zimene siziri zolondola, iwo samazindikira kuti ameneyo ndi Satana. Inu mukuti, “M’munda wa Mulungu?” Mungodikira mpaka ife titamaliza, tipeze ngati izo siziri, kapena ayi. Udzu ndi tirigu zimamera m’munda womwewo. Zonse ziwiri zimakhala ndi dzuwa lomwelo ndi mvula yomweyo. Mukuona?

¹⁵³ “Koma ngati patakhalala mmodzi pakati panu amene ali mneneri, Ine Ambuye ndidzayankhula kwa iye. Ndipo ngati chimene iye anena chichitika, ndiye ameneyo ndi Ine, mwaona, chifukwa iye sakuwonetsera zake zomwe. Iye akuwonetsera malingaliro Anga, zikhumbo Zanga za zinthu zimene zikuyenera kubwera, ndipo Ine ndidzagwiritsa ntchito pakamwa pake kuwonetsera izo. Ndipo atatha kunena zimenezo, izo zikuyenera kukwaniritsidwa. Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzalephera konse.”

¹⁵⁴ Yesaya anati, “Namwali adzayima.” Izo zikukhazikitsa izo. Iye adzayima. Chimene Mulungu ananena, Iye amachichita.

¹⁵⁵ Oh, kudziwitsa, mwa aneneri Ake, mawonetseredwe Ake onse, chifukwa ndi zikhumbo Zake za malingaliro Ake zikufotokozedwa.

156 Tsopano, apa izo zinali, mwa mkazi wamng'ono *uyu*. Iye anali chimodzi cha zikhumbo Zake. Mukuona?

157 Ndipo apo panali wansembe, akuyimira Kuwala. Iye anali ataphunzira izo kuchokera mu Baibulo. Iye anali ataphunzira kuti Mulungu anali Mulungu. Iye anali ataphunzira kuti chihero chinali cholondola. Iye anaphunzira kuti panali lamulo la Mulungu. Iye anali ataphunzira izo chifukwa cha lingaliro laluntha. Ndipo iye anabadwa mu mzere wolondola; iye anali Mlevi. Koma iye ankangodziwa izo mwa lingaliro laluntha. Ndipo pamene Kuwala kwa ora . . . Mwaona, iye anaphunzira izo ndi chimene *chinali* chitachitika, osati chimene chinkachitika; chimene chinali chitachitika! Ndipo pamene iye anapeza chimene chinkachitika, chipembedzo chake sichinanene kanthu za Ichu, chotero iye analibe choyimira cha Ichu.

158 Koma apa panali Muomboli pa dziko lapansi pa nthawi imeneyo, kuti awombole zikhumbo izo za Mulungu, ndipo iye anazilandira izo. Iye sanafunse nkomwe zimenezo. Iye anati, “Pamene Mesiya adzadza, Iye adzachita izi,” ndipo izo zinakhazikitsa izo. Ndipo iye anaziwona izo zikuchitidwa, chotero . . . Iye anati, “Ine ndine Mesiya,” kotero izo zinakhazikitsa izo. Panalibenso funso. Iye anangopita, kumakamuuza wina aliyense, “Bwerani, mudzawone Amene ine ndamupeza.”

159 Zochitika zimenezi zimatiyeretsa ife, kachisi wa malo Ake okhalamo: kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Moto. Izo zimachita kuyeretsa kwa (wathu) kachisi uyu.

160 Chotero, monga momwe chimango cha dziko lakale sichinawonongeke, ndi madzi pamene ilo linakokoloka; chimango cha dziko lapansi, chimango chakale, ndi . . . dothi lonse, zinthu zonse zimene Mulungu anaziyika pa dziko lapansi, sizinawonongeke pamene dziko loyamba linawonongedwa. Ndipo Baibulo linati ilo “linawonongedwa,” koma icho sichinawononge chimangocho. Ichu chinangowononga tchimo ndi ochimwa amene anali mu ilo. Chimangocho chinatsalira.

161 Koma, inu mukuona, monga kulungamitsidwa, monga inu Abaptisti ndi Amethodisti mumafuna kuganiza za zimenezo, kulungamitsidwa basi, kukhulupirira ndi kubatizidwa, izo sizokwanira. Inu mudzayendayenda kubwerera mu zinthu za mdziko, ndi kudula tsitsi lanu ndi kuvala zazifupi, ndi china chirichonse. Mwaona, palibe chimene chachitika panobe. Inu munangoyang'ana mmbuyo ndi kuwona kuti munachita cholakwika.

162 Kodi kulungamitsidwa kunachita chiyani kwa dziko? Sikunachite kanthu kwa ilo; zinayambiranso kachiwiri, tchimo lochuluka basi monga momwe limakhalira nthawizonse. Umo

ndi momwe munthu amachitira, ndipo ndi momwe amapitira patsogolo.

¹⁶³ Umo ndi momwe mvangeri wamkulu, Billy Graham, akuyenera kuwonera. Iye anati, “Ine ndimapita ndi kukakhala ndi owatembenuza sarte sauzande, ndikabwerera mu chaka ndipo sindimakapezako sarte.” Ndi patali ponse pomwe iwo anapitapo. Mukuona? Ndipo, ndithudi, iwo amalapa. Ine ndikukhulupirira kuti iwo amalapa; ambiri a iwo, kapena ena a iwo, pafupifupi. Koma izo sizomwe zimafunikira. Izo zikutsimikizira izo apa.

¹⁶⁴ Tsopano, chotero dongosolo la chimango cha dziko lakale silinawonongedwe ndi madzi. Dziko lapansi linangokokoloka. Ilo linapeza ubatizo wake. Ilo linabatizidwa.

¹⁶⁵ Momwemonso chimangocho chidzakhale, ngakhale chitawotchedwa ndi Moto. Iwo sumawononga dziko lapansi, mwawona, iwo umangowononga tchimo limene liri pa ilo.

¹⁶⁶ Zindikirani apa, ena a inu ophunzira Baibulo, ndipo makamaka Dokotala Vayle akuyang’ana pa ine. Zindikirani mu Petro, mu mutu wa 2 wa Petro apa, mutu wa 3, kani, iye akugwiritsa ntchito mawu akuti “dziko,” monga liwu la Chigriki lakuti *kosmos*, limene limatanthauza, “dongosolo la dziko.” “Dziko lapansi lidzapita, lidzasungunula zammwambazo ndi kutentha kwakukulu.” Mukuona? Izi sizimatanthauza kuti dziko lapansi, pulaneti, lidzapita. Koma dzikolo, *kosmos*, ndale, ochimwa, machitidwe, tchimo, matenda, majeremusi, chirichonse chimene chiri cholakwika, chidzapita. Chirichonse chimene nthawiyina . . .

¹⁶⁷ Mulungu nthawi ina anagwedezapo miyamba, koma nthawi iyi Iye anati Iye adzagwedeza dziko lapansi, miyamba ndi dziko lapansi. . . “Iye anagwedeza dziko lapansi,” kani, “ndiyeno nthawi ino Iye adzagwedeza miyamba.” Mukuona? “Pakuti tikulandira Ufumu umene sudzasunthidwa.” Ndi Ufumu Wamuyaya. Penyani momwe iye akupitira kwa izo.

¹⁶⁸ Zindikirani apa, Petro anati, “Ndipo lidzasungunuka ndi kutentha kwakukulu, ndipo ntchito zake zidzapserera,” osati pulaneti. “Ntchito zake mmenemo,” ntchito za munthu, andale awo onse ndi zochita zawo, ndi zipembedzo zawo zonse ndi zochita kupangidwa ndi muthu, zonse zidzapita ndi ilo pamene ilo lizidzapsya.

¹⁶⁹ “Ndipo—ndipo miyamba idzapita ndi nkokomo wawukulu.” Kodi inu munazindikira apa? “Miyamba idzapita ndi phokoso lalikulu.” Mvetserani! Dziko lonse lapansi lidzakhala pa moto, ndipo lidzayatsa mipweya imene ili pa dziko lapansi ndi kuiphulitsa iyo. Ndizo ndendende. Kuyankhula . . . Baibulo linanena apa, Petro anati, “Ndipo miyamba idzapita, ndi dziko lapansi, ndi phokoso lalikulu.” Kuphulika koteroko kudzaligwedeza ilo, oh, mai, chifukwa izo zikuyenera kupha

matenda aliwonse, nthula iliyonse, minga iliyonse. Chirichonse chimene chikuyenera kuchitidwa, Moto udzachiwotcha icho. Ndipo, kumbukirani, si pamodzi basi moto weniweni, iwo ulinso Moto woyera, mwaona, umenewo udzamuchotsa Satana ndi zake zonse, ziwanda zonse. “Ziwiri zonse kumwamba ndi dziko lapansi,” ameni, “zidzapita,” kupha majeremusi onse, tizirombo tonse, moyo wachirengedwe wonse pa ilo ndi pozungulira ilo, ngakhale H₂O (madzi) adzaphulika. Taganizani za zimenezo. Kukamba za phokoso!

¹⁷⁰ Inu mukuganiza kuti phokoso laling’ono lija kunja kuno mu Tucson linali chinachake, pamene Iye anatsegula Zisindikizo zisanu ndi chimodzi, limene linagwedeza dziko mozungulira, ndi kuyambitsa kuyankhulako. Mudikire kufikira dziko lino likamadzalandira ubatizo wake!

¹⁷¹ Inu mukudziwa, pamene munthu akulandira ubatizo wa Moto, pamakhala phokoso lambiri pamenepo. Iwo amaganiza kuti icho ndi chamanyazi, kumva anthu akukuwa ndi kufuula monga choncho. Mungodikira kufikira pamene dziko lino lizidzalandira ubatizo wake!

¹⁷² Eya, izo zidzafotozoa...zidzaphulitsa ilo, H₂O, madzi, pakuti Baibulo linanena apa mu Chivumbulutso 21, “ndipo panalibenso nyanja,” kuiphulitsa iyo. Izi zidzasintha kusalala konse kwa dziko lapansi lonse. Ilo lidzaphulika ndi kuphwasuka mu zidutswa. Kunja konse, chimng’alu, ndi kwa mapazi ma handirede pansi pake, zidzangophwanyidwa kwathunthu. Mumlengalenga, mipweya imene ili padziko lapansi tsopano, kumene iwo akupeza mabomba awa amene sangadutse pamenepo, mlengalenga mwamukulu mmenemo, mmwamba momwe mu mtundu wina wa mlengalenga kuti muli mitundu yonse ya mipweya, iwo amatero; ndipo izo zidzaphulika. Mkwiyoyera wa Mulungu udzabwera pa ilo, mwaona, ndipo udzaliyeretsa ilo, udzasintha malo onse.

¹⁷³ Tsopano, ambiri a inu amene mukufuna kuti mulembe mawu awa, mawu Achigriki, “kuchoka.” Iwo amachokera ku mawu... Ine ndinachita kuwafufuza iwo. Ine ndinaganiza, “Kodi dziko ili lidzachokapo chotani, ndipo komabe ife nkumadzakhala mwa ilo?” Koma ngati inu mungazindikire, ena a inu anthu amene mukufuna kuti muwalembe iwo, ine ndikutchulirani inu iwo. Ine ndimalephera kuti ndiwatchule iwo, p-a-r-e-r-e-c-h-o-m-i-a. Sindikudziwa momwe ndingawatchulire iwo.

¹⁷⁴ Tsopano, mwanjira imeneyo, monga ine ndinanenera, pamene ine ndifika...Kudzoza kumandikhudza ine pa chinachake, ndiye ine ndimabwerera kuti ndikafufuze mawuwo. Tsopano, apa, ine ndikulephera kuwatchula mawuwo, kapena sindingathe—sindingathe kulitchula ilo. Koma, mmenemo, Ambuye anandipatsabe ine njira. Ine ndimapita ndi kukafufuza

chimene mawu amenewo amatanthauza, kenako ine ndimapeza izo. Mukuona? Zikatero ine ndazipeza izo, aponso. Mukuona?

175 Miyamba ndi dziko lapansi *zidzachoka*, tsopano, mawu awa amatanthauza, “kuchoka ku mawonekedwe amodzi kupita kwa ena.” Izo sizimatanthauza “kutheratu psyiti,” monga liwu la Chingerezi limatanthauzira, *kuchokapo*, ndi kuthetsedwa psyiti. Koma liwu la Chihebri, kapena liwu la Chigriki apa, silimatanthauza *kuchokapo*; ilo limatanthauza, “kuchoka ku chinthu china kupita kwa china.” Taonani, koma, “kuchoka ku chikhalidwe chimodzi,” iwo amatero, “kwa china.”

176 Tsopano zindikirani, Paulo anagwiritsa ntchito amenewo, ngati mukufuna kuti muwerenge izo tsopano. Mulembe igo, mukhoza kukawerenga nthawi ina. Mu Tito 3:5, Paulo akugwiritsa ntchito liwu lomweli, kutanthauza kusinthidwanso kwa munthu, kuti munthu wachoka kwa wochimwa wapita kwa woyera, osati kuthetsedwa psyiti. Pamene munthu asinthidwa, iye sanathetsedwa psyiti, koma iye ndi munthu wosinthika. Iye wasinthidwa kuchoka ku chimene iye anali kupita ku chimene iye ali, osati kuthetsedwa psyiti.

177 Yesu anagwiritsa ntchito mawu omwewo mu Mateyu 19:28; tsopano, osati 28:19. Tsopano, 19:28, Iye anati kwa iwo, “Inu mudzakhalala ndi Ine mu Ufumu wa Atate Anga, kusinthidwanso,” inu mwaona, “kusinthidwa,” pamene inu mwasinthidwa. Iye anagwiritsa ntchito mawu omwewo.

178 Ndipo Iye anagwiritsa ntchito mawu omwewo pamene Iye anati, kwa mwana wa bulu, anati, “Mmasuleni mwana wa buluyo, ndipo msiyeni iye azipita.”

179 Ananenanso chinthu chomwecho pa kuuka kwa Lazaro, “Mmasuleni iye! Msintheni iye! Iye wamangidwa; msiyeni iye azipita!”

180 Kodi izo zikutanthauza chiyani? Dziko lapansi lidzamasulidwa m’manja mwa Satana. Ilo lidzamasulidwa. Ilo lidzamasulidwa ku ndale, lidzamasulidwa ku machitidwe achipembedzo; kuti ligwiritsidwe ntchito ku Ufumu wa Mulungu, kuti udzakhazikitse iwo pano pa dziko lapansi. Koma bola ngati ilo liri mmanja mwa Satana, ndale. . . Satana wolamulira wa dziko lapansi, ndi mwini wake; ilo linali lake, koma tsopano Khristu waliwombola ilo.

181 Nthawi ina, ine ndinali chuma chake, koma osati pano. Nthawi ina, mkazi wamng’ono ameneyo anali chuma chake, koma osati pano. Mwaona, Iye anabwera kuti adzamasule kugwira kwa izo. Iye anamasula kugwira kwa tchimo, kwa Satana, pa moyo wanga, pa moyo wanu, ndipo tsopano ife sitiri ake.

182 Kodi mwandimvapo ine nthawi zambiri ndikunena, mu pemphero, “chotsani manja anu pa chuma cha Mulungu”? Mukuona? Amen! Mukhale ndi chikhulupiriro chodzitengera

zanu. Umenewo ndi ufulu wanu. “Chotsani manja anu pa mkaziyo! Chotsani manja anu pa mwamunayo!” Mwaona, chikhulupiro chidzachita izo. Oh, mai! Osati kulithetseratu psyiti ilo, koma, basi, “Kuchotsa manja anu pa ilo,” kulimasula ilo, kulisiya ilo lizipita, kulichotsapo ilo. Ilo limasintha.

¹⁸³ Dziko lapansi lidzasintha. Ndale zidzasintha. Zipembedzo zidzasintha. Zipembedzo zidzapita. Ndale zidzapita. Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa.

¹⁸⁴ Ife timawerenga mu Yohane, timamuwerenga Yohane mu Chivumbulutso 6:14, onani, “ilo linasamuka ngati mkwamba.” Baibulo linanena a...kuti ilo...Yohane anati, “Ndinawona kumwamba ndi dziko lapansi zinasamuka ngati mkwamba.” Yohane, Chivumbulutso 6:14.

¹⁸⁵ Yesu anati, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita,” kapena, mawu ena, “miyamba ndi dziko lapansi zidzasinthidwa.” Mwaona, anagwiritsa ntchito mawu omwewo aponso.

¹⁸⁶ Ayi, osati kuthetsedwa psyiti. Pakuti, kenako, mu Chivumbulutso 21:2 mpaka 24, iye anawona Yerusalemu Watsopano akutsika pansu kuchokera kwa Mulungu kuchoka Kumwamba, ndipo atakhala pa dziko lapansi ili. Izi sizikutanthauza kuti ilo lidzawonongedwa psyiti. Machitidwe adzasinthidwa.

¹⁸⁷ Daniele anawona chinthu chomwecho. Thanthwe linakantha dziko, linasemedwa popanda manja; ndi chithunzi chonse cha machitidwewo chinasweka ndipo chinakhala ngati mankhusu padwale lopunthira mu chirimwe, ndipo mphepo inanyamula izo. Ndipo Thanthwelo, Palokha, linakula kukhala Phiri lalikulu limene linaphimba dziko lapansi. Penyani Phiri limenelo tsopano, pang’ono pokha. Phiri limenelo linaphimba dziko lapansi.

¹⁸⁸ Ndiponso, ife tikupeza apa, cha mu, aponso, mu Chivumbulutso mmenemo, ilo linati, “Mafumu a Dziko Latsopano adzabweretsa ulemu wawo ndi ulemelero mmenemo.” Mu dziko lapansi, pakukhala...Yerusalemu Watsopano wakhala pa dziko ili. Mwaona, ilo linangosinthidwa.

¹⁸⁹ Ndinu mwamuna yemweyo, mu thunthu, amene inu munali pamene Mulungu anakuitanani inu, mkazi yemweyo. Koma, inu mwaona, chimene icho chinachita, iko kunali kubadwanso. Moyo wakale unapita. Chikhumbo chakale chapita. Pamene, inu munkakonda kumwa, ndi kutukwana, ndi kukangana, ndi kudyana, ndi kuthamangathamanga, ndi makhalidwe, chinthu chimenecho chinangofa. Mukuona? Koma tsopano mumagwiritsidwa ntchito...Ndiye inu munali chida cha Satana; tsopano inu munawomboledwa.

¹⁹⁰ Ndipo ndicho chimene dziko liti lidzakhale, mwanjira yomweyo, kuwomboledwa, Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano.

¹⁹¹ Chimodzimodzi monga inu, “Inu ndi cholengedwa chatsopano.” Ndipo mawu a Chigriki pamenepo, aliyense akudziwa, anati, “Inu ndi cholengedwa chatsopano.” Ameni! Cholengedwa chatsopano mu kachisi wakale yemweyo. Aleluya. Penyani chimene chikuchitika pano tsopano. Ulemelero! Chabwino.

¹⁹² Tsopano ife tikupeza kuti dziko lapansi ili lidzagwirizira mafumu a dziko lapansi.

¹⁹³ Ndipo, kachiwiri, mu Mateyu 5:5, Yesu anati, “Ofatsa adzalandira dziko lapansi.” Izo sizidzatero, kudzangokhala ndi dziko lina. Ilo lidzangokhala dziko lomwelo. Ndikuyesetsa kutengere—dongosolo la chiwombolo kwa inu, kale, ngati ine sindipeza china chirichonse, mwaona. Ubatizo wa Moto, pa iwo, ndi woti udzangoliyeretsa ilo ndi kudzalipanga ilo kukhala malo oyenera kuti ofatsa Ake adzakhalemo. Mukuona? Oh!

¹⁹⁴ Monga Iye anachitira nafe, chirengedwe Chake, kuti azikhalamo. Iye asanabwere mmenemo, Iye ankayenera kutipatsa ife ubatizo wa Moto; kenako Mzimu Woyera unabwera ndi kudzakhala, ubatizo wa Moto. Ndiye, pamene inu mulandira ubatizo wa Moto umenewo, ndiye Mzimu Woyera ukhoza kubwera mmenemo. Chiyani? Pamene Iwo ukutero, Iwo ukuwotcha chirichonse chotsutsana ndi Mawu, kuchichotsa mwa inu. Mukuona? Iwo sungakhulupirire china chirichonse koma Mawu, chifukwa Iwo ndi Mawu. Mukuona? Mukuona? Mukuona?

¹⁹⁵ Tsopano, icho ndi chimene ife timayankhula tsiku lina, umboni wa Mzimu Woyera. Mukuona? Umboni wa Mzimu Woyera ndi pamene iwe ukhoza kulandira Mawu; osati dongosolo lina, koma kukhala ndi kumvetsa bwino. Inu mumadziwa bwanji kuti Mawu akumveka, mukuwamvetsa Iwo? Kuwawona Iwo akudzitsimikizira Okha.

¹⁹⁶ “Chabwino,” inu mukuti, “Ine ndikuwona *ichi* chikuchita izo, ndi *icho*.” Oh, inde, udzu umakhala moyo mwanjira yomweyo. Mukuona?

¹⁹⁷ Koma iwo akuyenera kukhala Mawu onse. Kuti ukhale Mkwatibwi, iwe ukuyenera kukhala gawo la Iye. Iye ndi Mawu. Mukuona? Ndipo ndi gawo lanji la Iye? Mawu amene analonjezedwera tsiku lino pamene Iye akuyitana Mkwatibwi Wake. Kukhala gawo la Iwo. Inu mukumvetsa zimenezo? Tsopano, musa—musataye izo tsopano. Zindikirani.

Ndipo Iye akuwapanga iwo kukhala malo oyenera kukhalamo kudutsa Muyaya.

¹⁹⁸ Zindikirani, izi sizinatchulidwebe. . .Ulamuliro wa Zakachikwi uwu, zaka sauzande, si Dziko Latsopano. Mwaona, ulamuliro wa Zakachikwi ndi ulamuliro wosiyana. Ndi kumene tikudzapitako, Zakachikwi, koma zimenezo si Dziko Latsopano, Kumwamba Kwatsopano. Ayi, ayi. Amenewo

ndi malo opumulira chabe, mwaona, nthawi yopumulira, osati konse Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano; pakuti, inu mwaona, mu Zakachikwi ife tiri ndi zinthu zimene sizidzati zidzalowe Mmenemo. Ndi choyimira cha tsiku lachisanu ndi chiwiri lakale, uko ku Edeni; tsiku lachisanu ndi chiwiri, Iye analenga dziko. Tsiku lachisanu ndi chiwiri, Iye anapuma mu Edeni, ndi Zakachikwi.

¹⁹⁹ Mwaona, dziko tsopano liri ndi pafupifupi zaka sikisi sauzande, usinkhu wake. Mukuona? Zaka thuu sauzande zirizonse ilo limakhala ndi a—chiwonongeko. Mukuona?

²⁰⁰ Thuu sauzande zoyambirira, kusefukira kunabwera, ndipo Iye analidzabatiza ilo ndi (chiyani?) madzi.

²⁰¹ Thuu sauzande zotsatira, Yesu anabwera kuti adzaliyeretse ilo ndi kudzalitenga ilo, anadzagwetsera Magazi Ake pa ilo, analitcha ilo Lake. Chabwino.

²⁰² “Ine ndidzabweranso,” uh-huh, tsopano monga Mfumu ndi Mfumukazi Yake, ndipo zaka thuu sauzande zachiwiri (Kodi Iye akuchita chiyani?) Iye akubwera ndipo akudzapereka nthawi Yake yopumulira.

²⁰³ Ndipo kenako nkudzaliwotcha ilo, ndi kudzitengera ilo kwa Ake Omwe; akudzayika Nsana Wake Womwe pa ilo.

²⁰⁴ Ndipo zindikirani, osati dziko langwiro, Zakachikwi izi, ndi choyimira cha tsiku lachisanu ndi chiwiri. Kenako pakubwera Chiweruzo cha Mpandowachifumu Woyera. Mwaona, ife tikanali ndi chiweruzo. Ife tikadali mu nthawi, mu Zakachikwi. Ndi tsiku, zaka wani sauzande. Ndi chochitika cha nthawi. Osati, musazisakanize zimenezo ndi Dziko Latsopano, tsopano, chifukwa izo si zimenezo.

²⁰⁵ Inu mukhoza kunena izi kwa ine. Tsopano ine ndikungomverera kuti wina anganene ichi kwa ine, zimenezo, “Tsopano, M’bale Branham, kodi inu muchita chiyani tsopano? Inu mwamaliza ma seveni anu athunthu. Kodi inu muchita chiyani tsopano? Tsopano, inu ndi wakanyengo.” Chimene, ine ndiri. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu ali, nayenso. Zindikirani, zindikirani. “Inu mwamaliza zoyimira za nyengo. Pakuti, ngati inu muti muyike chinachake kudutsa tsiku lachisanu ndi chiwiri limenelo, inu muzimvetisa motani zimenezo? Inu mukupita kuti tsopano?”

²⁰⁶ Chabwino, ine ndiyitanira tcheru chanu ku chinachake, mwaona. Uh-huh. Mukuona? Chotero, ine sindiri kunjja—ine sindiri kunjja kwa nyengo, panobe. Ine ndiri ndi Lemba lina apa. Ndipo, kumbukirani, zonse za Ilo zikuyenera kukwaniritsidwa, chidutswa chirichonse cha Ilo. Mukuona?

²⁰⁷ Tsopano inu mukuti, “M’bale Branham, inu mukuyesera kuyika chinachake kutali kudutsa tsiku lachisanu ndi chiwiri limenelo, sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri limenelo.”

208 Monga Mulungu anapanga dziko lapansi ndi kugwira ntchito masiku asanu ndi limodzi, ndipo anapuma lachisanu ndi chiwiri, chinali kokha choyimira cha nthawi, nthawi. Koma ine ndangonena kumene apa, ife timakhala Amuyaya.

209 “Chotero mtundu wanu uli kuti tsopano? Inu munanena kuti ndinu wofanizitsa. Chotero, inu, mwamalizitsa zoimira tsopano.” Ayi, ine sindinatero. Tiyeni tiwone ngati ife tiri nazo.

210 Tiyeni tipite ku Levitiko, mmbuyo mu mutu wa 23 wa Levitiko. Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire mu Levitiko, pamene ife tinali Lamlungu lathali, kapena lathali. . . Ichi ndi chimene chinandipatsa ine lingaliro, pomwe pano. Mutu wa 23 wa Levitiko, ndi ndime ya 26.

211 Tsopano kumbukirani, pali masiku asanu ndi awiri a phwando. Phwando la malipenga, phwando la—la makachisi, phwando la kuweyula mitolo, a . . . Zonse izi, alipo masiku asanu ndi awiri a phwando lalikulu, chimenecho chinali choimira chabe cha Mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mpingo. Ndipo inu mukukumbukira ndi masabata angati amene analipo pakati pa limodzi ndi limzake? Mwaona, masabata asanu ndi awiri pakati pa pentekoste ndi malipenga, imene inali Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Ndipo panali masiku asanu ndi awiri a phwando, amene akuimira Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Musunge manambala anu aziyenda.

212 Mukuti, “Chabwino, tsopano, M’bale Branham, inu mwatsiriza. Inu mwapeza zisanu ndi ziwiri zanu.”

213 Chabwino, tiyeni titenge phwando lotsiriza, lomwe liri phwando la makachisi. Tsopano zindikirani apa mu ndime ya 36.

Masiku asanu ndi awiri inu muzipereka zopereka zopangidwa ndi moto kwa AMBUYE: pa tsiku lachisanu ndi chitatu—pa tsiku lachisanu ndi chitatu padzakhale msonkhano wopatulika (pali nthawi ina yopatulika ikudza). . . msonkhano wopatulika kwa inu; ndipo inu mudzapereka chopereka chopangidwa ndi moyo kwa AMBUYE: ndipo ndi msonkhano wopatulika; ndipo inu musagwire ntchito yochuluka mmenemo.

214 Tsopano ife tiri ndi “tsiku lachisanu ndi chitatu.” Tsopano, alipo masiku asanu ndi awiri okha, koma apa ife tikukamba za “tsiku lachisanu ndi chitatu,” msonkhano wopatulika, msonkhano. Zindikirani, “Musadzagwire ntchito mmenemo.” Tsiku lachisanu ndi chitatu, ndi (chiyani?) abwerera ku tsiku loyamba. Bwanji, ilo likuyankhula za Muyaya, pamene iwo ukugudubuzika popanda malo oyimira. Amen. Kodi inu mukuziwona izo?

215 Zindikirani, izo zinalinso pa tsiku lachisanu ndi chitatu ili. Tsiku lotsiriza, tsiku la phwando la kachisi, zindikirani zitatha zimenezo, tsiku la phwando lotsiriza litadutsa, utatha

M'badwo wa Mpingo wotsiriza, atapita masiku asanu ndi awiri athunthu otsiriza pa dziko lapansi, zitatha Zakachikwi, mpamene Msonkhano Wopatulika uwu ukubwera.

²¹⁶ Kumbukirani, ili ndi phwando la makachisi, *makachisi*, “malo osonkhanirana.” Amen! Kumene, “Mu Zakachikwi,” Baibulo linati, “iwo adzamanga nyumba; iwo adzakhalamo.”

²¹⁷ Koma mu Dziko Latsopano, Iye anapita kale ndipo anakakonzana malo. Iwo akumangidwa. Ife tiribe kanthu kochita ndi kumanga kwa izo. Amen. Wamuyaya! Oh, ine ndikungowakonda Mawu amenewo! Mai! Msonkhano Wopatulika, tsiku lachisanu ndi chitatu. Chimene, ndi masiku asanu ndi awiri okha. Ndiye pa tsiku lachisanu ndi chitatu, zimene zikubwereranso ku tsiku loyamba aponso, likubwereranso ku tsiku loyamba, tsiku lachisanu ndi chitatu ndi Woyera Mso- . . . Msonkhano.

²¹⁸ Zindikirani, masiku asanu ndi awiri, ali kokha ndi chochita ndi chirengedwe chakale, nthawi ya dziko. Masiku asanu ndi awiri, amenewo ndi Zakachikwi, tsiku lopuma. Monga Mulungu anagwira ntchito masiku asanu ndi limodzi, anapumula lachisanu ndi chiwiri; Mpingo umagwira ntchito masiku asanu ndi limodzi, ndipo umapuma mu lachisanu ndi chiwiri, koma inu mukadali mu gawo la nthawi. Ine sindikuyankhula za Muyaya.

²¹⁹ Koma, inu mwaona, palibepo chinthu chotero monga masiku asanu ndi atatu; inu mumabwerera ku tsiku loyamba kachiwiri, mwaona, tsiku loyamba.

²²⁰ Sabata limakamba za lamulo lakale, limene linkayenera kuchokapo. Kusunga kwa sabata, kumene “kunachokapo,” kapena ndinati, “kusinthidwa kukhala lina.” Ilo silinachoke; ilo linangosintha kuchoka ku lamulo lakale, losunga tsiku linalake la sabata.

²²¹ Yesaya, mutu wa 19, anati, ine ndikukhulupirira 28:19, anati, “Langizo likuyenera kukhala pa langizo; apa pang’ono, ndi apo pang’ono.” “Gwiritsitsani kwa chimene chiri chabwino.” “Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ndidzayankhula kwa anthu awa. Ndipo apa pali mpumulo.” Mukuona?

²²² Inu mumalowa mu Moyo, osati kusunga tsiku kapena mthunzi. Paulo anati, cha uko mu Ahebri mutu wa 4. “Inu mumasunga masiku ndi mithunzi, ndi zinthu monga izo; ndikuchita mantha ndi zokuchitikirani zanu.” Mwaona, ife sitimadutsa kukalowa mmasiku ena ndi madongosolo. “Inu mwadutsa kuchoka ku imfa mwapita ku Moyo Wamuyaya,” osati masiku ndi nthawi. Inu mwadutsa kukalowa mu Muyaya. Ndiwo woyera msonkha- . . . msonkhano, msonkhano, kani.

²²³ *Masiku asanu ndi awiri*, penyani, amene “anachokapo,” kapena, ine ndanena, adza “sintha kukhala lina.” Masiku asanu

ndi atatu akuchita ndi chirengedwe chatsopano, mwaona, osati chirengedwe chakale. Masiku asanu ndi atatu ndi chirengedwe chatsopano.

²²⁴ Pakuti, linali tsiku lachisanu ndi chitatu limene Ambuye wathu anauka kwa akufa. Ndi umenewo msonkhano wanu wina, chiyero; osaganizira za masabata, nkomwe, kapena phwando la makachisi, phwando la *ichi*, ndi phwando la pentekoste. Yesu anauka kwa akufa, chifukwa cha kulungamitsidwa kwathu, pa tsiku lachisanu ndi chitatu. Atatha masabata asanu ndi awiri, kapena masiku asanu ndi awiri, Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo, Yesu anauka kwa akufa. Tsiku lachisanu ndi chitatu, limene liri msonkhano wopatulika, mwaona, limene liri tsiku loyamba.

²²⁵ Mwaona, inu mwatero, mwadutsa kale nthawi, ndipo mwagwera mu Muyaya kachiwiri; osati kusunga kwa masiku, ndi kusunga kwa masabata; ndi miyezi yatsopano, ndi zinthu monga zimenezo. “Koma *mwadutsa*,” kusintha mawonekedwe anu; osati kuthetsedwa psyiti. Ulemelero! “Koma munadutsa kuchokera ku imfa munapita ku Moyo Wamuyaya.” Oh, chimene Baibulo limatiphunzitsa ife! Mwaona, kudutsa kuchokera ku chimodzi kupita ku chimzake.

²²⁶ Chabwino, “kudutsa,” sabata lakale lachokapo. Yesu anawuka pa tsiku lachisanu ndi chitatu. Limenelo linali tsiku laulemu, lopatulika. Ndipo ilo silinali tsiku; chifukwa tsiku, nthawi, inali itatha. Iyo inali itapita mu Muyaya. Mwaona, ilo linasunthira kubwerera ku tsiku loyamba kenanso. Mukuona?

²²⁷ Muyaya umakhala ngati a—mkombelo. Inu simungapeze ngodya kwa iwo. Inu simungapeze malo oimikira mu mkombelo wangwiro. Inu mumangopitirira pitirira. Ine sindikusamala kuti mupita patali bwanji, inu mukupitabe. Inu mukhoza kuyamba kuzungulira monga *chonchi*; kudutsa pansi, kudutsa padziko lapansi, kupita kupyola dziko lapansi, inu mukadali kupitabe-. . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

²²⁸ Zinthu zonse zimene zinalengedwa pansi *apa*, ndi zopotozedwa, osati zolengedwa, ndi Satana, zidzagwa pamene belu lalikulu lagolide lidzalira ndipo Lipenga lidzalira.

²²⁹ Ndipo mmbuyo kutali uko pachiyambi, kumene chimango chinapangidwa mu Edeni, pamene munthu anabwera pa dziko lapansi ndipo iye anadzagwa, mwanawankhosa wamng’ono anadzakhetsa magazi ake, zimene zinkayankhula za Mwanawankhosa wamkulu anali akubwera kudzakhetsa Magazi Ake. Kalvare anadzutsa mtanda, umene unamangiridwa Chipangano Chakale; kwa iwo amene analungamitsidwa, ankayembekezera Iwo. Ndipo mu kanyengo katsopano aka, pa Kudza kwa Ambuye, pa Dziko Latsopano, chingwe cha chipulumutso (Magazi, Mphamvu yowomboledwa imene ine ndikuikamba, ndipo kudutsa mu kachitidwe komweko

awombola awiri onse munthu ndi dziko lapansi) adzawuka mpaka mu Muyaya kachiwiri. Ndipo Nyanja ya Moto idzanyeketsa chirichonse chimene chiri chopanda umulungu ndi chosakonzedweratu kwa Iwo. Kodi inu mukuziwona izo?

²³⁰ Zindikirani, tsiku lachisanu ndi chitatu, Yesu anawuka kwa kulungamitsidwa kwathu. Mfumu Yamuyaya, ndi Ufumu Wamuyaya zoti zibatizidwire, ku Moyo Wamuyaya. Osati masiku asanu ndi awiri; zinalibe chochita ndi masiku aliwonse. Izo zikukamba za ena, Amuyaya, akubwera; kuyankhula za nthawi Yamuyaya, Dziko limene ine ndikulikamba.

²³¹ Ndipo, zindikirani, atatha masiku fifite, kapena masabata asanu ndi awiri kuchokera pamenepo, panadzabweranso msonkhano wina wopatulika. Chinachitika ndi chiyani? Mzimu Woyera unagwa pa Tsiku la Pentekoste, pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. . . Kapena, tsiku lachisanu ndi chitatu, kani, tsiku lachisanu ndi chitatu, unadzagwa pa tsiku lachisanu ndi chitatu. Anali masabata asanu ndi awiri mtsogolo, ndendende, chitachitika chiukitsiro Chake, mwaona; chotero izo zingakhale kaseveni kuchulukitsa zimenezo kachiwiri, kuzibwezera izo mmbuyo mozungulira ku tsiku loyamba la sabata kenanso, ndendende. Mukuona?

²³² Ndi umenewo msonkhano wanu wopatulika, osati kukhala ndi chirichonse chochita ndi zinthu zenizeni. Izo zikudutsa pamenepo. Izo zalowa mu Ufumu wa Mulungu, ndi Moyo Wamuyaya, ndi okonzedweratu amene sanachite kuyamba konse. Izo sizinachite kuyamba pa tsiku lililonse. Inu simunapulumsidwe tsiku lieilonse. Inu munali nthawizonse opulumutsidwa. Amen. Yesu anangobwera kudzawombola izo; koma inu munapulumsidwa, kuchokera pachiyambi, chifukwa inu munali ndi Moyo Wamuyaya, kuyamba ndi kuyamba.

²³³ Nsomba ya mphuta singakhale konse ntchira kapena mbululu. Iyo ikhoza kukhala mmadzi omwewo ndi iyo, koma iyo inali, kuchokera pachiyambi, mphuta. Ukonde unangomugwira iye, mwaona, koma iye anali chimenecho kuchokera pachiyambi. Apo pali icho. . .

²³⁴ Tsopano, ife sitinachokere mu timbadwo. Ife ndi choncho? Ife tiri mu Lemba lomwe. Patapita masiku fifite, izo zinadzafika.

²³⁵ Mwaona, eyiti sangakhoze kuwerengedwa limodzi ndi sabata. Mwaona, iwo sangakhoze kuwerengedwa, masiku eyiti mu sabata. Inu simungakhoze kuchita zimenezo, mwaona, chifukwa alipo masiku seveni okha mu sabata. Awerengeni iwo mwanjira iliyonse imene inu mukufunira. Lamlungu ndi tsiku loyamba la sabata. Mwaona, inu mawerenge seveni, ndiye inu mukuyenera kubwerera ndi kukayambiranso kachiwiri. Werengani seveni, mubwereranso ndi kupitanso. Mukuona?

²³⁶ Ndipo ife tinakhala kudutsa mu zoyimira zonsezi mkati muno, koma, pamene inu munafika pa lachi eyiti, inu mumapita

ku Muyaya. Inu simumabwera mwa malamulo, ndi miyambo, ndi madongosolo. Inu mumabwera mwa kukonzedweratu. Amen! Ulipo weniweni, msonkhano woyera! Mukuona? Ndipo ife tikutsirizitsa m'badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, m'badwo wa mpingo, m'badwo wa Chipentekoste. Kodi inu mukuziwona zimenezo? Ife tikulowa mu msonkhano wopatulika umenewo. Ife tikulowa mu Umuyaya weniweniwo, woona, Umuyaya, kumene Mpingo ukuyitanidwa; osati kupita ku siteji ina, chipembedzo china, koma kukalowa mu Muyaya ndi Mfumu yawo Yamuyaya. Mukuona? Ife tiribe izo nkomwe, palibe chinthu chotero monga masiku, ndi zinthu, ndi nthawi. Inu mwadutsa kulowa mu Muyaya, kumene inu munachokerako. Inu munali Kumeneko, kuyamba ndi kuyamba. Mukuona?

²³⁷ Ngati inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ulipo mtundu umodzi wokha, umenewo ndi Mulungu, ndipo ndinu chikhumbo chofotokozedwa. Mukuona? Ngati inu. . . Ngati inu simuli, inu simudzakakhalako kumeneko, mulimonse. “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye.” Mukuona? Chimene, “kuchokapo,” zinthu zakale zonsezi; koma Zinthu zimenezi sizitero, chotero izo zimayankhula za Muyaya. Mzimu Woyera ndi Wamuyaya. Ndiye, inu muli mu Muyaya, kumene inu munali nthawi zonsezi, koma inu mwangozindikira kumene chimene chinachitika.

²³⁸ Mwaona, inu munapangidwira cholinga Chamuyaya, chifukwa inu munali—mawonetseredwe a chikhumbo chimene chinali mwa Mulungu, lingaliro limenelo la inu ndipo anakufotokozani inu; ndipo Iye analenga dziko lapansi kuti adzakutengereniko inu, ndi kudzakupangani inu munthu. Ndipo tchimo linadzabwerapo ndipo linadzapotoza njira Yake. Inu munabwera, mulimonse, koma inu munatayika limodzi ndi dziko. Chotero Iye anabwera ndipo anadzakuwombolani inu, chikhumbo chofotokozedwa, ndiponso akuliwombola dziko lapansi ili mwanjira yomweyo. Ndiye, cholinga Chake chikufunzululika. Mukuona? Oh! Aleluya! Oh, izo zikundichitira ine ubwino wochuluka kwambiri, tangoganizani za zomwe ziri mtsogolo!

²³⁹ Tsopano, mu Aefeso 1:10, zikutchedwa. . . Tsopano, ngati mukulemba izo, Aefeso 1:10, amatchedwa, osati kam'badwo, osati tsiku lachisanu ndi chiwiri. Izo zikutchedwa, “Chidzalo cha nthawi.” Ndipo pamene “chidzalo cha nthawi” chafika, apo ndi pamene nthawi yakwaniritsidwa. Pamene palibenso nthawi, ndiye inu mumapita mu Muyaya, utatha m'badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, ndipo izo ziri; M'badwo wa Luther unatha, m'badwo wa Methodisti unatha, m'badwo wa Pentekoste unatha. Ndipo tsopano inu mukukalowa mu (chiyani?) Muyaya; palibenso maseveni, palibenso ma firii, palibenso zinazo. Iwo ali mu Muyaya, kumene kulibe nthawi yoteroyo ngati manambala, ndi nthawi, ndi zinthu. Amen! Oh, mai! Inu mukuziwona izo

tsopano?

²⁴⁰ Kapena, nthawi itatha kukwaniritsidwa, tchimo lonse lapita, lachotsedwapo, pa Zakachikwi, pa Chiweruzo cha Mpandowachifumu Woyera wawukulu. (Choimira, mwa Mzimu Woyera.) Dziko litatha kuyaka moto ndi kubatizidwa, ndi ubatizo wa Moto woyera wochokera Kumwamba; tchimo lonse lapita, majeremusi onse apita, adierekezi onse apita, mayesero onse apita, zoyipa zonse zapita. (Choimira tsopano.) Ndiye kodi Mulungu akuchita chiyani? Iye akhoza kukhala pa dziko lapansi, mwaona, chifukwa tchimo lonse lapita.

²⁴¹ Ndicho chinthu chomwecho chimene Iye amachita pamene Iye akupatsani inu ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Moto. Iye akhoza kubwera ndi kudzakhala ndi inu, ndipo ife tikhoza kukhala mu malo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, chifukwa ife tiri kale mwa Iye. Osati ife “tidzakhala.” Ife tsopano tikukhala mwa Khristu Yesu. Kodi timalowa bwanji mmenemo? Mwa ubatizo umodzi wa Mzimu Woyera. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mwa Khristu,” chimene, ife tiri tsopano. Sikuti tidza “khala” mwa Khristu; ife tiri! Iye ndi Mfumu yayikulu yauzimu pa Mzimu umene uli mwa ife, chifukwa ife tinali mwa Iye pachiyambi.

²⁴² Mwaona, Mulungu, pachiyambi, pamene Iye anaganiza za inu ndi kuganiza za ena monga choncho, ankaganiza za Iyemwini kukhala wogwirika. Amenewo anali maganizo Ake. Mukuona? Chotero, Iye anawawonetsera malingaliro Ake mwa Mawu. Iye anati, “Mulole pakhale.” “Mulole pakhale,” ndipo apo panali. “Mulole pakhale,” ndipo apo panali.

²⁴³ Kenako, patapita kanthawi, Iye ankapitirira kumati “mulole pakhale,” mpaka anthu anati, tsiku lina, “Musalole kuti Mulungu ayankhule!”

²⁴⁴ Iye anati, “Tsopano Ine ndiziyankhula kwa iwo kupyolera mwa mneneri.” Mukuona? “Kuyambira pano, Ine ndiziyankhula kwa iwo kupyolera mwa mneneri.”

²⁴⁵ Ndipo mneneriyo anati, “Zidzafika podzachitika; kudzakhala,” ndipo izo zinatero, ndipo izo zinatero. Ndipo izo zinaterodi, ndipo izo zinaterodi, mwaona, monga choncho basi. Inu mukumvetsetsa izo tsopano?

²⁴⁶ “Chidzalo cha nthawi” chabwera nthawi itatha kukwaniritsidwa. Tchimo lapita, pambuyo pa ubatizo wa dziko lapansi, ubatizo wa dziko lapansi utatha kulipanga ilo kukhala malo oyenera; palibe matenda, palibe majeremusi; palibe minga, palibe nthula; palibe imfa, palibe chisoni, palibe zopweteketsa mtima; palibe ukalamba, palibe choyimira imfa; palibe cholakwika; chabwino; palibe chachirengedwe. Muyaya!

²⁴⁷ Kenako, chikhumbo Chake chikuwonetseredwa chifukwa icho chinali kumeneko, poyamba, kuyamba ndi kuyamba.

Ndicho chimene Iye ankaganiza. [M'bale Branham akuwonetsera pa bolodi—Mkonzi].

248 Ndipo kenako chinachitika ndi chiyani? Iye anamuyika Adamu ndi Eva kuno pa dziko lapansi, ndipo anati, "Muchulukane tsopano ndipo mulidzadzitse dziko lapansi." Matupi awo onse anali atayikidwa apa, kuti inu muzidya ndi kupanga thupi lanu. Imeneyo inali njira imene Iye anali nayo yochitira izo.

249 Koma tchimo linadzabwerapo ndipo linadasokoneza dongosolo Lake. Iye akupitirirabe, chimodzimodzi basi, nthawi imatero.

250 Koma kodi Yesu anachita chiyani? Mulungu anadzabwera pansu ndipo anadzadziwonetsera Yekha mmawonekedwe a Munthu, munthu wokhalapo; anapereka moyo Wake, mmalo mokhala kuno. Chimene, Iye anali Mfumu, koma Iye anadzipereka Yekha kuti awawombole ena onsewo. Inu mukumvetsetsa zimenezo?

251 Ndipo pamene izo zonse zidzatha, ndiye izo zidzakokedwera mmbuyo momwe, ndipo cholinga cha Mulungu chidzakwaniritsidwa. Ndi ameneyo Mfumu Yamuyaya kenanso ndi omumvera Ake Amuyaya, akuwonetseredwa mu thupi la munthu, ndendende momwe Iye anali nazo izo; tchimo likuchotsedwapo; mdierekezi wapita; zonse zachitika tsopano.

252 Chidzachte izo ndi chiyani? Dziko lapansi lino silingakhale malo oti Kumwamba kudzakhalepo tsopano. Tayang'anani pa ilo, tchimo. Ilo likuyenera lidzayeretsedwe.

253 Palibe mwamuna, palibe munthu, palibe mkazi, mnyamata, mtsikana, ine sindikusamala kuti iye ndi ndani, amene ali woyenera kupita pa guwa, kapena ngakhale kudzinenera kuti ndi Mkhristu, wopanda kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Inu mulibe ufulu wopita ku mgonero wa Ambuye, kapena mgonero uliwonse, kusambitsidwa mapazi, kapena chirichonse, kufikira mutayeretsedwa ndi Moto Woyera wa Mulungu.

254 Palibe munthu amene ali ndi ufulu wolalikira pokhapokhapo ngati inu, monga Mose, mutakomana ndi Iye kunja uko pa malo opatulika amenewo, Lawi la Moto lija litapachikika pamenepo, pamene iye akudziwa kumene iye ali. Mukuona?

255 Zindikirani momwe, momwe ife tikupitira. Utatha ubatizo wa Moto wa mdziko, majeremusi onse apita, ukupangitsa iwo kukhala malo oyenera ndiye kuti Kumwamba kudzakhale pano pa dziko lapansi.

256 Choimira, tsopano, chokhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu; kudutsa kuchokera ku ichi, wodetsedwa monga mkazi wamng'onoyo anali, kulowa mu chikhumbo chowonetseredwa cha Mulungu. "Tsopano ndife ana a

Mulungu,” osati ife *tidzakhala*. Ife ndi zikhumbo za kuganiza kwa Mulungu. Mukuona?

257 Tsopano inu mukuti, “Chabwino, tamuwonani wansembe uyu. Kodi iye sanali mwana wa Mulungu?” Zinatsimikizira kuti iye sanali. Iye sanakhoze kuzindikira chiyani? Kodi iye anati, “Ine ndimakhulupirira Baibulo?” Ndithudi. Koma iye sanathe kuwazindikira Mawu ofotokozedwa a oralo. Iye anangokhala ndi kuphunzira kwaluntha kokha kuchokera kwa gulu lina limene linalipo iye asanakhalepo.

258 Ndipo ndi chinthu chomwe chomwecho lero! Mukuona? Ine ndikudziwa kuti izo nzolimba, koma ndicho Choonadi.

259 Apo panali Mawu, monga anayankhulidwa ndendende a tsiku limenelo; ndipo, iye, komabe iye anali sikolala, komabe iye anali munthu wodziwika, koma iye sankakhoza kuwazindikira Iwo. Bwanji? Ziribe kanthu kaya iye anali sikolala chotani, chirichonse chonga icho, iye analibe chomuimira cha kukonzedweratu. Mukuona?

260 Okonzedweratu okha adzakhala okhawo amene adzachite izo; okhawo angakhale. Ndipo inu nokha mukhoza kuchita zimenezo... Chifukwa, taonani, izo zikutsimikizira kukonzedweratu. Chifukwa, ngati inu muli ndi Moyo Wamuyaya, inu muyenera kuti munali gawo la Mulungu nthawi zonse, chifukwa Iye ndi Mmodzi yekhayo amene ali Wamuyaya. Inu mukuwona zimenezo? Oh, mai! Taganizani za zimenezo.

261 Tsopano taonani zimene zikuchitika kudutsa mu Zakachikwi zazikuluzi. Tchimo lonse litapita, Zakachikwi tsopano zayambika, ndi nthawi tsopano imene Mzimu Woyera ukutenga malo Ake.

262 Chimodzimodzi monga momwe Iye akuchitira mwa ife, “tikudutsa kuchokera ku imfa tikupita ku Moyo,” kumakhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu, mu Kukhalapo Kwake kwaulemlero. Ngakhale imfa yathupi idzachoka pamene; chimodzimodzi monga momwe imfa yauzimu yachoka tsopano.

263 Palibepo chinthu chonga imfa yauzimu tsopano, kwa a—kwa a—woyera wobatizidwa wa Mulungu. “Ngakhale iye anali wakufa, komabe iye adzakhala moyo. Aliyense amene adzakhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Malemba onse, Iwo akuyenera kukwaniritsidwa. Mukuona? Inu simungafe. Inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Chinthu chokhacho, Muomboli wakupangani inu kuzindikira izo. Ndipo inu nthawizonse munali Chimenecho, ndipo ndi chifukwa chake inu mukuliwona tsiku limene inu mukukhalamo. Ndi angati akuliwona ilo? Kwezani dzanja lanu. Mukuona? Zikomo inu. Mukuona? Tsiku limene ife tikukhalamo, inu mukulizindikira ilo.

264 Tsopano, Amethodisti anati, “Pamene inu mufuula, inu muli nawo Iwo.” Ambiri a iwo anafuula ndipo sanakhale nawo Iwo.

265 Apentekoste anati, “Pamene muyankhula mmalirime, inu muli nawo Iwo.” Ambiri anayankhula ndi malirime, ndipo sanakhale nawo Iwo.

266 Taonani momwe, mitundu yonse ya maonekedwe Afarisi amenewo anali nayo, koma pamene Mawu anawonetseredwa, iwo sanawazindikire Iwo. Mukuona? Mukuona?

267 Ndipo ngati inu muli Mkwatibwi, Mkwatibwi amakhala gawo la Mwamuna. Ndipo ngati. . .Malo okhawo omwe inu mudzawazindikire konse Iwo, ndi kuzindikira kuti ndi gawo lanji la Mwamuna ameneyo (Mawu amenewo) amene inu muli, kapena inu simungazindikire kukhala Mkwatibwi. Ndi angati akuziwona zimenezo? Mukuona? Mukuona? Inu mukuyenera kuzindikira malo anu.

268 Inu simungathe kuzindikira a wina. Nanga bwanji—bwanji ngati Mose akanabwera ndi uthenga wa Nowa? Ndipo Nowa anali gawo la iwo, koma izo sizikanagwira ntchito. Nanga bwanji ngati—ngati—ngati—ngati Yesu akanabwera ndi Uthenga wa Mose? Izo sizikanagwira ntchito. Mwaona, iwo unali m’badwo wosiyana, iwo unali uneneri wosiyana, gawo losiyana la Mawu linkayenera kuti likwaniritsidwe pamenepo. Iwo anali mu tsiku lina la sabata. Sichoncho, ntchito ya Lachiwiri singachitike Lachitatu. Ndipo Lachitatu ikuyenera kuchitidwa Lachitatu. Mukuona? Loweruka ikuyenera kukhala ntchito ya Loweruka. Mukuona?

Ndipo, iwo, iwo anazindikira, “Oh, Mose, ife tiri naye Mose.”

269 Iye anati, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanandidziwa Ine, pakuti iye anali amene anayankhula za Ine. ‘Ambuye Mulungu wanu adzadzutsa mneneri wonga ine.’” Mukulimva lingalirolo? Oh, mai! Mukuona?

270 Kenako Yesu anati, mu Yohane 14, “Pamene Iye, Mzimu Woyera, adzabwera, Iye adzabweretsa zinthu izi ku kukumbukira kwanu, mwaona, kukuwonetsani inu tsiku limene inu mukukhalamo. Ndipo kenako, chinthu china chimene inu mudzamudziwire Iye, Iye adzakuwonetsani inu zinthu zimene ziri nkudza,” mwaona, mwaona, kubwerera ku uneneri kachiwiri, “pamene Iye adzabwera.” Mukuona?

271 Mu Dziko Latsopano ndi Miyamba Yatsopano, simudzakhalanso mdima nkomwe, pamene Dziko Latsopano ili liti lidzabwere. Mdierekezi adzamangidwa. . .Satana, iye akadali womasulidwa tsopano; iye ndi woneneza. Koma mu Dziko Latsopano, iye adzamangidwa ndi kuponyedwera mu Nyanja ya Moto, mu Moto woyera uwu.

272 Kenako, mu Dziko Latsopano ili, tiyeni tiyang’ane pa ilo kwa maminiti pang’ono tsopano. Mu Dziko Latsopano ili,

mlengalenga simudzakhalanso mwakuda; ayi, izo zikuchokera ku themberero, mwaona. Simudzakhalanso mwakuda ndi mitambo yokwiya. Mphepo sizidzawombanso kudutsa ilo kachiwiri monga choncho. Ayi. Izo sizidzagwetsa konse mitengo, ndi kugwetsa nyumba, ndi kutembenuza zinthu. Mphenzi ndi mkwiyo sizidzawomba kuchokera kwa Satana kutsidya kumeneko, ndi kupha munthu akuyenda mu msewu, kapena kuwotcha nyumba. Mukuona? Ayi, zidzakhala zitatha. Sikudzakhalanso mvula yamkuntho imene idzasese, kapena mikuntho ndi namondwe, ndi kudzaphwasula nyumba, ndi kupha ana aang'ono, ndi zinthu. Huh-uh, sizidzakhhalako nkomwe. Kuyesera kuti ziwononge, izo sizidzakhhalako kumeneko. Satana waponyedwa kunja.

²⁷³ Ndikanakonda ndikanakhala ndi nthawi tsopano. Ine ndikuwadutsa Malemba, tsopano, kuchitira kuti tisachedwe kwambiri. Ine ndikuyenera kupempherera odwala.

²⁷⁴ Miyamba ndi dziko lapansi zakomana; Mulungu ndi munthu akuyanjanitsidwa. Edeni wobwezeretsedwa wayambapo; mwaona, themberero lonse lapita.

²⁷⁵ Chimodzimodzi monga ngati, themberero lonse la tchimo limachokapo pamene Mzimu Woyera ukulandirani inu. Mwaona, inu simumawulandira Iwo; Iwo umakulandirani inu, mwaona, chifukwa Iwo ndi chikhumbo cha Mulungu. Mwaona, ngati Iwo uli Mzimu Woyera, kutanthauza, Mzimu wa Mulungu; ndipo ndi chikhumbo, lingaliro la Mulungu, lakulandirani inu chifukwa chakuti inu munadzozedwera cholinga chimenecho. Mukuona? Komabe, inu munabadwira mu tchimo; koma Mulungu anali ndi chikhumbo chimenecho, ndipo apa inu munadzifotokoza nokha kuno pa dziko lapansi, ndipo Iye akutsika pansu ndipo akudzakutengani inu. Mwaona, inu mwabwerera *apa*; *apa* ndi pamene inu muli. Mukuona? Mwaona, tchimo lataya mphamvu yake. Uko nkulondola. Chikhumbo cha tchimo chachoka mu mtima mwanu, pamene Mzimu Woyera walowa mkati. Inu ndi munthu wobwezeretsedwa.

²⁷⁶ Ndiyeno pamene dziko likubwezeretsedwa, ndi chinthu chomwecho, apo sipangakhalenso themberero nkomwe, sipangakhalenso mikuntho, sipangakhalenso mphepo, sipangakhalenso namondwe—namondwe, kani. Inu mwayanjanitsidwa; munthu ndi Mulungu akumana. Dziko Latsopano lidzayikidwa pa kukongola kwake kwa Edeni kachiwiri. Dziko Latsopano lidzafalikira, ilo, utatha ubatizo wake wa Moto.

²⁷⁷ Tangoganizani, ilo lidzayaka moto ndi kupsya. Zammwamba zidzapsya ndi—ndi kutentha kwakukulu. Ntchito zonse za padziko lapansi zidzapsya. Madzi onse adzaphulika; iwo adzayaka ndi kudzaphulitsa onse. Chirichonse chidzaphulika. Ziphala za moto zidzaphulika ndipo, masauzande a

mailosi mlengalenga, zidzawulutsa ziphalaphala za moto. Nyongolosi iliyonse. . . Mzimu Woyera wa Mulungu udzayeretsa kachidutswa kalikonse ka tchimo lonse ndi chirichonse. Mdierekezi yense adzamangidwa ndi kudzaponyedwa mu Nyanja ya Moto, Moto wonyeketsa, mkwiyo wa Mulungu wa Moto.

278 Palibe chirombo chimene chidzakhale kumeneko kuti chikuwonongeni inu kenanso. Mukamadzayenda kumusi mumsewu, m'minda ya maluwa, sikudzakhala njoka iliyonse kumeneko kuti iwuzire pa inu ndi kukulumani inu, ndi malovu ake a chiphe. Oh, mai! Kodi izo sizidzakhala zodabwitsa? Mvetserani. Kumeneko sikudzakhala lirilonse la Dziko Latsopano limenelo lomwe lidzayikidwe pa gombe la kapinga wochita kupanga wachikasu, ngati manda; sikudzakhala mmodzi wa iwo kumeneko.

279 Munthu ndi Mulungu abwera pamodzi; Mkwatibwi ndi Mkwati. Miyamba ndi dziko lapansi zakumbatirana wina ndi mzake; Mulungu watsika kudzakhala pakati pa anthu. Kachisi Wake ali ndi iwo.

280 Sipadzakhalanso tchimo, sipadzakhalanso chisoni. Sipadzakhala konse dontho la misozi kuchokera pa tsaya la amayi, pa mwana wake. Ameni. Izo sizidzakhhalapo, pa Bwalo Latsopano limenelo. Ayi. Ilo ndi lowomboledwa. Ilo ndi la Iye, ndi la Ake amene anawomboledwa kuchokera mmenemo. Mukuona?

281 Ndipo, taonani, inu ndi gawo la nthaka imeneyo. Nkulondola uko? Ndipo pamene Iye anakuwombolani inu, Iye analiwombola dziko lapansi ndi chinthu chomwecho, ndipo inu muli limodzi kachiwiri. Oh, zingakhale zomveka mochuluka bwanji. Mukuona? Iwe ukuyenera kuwomboledwa chifukwa ndiwe gawo la izo. Ndipo ngati Magazi sanagwere pa iwe, iwe sunawomboledwe panobe; iwe sunaitanidwe. Kenako Iye akuliyeretsa ilo; ndicho chinthu chomwecho chimene Iye akuchichita mu Moto. Ngakhale, Magazi anakhetsedwa, ilo likuyenerabe kuti liyeretsedwe ndi Moto, uko nkulondola, chifukwa cha malo okhalapo Mulungu.

282 Mulungu anatenga kale malo Ake, mwakungoyankhula. Ufumu wa Mulungu uli pa dziko lapansi tsopano, mmitima ya oyera mtima Ake. Ndi zikhumbo Zake zimene Iye anaziyamba pachiyambi. Tsopano zikhumbo Zake zawomboledwa. Kodi Iye akuyembekezera chiyani? Kuti aliwombole dziko lapansi, kuti adzayike zikhumbo Zake pa ilo, kuti adzakwaniritse ndendende dongosolo Lake lokonzedweratu. Kodi inu mukuziwona zimenezo?

283 Zindikirani, kulibeko manda, kulibeko misonzi, palibe, kulibenso kukhetsa magazi. Ilo silidzanyowetsedwa ndi misonzi kapena magazi. Ayi. Sikudzakhalanso nkondo. Ayi. Kopanda

mitambo ya chisanu. Sikudzakhala chipale chozizira pa chifuwa chake; sichidzakhala pamenepo kenanso pa ilo. Dzuwa lotentha silidzakwanitsa, silidzawotcha konse udzu wake. Aleluya! Ngakhale chipululu chidzabala maluwa. “Chipululu chakale chimenecho, chomata chidzaphuka, tsiku lina, ngati duwa,” Mulungu ananena chomwecho; pamene ilo likadzawomboledwa, pamene ilo lidzakhale nawo ubatizo wake wa Moto. Pali mitundu yonse ya akaloga ndi zomata ndi chirichonse kumeneko tsopano, koma ilo liri ndi ubatizo wa Moto ukubwera.

²⁸⁴ Monga momwe munthu anali, pamene iye anali akadali ndi udani, dumbo ndi mkwiyo mwa iye; pamene ubatizo wa Moto unabwera, iwo unayeretsa zimenezo. Palibenso nsanje, palibenso kanthu; basi mwamtheradi ndi malo okhalamo a Mulungu. Ndipo, kumbukirani, zimenezo ndi nthumwi Zake zomwe ziti zidzakomane ndi Iye kutsidyako. Amen! Oh, chiyani a . . .

²⁸⁵ Imeneyo si nkhani chabe; icho ndi Choonadi. Icho ndi chimene Mulungu ananena. Icho ndi chimene Iye analonjeza. Ndicho chimene Mkwatibwi akupitako. “Ngakhale chipululu,” Iye anati, “chidzaphukira, kukhala duwa.”

²⁸⁶ Satana, tchimo, ndi ochimwa, apita, kwanthawizonse. Izo zonse zachitika; kuzisakanizira izo mpaka mu Muyaya. Ndipo zonse zimene zinapotozedwa, mngelo wamkulu uja amene anakhala pamenepo tsiku lina, Satana, amene anachita zoyipa zonsezi, adzawonongedwa. Inu mukukumbukira, Baibulo linati, “Ngati moyo umenewo sudzachita monga Iye anachitira, anati achite, Iye adzawononga ngakhale moyo umenewo.”

²⁸⁷ Koma, inu mukuona, Iye sangadziwononge Yekha ndi kukhalabe Mulungu. Kotero, ngati moyo umenewo uli wa dziko, iwo ukuyenera kudzawonongedwa. Koma ngati iwo uli Wamuyaya, ndi Mulungu, iwo sunachite kuyamba nkomwe, chifukwa ndi gawo la Mulungu ndipo sungawonongedwe. Amen! Ndi zokongola bwanji! Ndi—ndi kuthokoza bwanji, kuti Mpingo ukuyenera uziwone zimenezo!

²⁸⁸ Anthu, zonse zomwe mwachita ziri apa. Ichi ndi chimene ine ndikuyesera kunena. Ndikusiya zina za izo chifukwa ndikufuna kuti ndibwerere kwa izo kachiwiri.

²⁸⁹ Ngakhale zinthu izi, Satana, ochimwa, apita, kwa Muyaya; sadzakhala ponso. Zonse . . . Mwaona, Satana sangathe kulenga. Ngati iye atatero, iye ndi Mulungu. Mukuona? Iye akhoza kungopotoza chimene chalengedwa. Mukuona? Ndipo kupotoza konse kudzatero, kupotoza, kudzathetsedwa. Ndipo imfa ndi chopotozedwa cha moyo; ndipo pamene kupotoka kwachitika, apo sipangakhalenso imfa nkomwe. Ukalamba ndi chizindikiro cha imfa; ndipo pamene ukalamba wachotsedwapo, moyo wabwerapo. Zizindikiro zonse zopotoza ndi china chirichonse chapita. Minga ndi nthula ndi chizindikiro cha tchimo, “dziko lapansi lidzatembereredwa ndi izo,” ndipo izo zathetsedwa.

Matenda amabwera, ndi zimenezo; iwo adzathetsedwa. Imfa idzathetsedwa. Kukhetsa magazi kudzathetsedwa.

²⁹⁰ Palibe chimene chiti chidzakhudze konse kapanga wochita kupanga ameneyo koma chiyero, Owomboledwa. Oh, mai! Eya. Oh, ine ndikungomverera bwino kwambiri. Mulungu, ndi chirengedwe Chake; ndipo zolengedwa Zake za chirengedwe ichi zawomboledwa ndi Magazi Ake Omwe. Kuyeretsetedwa ndi njira Yake Yomwe yoyeretsera; njira Yake yophera majeremusi, yophera tchimo!

²⁹¹ Monga ngati chirichonse chiwawulidwa, njira yabwino yowawulira yomwe tinayamba takhalapo nayo ndi moto. Inu mukhoza kutenga chirichonse ndi kuchitsuka icho ndi sopo ndi mankhwala onse awa amene iwo amawakamba, icho chimakhala chosatetezekabe. Koma muchiwotche icho kamodzi!

²⁹² Ndipo pamene Moto woyera wa Mulungu udzawawula dziko lapansi ndi Mankhwala; Iye wamukweza Mkwatibwi Wake, amene akhoza kubwera Kumwamba ndi Iye, pamene izi zikuchitika. Ndipo akudzabwerera pa dziko lapansi kachiwiri, Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano. Nyengo yozizira singapweteke ilo. Chirimwe chotentha sichingapweteke ilo. Zipululu zidzaphuka ngati duwa. Tchimo ndi ochimwa apita.

²⁹³ Mulungu, ndi zolengedwa Zake ndi chirengedwe, akukhala limodzi mu mgwirizano wamngwiro. Monga miyamba ndi dziko lapansi ndi mwamuna ndi mkazi, chomwechonso Khristu ndi Mpingo, ndipo iwo onse akukomana mu dongosolo limodzi lalikulu laulemelero la chiwombolo ndipo akubweretsedwa mu zifuwa za Mulungu kachiwiri. Inu mukuwona zimenezo?

²⁹⁴ Ndipo, mu Dziko Latsopano, muli Mzinda Watsopano. Oh, mai! Tsopano mvetserani mwatcheru. Musaiwale izi. Kuti, Yesu anati, mu Yohane 14, Iye adzapita kukakonzekera. “Mitima yanu isavutike.” Pamene Iye akupita, “Ndiri ndi chifukwa choti ndichokepo. Inu mwakhulupirira mwa Mulungu,” Iye anati, “khulupiriraninso mwa Ine.” Iwo sankakhoza kuwona kuti Iye anali Mulungu. Anati, “Inu mwakhulupirira mwa Mulungu, tsopano mukhulupirire mwa Ine. Ndipo Ine ndikupita kukakonzekera inu Malo. Mu nyumba ya Atate Anga muli nyumba zazikulu zambiri; mu Ufumu wa Atate Anga muli nyumba zachifumu zambiri.” Khristu ali kumeneko, pansu pa kumanga kwa Yerusalemu Watsopano uyu tsopano. Tsopano mvetserani mwatcheru. Musati musunthe. Musatero, musachiphonye ichi. Khristu ali Kumwamba, lero, akukonza Yerusalemu Watsopano.

²⁹⁵ Chimodzimodzi monga Mulungu analenga dziko lapansi mmasiku sikisi, analipanga dziko lapansi m’masiku sikisi, kapena zaka sikisi sauzande. Monga iye anati, “Musakhale osadziwa,” ife timawerenga m’Malemba, “zaka wani sauzande ndi tsiku limodzi.”

296 Ndipo Khristu anapita ndipo akukonza Malo, iwo akhala akumangidwa kwa zambiri, zaka masauzande ambiri, kukonzekera Malo. “Ndipo ngati Ine ndikupita kukakukonzerani Malo, Ine ndidzabweranso, ndipo ndidzakulandirani inu; kuti kumene Ine ndiriko, kumeneko inunso mudzakakhalenso.” Zindikirani Muwomboli ndi Wowomboledwa!

297 Ndikanakonda tikanakhala ndi nthawi tsopano. Ndalembe apa, Solomoni akumufunsira, “mtsikana uyu, Mkwatibwi.” Oh, ife tikungoyenera kuzilumpho zimenezo; nthawi ikutha kwambiri, mwaona. Ndidzazitenganso zimenezo, kachiwiri. “Pamene iye akuyesera kumutenga iye, koma iye watomeredwa ndi mnyamata wolishya.” Ena mwina ankaganiza kuti imeneyo inali nyimbo imene iye anayimba. Oh, ayi. Solomoni anali wolandira mpando wachifumu wa Davide, pa dziko lapansi, koma zinasonyeza kuti ufumu umenewo unkayenera kutha. Icho chinali choyimira cha Khristu mu chikondi ndi Mkwatibwi. Mukuona?

298 Zindikirani kuti Yesu anati, Yohane 14 tsopano, “ndikupita kukakukonzerani Malo.”

299 Oh, izo zidzawoneka motani? Kodi inu munayamba mwaganizapo tsopano, Mkwatibwi, momwe izo ziti zidzawonekere? Iwo unakonzedwa ndi kupangidwa ndi Womanga Waumulungu. Kodi Mzinda umenewo uzidzawoneka motani? Tsopano, ife tikamba za izo kwa maminiti angapo. Womanga Waumulungu wawukonza iwo, wawujambula iwo. Ndipo, taonani, Iye wawujambula iwo ndi manja achifundo, chifukwa cha Mkwatibwi Wake wokonedwa. Kodi iwo uzidzawoneka motani?

300 Kodi mungalingalire mwamuna kukwatira mkazi, amene ndi wozitsata, momwe iye amamangira ndi kuyika kanthu kakang’ono kalikonse chimodzimidzi basi momwe iye amafunira, basi zomwe iye angafune? Ameni.

301 Tsopano, Womanga Wauzimu wakonza Mzinda Watsopano, kumene Iye ati adzakakhale ndi Mkwatibwi Wake, basi momwe Iye akufunira. Nzosadabwitsa mtumwiyo anati, “Diso silinawone, khutu silinamve, kapena sizinalowe konse mu mtima mwa munthu.” Tiyeni tiwone ngati tingathe kufufuza mmenemo kwa mphindi, tiwone momwe izo ziti zidzawonekere.

302 Womanga Waumulungu anamupangira izi Wokonedwa Wake. Mukuona? Oh, iwo akuyenera kukhala malo otani, pamene, Chirengedwe Chauzimu, Womanga Wauzimu wapangira izo chikhumbo Chauzimu chimene chinakonzedweratu Mwauzimu ndi Mulungu Wauzimu Amene—Amene ali Mwini wa Moyo Waumulungu! Kodi Mzinda umenewo udzawoneka bwanji! Taganizani za izo.

303 Kumbukirani, si Kumwamba. Yohane anati, “Ine ndinawuwona iwo ukutsika kuchokera Kumwamba.” Iwo ndi woti udzakhala padziko lapansi. Mukuona?

304 Sikuti dziko ili lidzapita; ndi dziko lowomboledwa. Mulungu sananene kuti azadzutsa kam’badwo katsopano; Iye adzawombola ilo limene liripo pano. Iye sikuti adzadzutsa m’badwo watsopano; Iye akuwombola ilo limene ali kale kuno. Iye sadzapanga dziko latsopano; ndi ili pomwe pano. Iye azangongoliwotcha ilo, kuliyeretsa ilo, monga Iye anakuchitirani inu. Zolinga zake zikuyenera kukhalapo mpaka kalekale. Tsopano, penyani, izo zidzakhala ziripo.

305 Kumbukirani, sikudzakhala Kumwamba. “Iwo ukutsika kuchokera Kumwamba.” Ndi Malo okhalapo, Malo okhalamo, kuti Iye azikhalamo. Monga, anali Yohane, pa chisumbu cha Patmo, apa mu Chivumbulutso 21, iye anawuwona iwo “ukutsika.” Yohane anawuwona Mzindawo, “ukutsika kuchokera Kumwamba,” monga nkunda, monga iye anawonera.

306 Apa pakubwera Mulungu, pansu pa kachisi Wake wa padziko lapansi, Yesu, mu. . . “ukutsika kuchokera Kumwamba.” Yesu amabatizidwa, anapita molunjika. . .

307 Pamene Iye anakomana ndi mneneri! “Mawu amadza kwa mneneri.” Ndipo Iye anali Mawu. Ndipo mneneri anali atayima pamenepo, akukana chipembedzo chawo chonse, chirichonse. Ndipo, pamene iye anawawona Mawu, Mawu anabwera kumene kwa iye.

308 Ndipo mneneriyo anadabwitsidwa kwambiri, iye anati, “Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi Inu. Chifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

309 Iye anati, “Balola kuti zikhale chomwecho, pakuti nkoyenera kwa ife (ife tikuwudziwa uthenga) kukwaniritsa chirungamo chonse. Ine ndi Nsembe; Iyo ikuyenera kutsukidwa.” Iye anamulolera iye.

310 Pamene Iye anatuluka mmadzi, iye anati, “Ndinawona miyamba itatseguka.” Mneneri anaziwona izo. Iye anawona miyamba itatseguka.

311 Ndipo apa pakubwera, kutsika kuchokera Kumwamba, mawonekedwe a Nkhunda; ndi Liwu, likuti, “Ili ndi gawo Langa la dziko lapansi limene ndaliwombola, ndipo kuchokera ku gawo ili la dziko lapansi Ine ndidzawombola lina lonse la ilo, pakuti Iye ndi Mawu Anga akuwonetseredwa.” “Ndipo dziko lonse, Ine ndinaliyankhula ilo kuti likhalepo mwa Mawu Anga,” Ahebri 11. “Ndipo Satana waligwirizira ilo nthawi yonseyi, koma Ine ndabwera kuti ndidzaliwombole ilo. Zochulukana za izo zapanga thupi Lake, ndipo Ine ndikubwera kudzakhala mmenemo.”

³¹² Yohane anati, “Ine ndinawona Mzinda woyera, Yerusalemu Watsopano ukutsika kuchokera Kumwamba, monga Mkwatibwi wokongoletsedwera Mwamuna wake.” Ndipo iwo unadzakhazikika pati? Ndendende basi monga izo zinachitira pamenepo; pa dziko lapansi.

³¹³ Yesu anali gawo la dziko lapansi limenelo limene Mzimu Woyera unadzatsikirapo, (nkulondola uko?) ndipo nkudzakhazikika pa Iye kwanthawizonse. Iwo sungakhoze konse kumusiya Iye. Iwo umakhala pamenepo nthawizonse. Iye ndi Mulungu ali Mmodzi. Nthawizonse ayenera kumakhalapo!

³¹⁴ Ndipo chotero Yohane anawona Mzinda woyera, Yerusalemu Watsopano, ukutsika ngati nyenyezi, kapena a—nkhunda, ukutsika pansu kuchokera Kumwamba ndi kudzakhazikika pa wowomboledwa, dziko lonse lapansi, (kudzachita chiyani?) kudzatenga chikhumbo chirichonse chimene Iye anachipangira dziko lapansi. Mwamuna aliyense amene anaimiridwa mu Muyaya, ndi mkazi aliyense, wawomboledwa zikatero. Iye wakwechedwa ndi kuwotchedwa ndi Moto.

³¹⁵ Yesu, mu mayesero Ake amoto mchipululu, kwa masiku forte. Zitachitika zimenezo, zindikirani, izo zinali zitakonzekera utumiki Wake pamenepo.

³¹⁶ Taganizani za zimenezo, Mzimu Woyera ukutsikira pa dziko lapansi, Yesu, ndi Magazi oyera amenewo! Tsopano penyani, ndipo ine ndikuyembekeza ine sindikupita mwakuya kwambiri kwa inu, mwaona. Magazi oyera amene analengedwa ndi Mulungu; Magazi, Moyo, chirengedwe cha Mulungu. “Yesu anali chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu.” Oh! Inu mukuwona zimenezo? Mulungu, anapangidwa mu chirengedwe. Iye anali Mzimu. Baibulo linati, “Iye ndi chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu.” Kodi Iye anayamba bwanji? Mmimba mwa mkazi. Chimene chiri chiyani? Mkaziyo si . . .

³¹⁷ Monga momwe anthu akhungu amenewo sangawone “mbewu” ya serpenti pomwe pano. Mukuona? Eva anayikidwa kuno pa dziko lapansi, ndipo, Satana asanamukhudze konse iye, kapena china chirichonse, Mulungu anati kwa iwo, “Muchulukane ndipo mulidzadzitse dziko lapansi.” Uko nkulondola, koma Satana akubwera apa. Ndipo, ngati uyo anali mwana wa Adamu, ndiye kumene. . .

³¹⁸ Adamu anali mbadwa yolunjika yochokera kwa Mulungu. Ndipo iwe umangotenga chikhalidwe cha kholo lako.

³¹⁹ Ndipo pamene ubadwa mwatsopano, iwe umatenga Chikhalidwe cha Kholo lako, wa Kumwamba. Ndipo Kholo lanu la Kumwamba ndi chikhumbo cha Mawu . . . Kapena, Mawu ndi chikhumbo cha Kholo lanu. Ndiye, inu mungawakane bwanji Iwo, chifukwa cha chipembedzo? Oh, mai!

Ine ndikuyembekezera kuti simuziphonya izi. Ndikudziwa kuti izo zikuchokera kwa Mulungu.

320 Yesu. Apa Iye akubwera, akutsika; ndipo apo panali Yesu, chikhumbo cha Mulungu.

321 Tsopano, “mkazi,” iye. Penyani. Mulungu anati, “Chifukwa iwo achita ichi,” anati, “Ien ndidzayika udani pakati pa Mbewu yako ndi mbewu ya serpenti.” Nkulondola uko? Ndipo mkazi samakhala ndi mbewu iliyonse. Kodi inu munayamba mwaganizapo za izo? Iye ali ndi munda, osati mbewu. Mwaona, serpenti anali atayika kale “mbewu” yake pamenepo.

322 Ndiye, ngati mkazi alibe mbewu, iye akuyenera kukhala kuti akhale ndi Mbewu.

323 Inu mwaona, kudzera mu kugonana apa, anali atabweretsa kuchokera kwa Satana, serpenti, amene sanali chokwawa; anali ndi miyendo, chifukwa miyendo yake inachoka pa iye. Iye anali wothyathyalika kwambiri, chirombo chokhacho chimene chinkatha—chinkatha kulumikizana ndi mkaziyo.

324 Mbewu ya chirombo siingachite zimenezo pano, ndi china chirichonse. Iwo anayeserapo zimenezo. Izo sizingagwire ntchito. Mwaona, moyo wa mbewu kuchokera mwa mwamuna sungapite mwa wamkazi. Izo sizingachite izo.

325 Koma icho chinali chinthu chapafupi kwambiri. Mwaona, iwo amalephera kupeza mtundu umenewo pakati pa chimpanzi ndi munthu. Mwaona, chirichonse, pamene icho chasinthika, kuchokera ku mbalame, ndi kupitirira mpaka kwa anyani, ndi zina zotero, mpaka kwa chimpanzi, kenako pali “otayika.” Imeneyo inali serpenti, osati njoka; mawonekedwe aliwonse anatayika kwa iye, chifukwa iye anatembereredwa.

326 Tsopano, Mulungu sanamutemberere Adamu; iye mwinamwake anachita chinthu chomwecho, koma Iye anatemberera dziko lapansi, “minga ndi nthula.”

327 Iye sanamutemberere Eva, koma anati Adamu adzakhala “womulamulira” wake. Kuyambira tsopano mpakana, iye sakuyesera kulalikira kulikonse kapena chirichonse, Adamu ndi womulamulira wake. “Ndipo masiku onse a moyo wako, ndipo mu chisoni, ndipo iwe udzabweretsa wako. . . moyo padziko lapansi.” Koma Iye anati, “Ndidzayika udani pakati pa Mbewu yako. . .”

328 Tsopano, iye analibe mbewu iliyonse, iye sanakhale nayo konse, kotero, iye ankayenera kuti alandire Mbewu kuchokera mwanjira yina. Mulungu anamupatsa iye Mbewu, osati mwa kugonana, koma mwa chirengedwe.

329 Kodi inu anthu akhungu simungawone kuti imeneyo ndi “mbewu” ya serpenti? Oh, mai! Satana anafika kumeneko Adamu asanafikeko; imeneyo inali “mbewu.”

330 Koma iye analandira Mbewu. Icho chinali chiyani? Mulungu Mwiniwake. “Iye anali chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu.”

331 Tsopano penyani pamene Seti anabadwa, kapena Abele, iye anali mwamuna wolungama, kuchokera kwa abambo ake. Seti ali mwanjira yomweyo.

332 Kodi munthu woyipa uja anachokera kuti; wakupha, wabodza? Mukuona, mukuona kumene izo zinachokera? Iyo inkayenera kukhala “mbewu,” chifukwa iye anali mbewu; Kaini anali munthu.

333 Oh, ali kuti anthu akhungu aja? “Mulungu wa dziko lino wawachititsa iwo khungu.” Chabwino, nzosadabwitsa, Yesu anati palibe munthu angathe kuwona izo. Inu mukuona?

Inu mukuti, “Chifukwa chiyani iwo sakuwona izo?”

334 Yesu ananena nthawi ina, kwa wophunzira Wake, “Kwapatsidwa kwa inu kuti mudziwe Ufumu wa Mulungu, koma osati kwa iwo.”

335 Ndipo ndi chifukwa chimene inu mumachokera ku mailosi fifitini handiredi mbali zonse, mwaona, “Zapatsidwa kwa inu kuti mudziwe Ufumu.” Penyani, anthu amabwera ngakhale kuchokera ku South Africa ndi kozungulira, ora lakumapeto lino pamene Mkwatibwi akupangidwa kuti apite mu Ufumu.

Ine ndiribe nthawi yokwanira. Zindikirani. Penyani tsopano, mwaona.

336 Tsopano inu mukhoza kuwona “mbewu” ya serpenti pamenepo, mukuona momwe iye anachitira izo? Ndi zangwiwo, mwaona. Tsopano ena a iwo anati . . .

337 Tsopano, monga munthu uja ku Tucson tsiku lina, akuyesera . . . Ah, iye akhoza kudzamvetsera tepi iyi. Koma, ngati izo ziri, bamboyo, ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinachake.

338 Pamene iye anati, “Eva anati,” apa ndi pamene iwo amapitako, “Ine ndalandira mwana wamwamuna kuchokera kwa Ambuye, kapena mwamuna kuchokera kwa Ambuye.” Bwanji, ndithudi. Mulungu ali ndi lamulo.

339 Penyani, inu mudzatenge mbewu ndi kudzaibzala iyo kunjika kuno mmunda momwe muli tirigu, ndipo inu nkubzala nansongole kunjika uko. Ine sindikusamala, dzuwa lomwelo ndi mvula yomweyo zimabweretsa mbewu imeneyo ku moyo. Mulungu ali ndi lamulo, ndipo lamulo limenelo silingasweke.

340 Ine sindikusamala ngati a—ngati a . . . mkazi wopanda makhalidwe kwambiri mtawuni ndi mwamuna wopanda makhalidwe kwambiri, ndipo osakwatirana ndi chirichonse, amakhoza—kukhala paubwenzi, ndi kumakhala limodzi ndi kubereka mwana; mwana ameneyo ayenera kubwera mwa lamulo la Mulungu, chifukwa palibe njira yina. Ngati simutero, inu mumupanga Satana kukhala mlengi, ndipo kenako iye ndi mulungu. Oh, inu mungakhale wakhungu bwanji! Mwaona, lamulo la Mulungu, ndithudi.

³⁴¹ Ngati munayamba mwakhalapo ndi mwana, ine sindikusamala kaya anali Esau, Yakobo, aliyense yemwe anali, kapena munthu wa mbiri yoyipa aliyense, ngati anali Yudasi, iye ankayenera kubwera mwa Mulungu. Mulungu ali ndi lamulo.

³⁴² Baibulo linati, “Dzuwa limawalira pa olungama ndi osalungama; mvula imagwera pa olungama ndi osa-...” Ahebri mutu wa 6, ndipo ilo limanena kuti, “A—mvula imabwera mowirikiza pa dziko lapansi, kudzalithirira ilo, ndi kulikonzekeretsa ilo ku zomwe zabzalidwa, inu mukudziwa, kuti zikhale moyo; koma minga ndi nthula zimakhala moyo ndi madzi omwewo, kuwala kwa dzuwa komweko.” Pakuti, ndi lamulo la Mulungu, kuti likhwimitse mbewu iliyonse, kuti lipange mbewu iliyonse kumadzibala yokha.

³⁴³ Chotero, iyo inkayenera kubala ya “mbewu” ya serpenti. Ndipo iyo sina—sinamutchingire konse Mulungu; iyo inakwaniritsa dongosolo Lake lathunthu, iyo inamupanga Iye Muwomboli. Wakhungu aliyense akuyenera pafupifupi kuziwona zimenezo, pokhapokha zitabisidwa. “Mulungu wa mdziko” wazibisa izo kwa inu. Ndi zomveka basi monga chirichonse chimene inu mukhoza kuchiwona. Ndi zimenezotu. Ndi imeneyo “mbewu” yanu ya serpenti. Tsopano zindikirani.

Koma, “Yesu anali chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu.”

³⁴⁴ Tsopano kodi mkaziyo amachita chiyani? Pamene, nyongolosi ibwera kuchokera kwa wamwamuna. Tsopano kukana zimenezo? Mkazi samakhala ndi moyo mwa iye, nkomwe. Iye amangokhala ndi dzira laling’ono lokha, limene ndi munda kunjaku kuno.

³⁴⁵ Monga inu munatenga munda ndipo munawulima wonsewo, ndipo—ndipo munawupopera iwo, ndi kupopera majeremusi onse kuwachotsa mmenemo. Ndipo osati—osati ngakhale udzu kapena kanthu kangamere mmenemo; ndiyeno inu nkudzathiranso fetereza kachiwiri, kudzafetsa mbewu ina yabwino mmenemo. Ngati mdani angabwere ndi kudzafesa mbewu ina, lamulo lomwelo la Mulungu lidzachetsa mbewu zonsezo.

³⁴⁶ Chabwino, Mulungu sankalinga kuti izo zidzatero, mwaona. Koma chinachitika ndi chiyani?

³⁴⁷ Mwaona, mbewu yochokera kwa mwamuna imanyamula magari a moyo, amene ali magari. Mmagazi mumakhala moyo. Ndipo ngati inu konse. . . Ine ndinaziwonapo izo, mu kusakaniza ng’ombe ndi zinthu monga izo. M’bale Shakarian ndi ine tinazilondoloza zimenezo, ndi madokotala ndi ena otero, kupenyetsetsa momwe izo zimayendera, azamankhwala. Mukuona? Ndiye apa pakubwera mbewu kuchokera kwa mkazi, amene amakhala mulu wa mazira. Apa pakubwera mbewu yochokera kwa mwamuna, imene ili gulu la majeremusi.

348 *Iyi* ilibe majeremusi pang'ono mmenemo. Iyo ndi chotuluka mwa munthu. Umo ndi momwe iye anabwerera kuno, poyamba pomwe, ndipo iye ndi munda chabe. Apo pali dzira; ilo liri ndi nthaka yachonde ya moyo uwu. Ndipo moyo uwu umasunthira mkati ndi kukwawa. Pali chinsinsi, momwe izo . . .

349 “Mwinamwake,” inu mukuti, “chabwino, oyambawo akakumana. Ena onsewo amafa.” Chabwino, bwanji, ndani amatsimikizira izo? “Chabwino, oyambawo.” Kodi adzakhala amene ali kutsogolo; dzira loyambirira kutsogolo, ndi nyongolosi yoyambira? Ayi, ayi.

350 Ilo likhoza kukhala dzira limodzi; mpaka mmbuyo, kumbuyo, pakati pa mbewu, padzatulukira nyongolosi ndi idzapita kukakomana ndi ilo. Zimasonyeza kuti luntha lina limatsimikizira ngati uyo adzakhale wamutu wofiira, wamutu wakuda; kaya adzakhala wamng'ono, wamkulu; wamwamuna kapena wamkazi. Mukuona? Inu simungathe, inu simungachite china chirichonse cha izo; izo sizingagwire ntchito. Inu mukhoza kuwasakaniza iwo pamodzi, ndi chirichonse, izo sizingapange kusiyana pang'ono. Mulungu amatsimikizira izo. Ndipo pakapita kanthawi, nyongolosi imodzi yaying'onoyo imakwawira mmunda umenewo, dziralo. Imene ili ndi mchira wawung'ono, wonga, pa iyo, ikumazipiringiza mozungulira; nkumathothoka, ndipo pamenepo pamayamba nsana wa mwanayo.

351 Ndiye kodi iye ndi chiyani? Iye alibe mbewu. Iye ali ndi munda woti alandirire mbewuyo. Koteri a . . .

352 Mwaona, mdani anapita. Pamene wofesa wabwino anapita, akufesa Mbewu yabwino; ndipo mdani anabwera kumbuyo kwake, kumadzafesa mbewu yoyipa. “Koma mvula imawagwera pa olungama ndi osalungama; dzuwa.” Zonse zikuyenera kukula.

353 Yesu anati, “Zisiyeni izo zikulire limodzi. Pa tsiku limenelo izo zidzamangidwa mtolo, namsongole.” Ndipo iwo akumanga mtolo tsopano, mmabungwe aakulu; akupita ku mtolo waukulu, World Council of Churches. Ndipo mapeto ake anali chiyani? Ndi kuti adzawotchedwe. Koma njereyo ndi yakuti itengedwere ku nkhekwe. Mukuona? Kumene, ziwiri zonsezo zimakhala moyo ndi chinthu chomwecho, madzi omwewo, mvula yomweyo.

354 Mtengo wa zowawasa, ndiwo—ndiwo mtengo wa lalanje, umabala, umayenera kutero; udzabala pa iwo, ngati iwo unamezanitsinidwa mmenemo, makangaza. Iwo udzabala ndimu. Iwo udzabala mphesa. Mukuona? Koma iwo sadzakhala malalanje, koma izo zikukhalira moyo moyo womwewo umene mtengo wa malalanje ukubala.

355 Zipembedzo zabairidwa mu Mpesa. Chifukwa, ngati iwo amadzinenera “Akhristu,” amakhala moyo ndi zimenezo. Kayafa anali; inu mukudziwa chimene iye anali, ndipo komabe

iye mpaka ananenera. Mukuona? Mwaona, iwo amakhala moyo ndi zimenezo.

³⁵⁶ Oh, ndikukhumba tikanakhala ndi sabata, kuti ife tidzangophunzira chinthu ichi, ndi kuchifotokoza icho momveka bwino inu—inu nkusaphonya kuchiwona icho. Tsopano ndisiya zina mwa zinthu izi.

³⁵⁷ Tsopano penyani. Taonani, manja amenewo anakonzera izi Mkwatibwi Wake Wokonedwa, amapangira mu chikondi chachifundo kwa Mkwatibwi Wake.

³⁵⁸ Mukumbukire kuti Mzimu Woyera unatsikira pa Yesu, chimene, Yesu anali gawo la dziko lapansi. Chifukwa chiyani? Nyongolosi ya Mulungu, Moyo wa Mulungu, inapangidwa mu chiberekero cha mkazi (kulondola uko?), chimene chinali dziko lapansi. Chabwino. Ndipo kenako Moyo wa Mulungu unadzabweramo, chotero, “Iye anali chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu.” Mukuona? Ndipo kenako Magazi a Mulungu amenewo, amene anali pamenepo mwa nyongolosi imeneyo; pamene iwo anakhetsedwa pa Kalvare, anagweranso pa dziko lapansi. A chiyani? Kuti adzaliwombole dziko lapansi. Tsopano, ilo lalungamitsidwa; layeretsedwa; laitanidwa, ndipo ladzatengedwa; ndipo tsopano ilo ndi loti lilandire ubatizo wake wa Moto, ndi kuyeretsedwera kwa Yesu ndi Mkwatibwi Wake.

³⁵⁹ Ndipo inu ndi magawo ena awa amene anatuluka kuchokera pa dziko lapansi. Dziko lapansi, ndinu gawo la dziko lapansi; thupi lanu. Solo yanu ndi gawo la Mulungu, chikhumbo cha Mulungu, mukuwonetseredwa pano pa dziko lapansi mu thupi. Thupilo ndi loti lidzawomboledwe.

³⁶⁰ Tsopano, moyo wawomboledwa, chifukwa iwo unali mu tchimo. Chotero Mulungu anadzatsika pansu, mwa dongosolo la kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo anadzawombola moyo wanu.

³⁶¹ Ndipo inu, pokhala gawo la dziko lapansi, ilo linawomboledwa ndi ilo. Inu muli mu zochitikazo tsopano. Ilo likukula. Thupi lanu linalungamitsidwa pansu pa ubatizo wa Nowa. Ameni! Ndipo, mnofu wanu, pamene Iwo unadzagwera pamenepo. Ndipo dziko lapansi likuyenera kuyeretsedwa ndi Moto, malo amene inu mudzakhalemo, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera; Malo okhalamo a Khristu ndi Mkwatibwi Wake, Yerusalemu Watsopano.

³⁶² Penyani Mzinda uwu; dziko lapansi, ukutenga kukhala kwake padziko lapansi. Tsopano mukhoza kuwona momveka bwino monga ndinanenera, a . . . kusintha uku, dziko lapansi likuyenera kusinthidwa. Ilo silingakhale ndi Iwo monga chonchi. Mpingo sukanapita . . . Kapena, dziko silikanapitirirabe, zitatha Zakachikwi, popanda kusinthidwa. Mukuona? Kuti likhale ndi Malo oterowo mmenemo, Ilo likuyenera kusinthidwa.

363 Chimodzimidzi monga momwe, ife tikuyenera kusinthidwa ndi Moto Wake woyera, kuti tikonzedwe ndi kupangidwa kukhala malo akuti Iye adzakhazikidwe mwa ife; zimenezo ndi, Mzimu Woyera.

364 Zindikirani tsopano, mudzakhala malo ochuluka mu Dziko Latsopano. Uh-huh. Mwaona, malo ochuluka! Ilo lidzakonedwa, ndizo zoono, ndi Moto, koma sipadzakhalanso nyanja. Zindikirani, Mzindawo ndi mailosi fifitini handiredi mbali zonse zonse.

365 Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni pamene tikujambula miyeso iyi. Ine ndikufuna kufufuta pa bolodi, mphindi chabe.

366 Apa pali vumbulutso lakuya lochokera kwa Mulungu. Apa, ine ndingoimikira apa. Palibe mwa ena awa...Ine ndizibweretsa zina zonse izi, Ambuye akalola.

367 Zindikirani tsopano dziko lapansi liri...Chabwino, inu mutsegule ku Bukhu la Chivumbulutso, mutha kuwona momwe iye anayeza ilo ndi mikono ndi mastadiya. Twente-firii handiredede...Chotero tsopano ife tikupeza kuti—Mzindawu unayezedwa, “mailosi fifitini handiredede” mbali zonse zonse.

368 Inu mukudziwa kuti zimenezo ndi kufika mpaka kuti? Ine ndinayeza izo, sabata ino. Izo zikhoza kufika kuchokera ku Maine kupita ku Florida, ndi kuchokera kunyanja yakum'mawa kupita mtunda wa mailosi sikisi handiredede, kumadzulo kwa Mississippi. Mwa kuyankhula kwina, theka la United States, kwa Mzinda wokha.

Inu mukuti, “Mulibemo malo.”

369 Pamene nyanjayo ikadzachotsedw adzakhalamo, chifukwa pafupifupi magawo foro pa asanu a iwo ali mmadzi. Nkulondola uko? Kuphulikako kudzaumitsa nyanja, kuphulitsa dziko lapansi. Oh, mai! Kumbukirani, mailosi fifitini handiredi mbali zonse zonse, ndi Mzinda wotani! Ndipo, koma, kumbukirani, nyanja yapita.

370 “Ndipo kutambalala ndi kutalika ndi mofanana.” Izo zikuwupanga iwo mailosi fifitini handiredi mbali *iyi*, mailosi fifitini handiredi mbali *iyi*; mailosi fifitini handiredede; utali ndi kutambalala chimodzimidzi ndi usinkhu. Mailosi fifitini handiredi, taganizani za izo, golide wowonekera. Ndipo Mzindawo unali ndi khoma mozungulira iwo.

371 Tsopano, tsopano, izo sizikutanthauza kwenikweni, pokhala mofanana...Ilo linati, “Ndipo makoma ndi maziko anali ofanana,” izo sizikutanthauza kwenikweni kuti ndi kabokosi kapena mphwamphwa. Pali muyeso wina wa malo, wakuti miyeso yake imakhala yofanana, ndiko kuti, piramidi. Mbali foro zofanana, “pali mbali foro zofanana,” ndipo makomawo anali ofanana.

372 Ndiroleni ndijambule zimenezo. Onani: mulitali, kutambalala, usinkhu. Ife tilowa mu chinachake, motsimikiza basi monga dziko. Mukuona? Zindikirani, miyeso ya ngodya *iyi* ndi yofanana ndendende, yonseyo, mulitali ndi—ndi usinkhu. Pali muyeso wina, piramidi, umene umatsimikizira zimenezo.

373 Izi, pokhala mwanjira *iyi*, zingayankhe ndendende chizindikiro cha Enoki mu Igupto, piramidi. Izo zingatero? Enoki, chiwonongeko cha chigumula chisanachitike, pamene kulungamitsidwa kunkabwera umo, iye anabweretsa chizindikiro, ndipo mu piramidi *iyi* muli masitepe seveni opita kuchipinda cha mfumu. Muyang'ane pa sitepe yachiseveni, ngati munaphunzirapo miyeso ya piramidi, chimene chimatuluka kudzatenga wakudzayo, kuti amudziwitse kwa mfumu. Penyani ndi malo a ndani amene akuyima pamenepo, ndipo inu mudzawona tsiku limene inu mukukhalamo, mu piramidi.

374 Tsopano, Mulungu anapanga Mabaibulo atatu. Tsopano, pali chiphunzitso cha piramidi chimene chiri zamkutu, koma pali piramidi yeniyeni. Mukuona? Zindikirani. Tsopano, Mulungu, Baibulo loyamba . . . Iye anapanga atatu. Pakuyenera kukhala chirichonse mu zitatu.

375 Yesu akubwera katatu. Anabwera, kamodzi, kuti adzamuwombole Mkwatibwi Wake; nthawi yotsatira, kuti adzamtenge Mkwatibwi Wake; nthawi yotsatira, ali ndi Mkwatibwi Wake. Mukuona?

376 Tsopano zindikirani kukongola kwake. Mukuona? Ndipo mu piramidi *iyi* munali masitepe seveni, ndipo kenako chipinda cha mfumu. Ndipo ife tiri mu m'badwo wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri, Mfumu isanatenge Mpandowachifumu Wake. Ndipo, kumbukirani, piramidi inalibe konse mwala wapamutu pa iyo.

377 Baibulo loyamba la Mulungu linali mu mlengalenga, Zodiaki; ilo limayamba ndi kuyenda m'badwo uliwonse. Choyamba, poyambira pa Zodiaki, ndi namwali; umo ndi momwe Iye anabwerera, poyamba. Chithunzi chomalizira mu Zodiaki ndi Leo mkango; Kudza kwachiwiri. Basi pasanakhale nsomba zopingasa, umene uli m'badwo wa khansa; umene ife tikukhalamo tsopano.

378 Panali piramidi pambuyo pake, Enoki, amene anachitira umboni ndendende. Ife sitikanakhala ndi nthawi yoti tilowe mu zimenezo, koma, tsiku lina, mwa thandizo la Mulungu, ine ndidzakuwonetsani inu, ndendende basi imakoka gawo la ora limene ife tikukhalamo. Mukuona?

379 Zindikirani, koma muyeso wa malo uwu umene ife tiri nawo tsopano, umene miyeso yake ndi yofanana, sizikutanthauza kwenikweni kuti iwo akuyenera kukhala a—a kabokosi. Zindikirani, izi zingayankhe cha Igupto . . . kapena chizindikiro cha Enoki ku Igupto.

380 Mu nthawi ya kuyeretsewa kwa dziko lapansi, mwa ubatizo wake wa Moto, padzakhala chiphala chamoto, monga ngati dziko lino kuphulika, ndipo lidzakankhira mmwamba Phiri ngati piramidi. Mukuona? Malo ambiri oti adzachite zimenezo! Chinthu chonsechi chidzasinthidwa. Malo onse adzasinthidwa. Inu mwamvetsa zimenezo? Iwo adzakankhira mmwamba Phiri longa piramidi.

381 Izi zidzakhala ndendende ndi Mawu ngati izo zidzachite zimenezo, chimene izo zidzatero. Tsopano zindikirani, pakuti, mu Yesaya 65:25, pamene ife tangowerenga kumene, Iye anati.

Iwo sadzavulaza kapena kuwononga mu phiri langa lonse loyera, atero AMBUYE.

382 Oh! “Phiri Langa lonse loyera!” Kumbukirani, nthawizonse zimakhala “Phiri.”

383 Ngati makomawo anali olunjika mmwamba-ndi-pansi, Mzindawo ukanangowoneka kuchokera kunja kokha. . . kapena kuchokera mkati, Mpandowachifumu ukhoza kungowonedwa kuchokera mkati; koma zindikirani iwo ukhoza kungowonedwa kuchokera mkati mokha.

Koma tsopano tikuwona lonjezo la pa Yesaya 4:5. Tiyeni tingowerenga izo.

384 Kodi muli pa changu? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Ayi, musakhale pachangu tsopano. Ife—ife—ife tiri ku—ku chinthu chapadera tsopano, mochuluka kwambiri—mochuluka kwambiri za—nthawi imene inu mukuyenera kumvetsetsa pomwe pano. Chifukwa, ine ndikufuna kuti ndifotokoze izi momveka. Ndipo kenako tikadzabwerera kwa izo kachiwiri, ine ndi—ine ndikuwonetsani inu ndiye pamene ife tiri—pamene tikukambapo, chiyani, mu phunziro lathu lotsatira pa izi, nthawi ina.

385 Oh, Ambuye Yesu alemekezeke! Penyani apa, momwe Mawu sangathe kulephera. Tsopano penyani apa mu Yesaya. Ine ndazilemba izo apa, ngati ine ndingazipeze izo kachiwiri, miniti yokha. Yesaya 4:5. Tsopano mvetserani, iye akuyankhula za Kudza kwa Ambuye, momwe akazi akanati adzakhale amakhalidwe oyipa kwambiri. Oh, iye anati, “Akazi seveni. . .” Mvetserani. Tiyeni tingowerenga zimenezo. Yang’anani apa.

Ndipo mu tsiku limenelo akazi seveni adzangwira mwamuna mmodzi, akuti, Ife tidzidya chakudya chathu chathu, . . . tizivala zovala zathu: mungotilola ife tidzitchulidwa dzina lanu lokha, kuti tichotse chitonzo chathu.

386 Imeneyo ndi nthawi yakumapeto, imene ife tikukhalamo tsopano; ukwati, chilekano, ndi uhule, ndi chirichonse.

Mu tsiku limenelo nthambi ya AMBUYE idzakhala yokongola ndi yaulemelo, . . . chipatso cha nthaka

chidzakhala chabwino ndi chokongola . . . iwo amene . . . anathawa Israeli. (Momwe inu munathawira chiwonongeko chonsecho! Mukuona?)

Ndipo padzachitika, kuti iye amene watsala mu Zioni, ndi iye amene ali wotsalira mu Yerusalemu, adza . . . (Tiyeni tiwone.) . . . mu Yerusalemu adzatchedwa woyera, ngakhale aliyense wolembedwa mwa amoyo mu Yerusalemu, mwaona:

Momwe Ambuye adzakhala atatsuka zonyansa za mwana wamkazi wa Ziyoni, (kumbukirani, ameneyo nthawizonse ndi Mkwatibwi, mwaona) . . . ndipo adzakhala atayeretsa magazi a Yerusalemu (amenewo ndi otsalira a Ayuda, kuphatikiza Mkwatibwi, mwaona) . . . ndipo pakati pake ndi mzimu wa chiweruzo, moto . . .

³⁸⁷ Icho nthawizonse ndi chiweruzo cha Mulungu, pamene Iye akupanga chiweruzo Chake chotsiriza. Amakuitanani inu, amadzakulungamitsani inu, ndipo nkukubweretsani inu ku chiwombolo; kenako chiweruzo Chake chimadzagwera pa inu, ndipo Mzimu Woyera ndi Moto zimadzatsuka tchimolo. Zikatero ndinu Wake.

³⁸⁸ Chinthu chomwecho iye amachita pa dziko lapansi, pamene iye akuliyeretsa ilo ndi Moto, “ndi mwa mzimu woyaka.” Tsopano yang’anani. Mvetserani! Kodi mwakonzeka?

Ndipo AMBUYE adzalenga pa malo onse okhalapo pa phiri la Ziyoni, ndi pa osonkhana ake, mtambo wa utsi masana, ndi kuwala kwa . . . moto usiku: pakuti pa ulemelero wonse padzakhala chitetezero.

³⁸⁹ [M’bale Branham akuwonetsera pa bolodi—Mkonzi]. “Ambuye, mu tsiku limenelo, pamwamba pake, adzalenga Moto wa Kuwala kuti udzayake pa sikulo.” Ndipo ikupitirira ndikuti, “Udzakhala potchingika, mpumulo, pothawirapo.” Zindikirani, kupanga ndendende kuyankhula kwa Baibulo, ndendende. Makomawo anali oyima molunjika mmwamba-ndi-pansi, inu simukanakhoza kuwuwona iwo. Iwo ayenera kutsamira. “Mapiri Anga Onse oyera . . .” “Iye adzalenga Kuwala uku pa Phiri ili, ndipo ilo lidzakhala la chitetezero.” Oh, ife timayimba nyimbo ija:

Oh, Mzinda umenewo pa Phiri la Ziyoni,
Monga mwendamnjira, komabe ine
ndikuzikonda izo apobe;
Tsopano ndipo kupyola mibadwo imeneyo,
Pamene ndidzafika ku Mzinda pa Phiri.
(Mukuona?)

³⁹⁰ Zindikirani, Phiri la Sinai linali pamene Mulungu anatsikira pamwamba pake, pamene Iye ankayankhula kwa Israeli mu Lawi la Moto. Iye anatsikira pamwamba pa Phiri la Sinai.

³⁹¹ Pa Phiri la Chiwalitsiro, pamene Iye anadzalengeza, “Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa; mvereni inu Iye,” Iye anatsikira mu Lawi la Kuwala ndi kuwala kowala, pamwamba pa phiri, pamaso pa Petro, Yakobo, ndi Yohane. Ndipo, pamenepo, Iye anaimiridwa ndi awiri onse Mose ndi Eliya; osandulika, ndipo akufa anawuka. Ulemelero!

³⁹² Mzinda Watsopano ndi Dziko Latsopano; chirengedwe chatsopano; Mzinda pa Phiri, ndi Mpandowachifumu pamwamba pake. [M’bale Branham akujambula zithunzi pa bolodi mu ndime zingapo zotsatirazi—Mkonzi]. Mpandowachifumu pamwamba *apa*, pamwamba; ndi okhalamo, onse chokwera-ndi-chotsika, pa Phiri ili.

³⁹³ Ndipo khoma lozungulira ili, linali ndi maziko thwelofu. Ndipo aliwonse a iwo anali ndi mwala wa pachifuwa umene unali mwa Aroni, umene unkaimira mafuko thwelofu a Israeli.

³⁹⁴ Ndipo, mu zipata, iwo anali ndi zipata foro zoyikidwa chimodzimidzi basi monga kachisi mu chipululu, monga chihema chinali mu chipululu. Zindikirani mmodzi aliyense, anali—anali ndi atumwi, atatu mbali iliyonse, atumwi thwelofu. Aliyense. . . Ndipo iwo unali mikono wani handirede forte foro usinkhu wake. Mikono wani handirede ndi forte foro ndi chimodzimidzi mapazi thuu handirede ndi sikisitini, kupanga uliwonse wa miyala yaikulu imeneyo pafupifupi mapazi twente kutalika, chapachifuwa pa chipata chimenecho, kupanga khoma limenelo limene linali kuzungulira Mzinda.

³⁹⁵ Tsopano iwo, Mzinda, sumakhala pamwamba pa khoma, chifukwa mzinda, mailosi fifitini handiredi, sungakhoze kuchita zimenezo. Ndi khoma *apa* limene mumalowamo, monga zipata za Yerusalemu wakale. Munkalowa kudzera pa khoma, kulowa mmenemo.

³⁹⁶ Ndipo lililonse mwa awa anali ndi maziko thwelofu, ndipo uliwonse unali ndi smargedo ndi miyala yosiyanasiyana, imene inkaimira mafuko thwelofu a Israeli.

³⁹⁷ Ndipo atumwi, aliyense, pa chachikulucho, chipata chimodzi cha ngale-yolimba, anayika dzina la mtumwi. Ndipo kodi Yesu sanati, “Inu mudzakhala pa mipando yachifumu thwelofu, kuweruza mafuko thwelofu a Israeli?” Ndani amakhala pa chipata, kuti aziweruza, pamene iwo ankabwera mu Mzindawo? Oh, mai! Ndi zimenezotu pamenepo. Mafumu a dziko lapansi akulowa mu Mzinda, akubwera pamaso pa woweruza wa atumwi, monga Yesu analonjezera. Oh, mai!

³⁹⁸ Pa Mpandowachifumu uwu, pamwamba pake, kutalika mailosi fifitini handirede, dziko lonse lidzawona Kuwala kwa dzikolo, Yesu, atakhala pa Mpandowachifumu pamwamba pa dziko, pamwamba pa Mpingo, pamwamba pa Phiri la Ziyoni; limene liri mailosi fifitini handirede, theka kukula kwa United

States, ndi kukwera mmwamba mpaka inu mukhoza kumuwona Iye dziko lonse, kutalika mailosi fifitini handiredi.

³⁹⁹ Ndipo onse mmwamba-ndi-pansi *apa*, adzakhala Owomboledwa. Padzakhala nyumba za golide woyengeka bwino. Mudzakhala tinjira, ndi mapaki, ndi minda. Ndipo Mtsinje wa Moyo ukubwera, ukusefukira kuchokera ku Mpandowachifumu, ndipo ukuyenderera kudutsa mu maphompho aang’ono ndipo, oh, kuwoloka mitumbira. Ndipo Mtengo wa Moyo udzakhala ukuphukira mu bwalo lililonse; ndi kumabala zipatso Zake, ka thwelofu pa chaka, chipatso china mwezi uliwonse.

⁴⁰⁰ Ndipo mafumu a mdziko azidzalowamo ndi kumabweretsa ulemelero wawo. “Ndipo masambawo ndi ochiritsira mafuko,” pamene mafumu akukhala mwamtendere kunjira uko. Pamene azidzatuluka, iwo azidzathyola mtengo, tsamba kulithothola monga *choncho*. Monga nkunda inabwerera, kuti mkwiyo wa Mulungu unali utathetsedwa, ndipo inabweretsa tsamba loyera mu chombo. Chotero pamene mfumu izidzanyamuka, izidzabweretsa ulemelero wake mu chipinda cha Mkwatibwi kuno mu Mzinda, iye azidzagwirizira tsamba kwa mfumu yoyandikana nayo, ndipo, “Ife tiri mu mtendere mpaka kalekale.” Amen! Machiritso a mafuko! “Zonse zakhazikika. Nthawi ina ife tinkamenyenirana magazi a wina ndi mzake, m’bale. Ndipo ife tasamalirapo, ndipo timakuwa; ndi kuwombera, ndi kuwotcha ana, chirichonse. Koma tsopano kuli mtendere, machiritso.” Kulibeko kuchiritsa matenda; zonse zachitika. Kuchiritsa kwa fuko! Amen!

⁴⁰¹ Mzinda wokhala ndi Mpandowachifumu pamwamba. Chivumbulutso 21:23, “Ndipo iwo samasowa kuwala, pakuti Mwanawankhosa ndi Ambuye Mulungu ndi Kuwala kwake.” Mukuona? Ambuye Mulungu ndi Lawi la Moto limenelo limene linkawatsatira ana a Israeli kudutsa mchipululu. Ndipo Iye wakwera pamwamba pa Mpandowachifumu, mu Ufumu wangwirowo umenewo. . . pamene nthawi. . . “Ufumu umene Yesu adzawupereke kwa Atate, kuti Mulungu akhale zonse, ndi mwa onse.” Yesu akukhala pa Mpandowachifumu Wake apa, ngati Yosefe wathu. Ndipo Mfumu ndi Kuwala kumeneko kumene kudzakhale pamwamba pa Phiri la Ziyoni, ndipo Kuwala Kwake koyera kudzasefukira pa Mzinda wonse. Aleluya!

⁴⁰² Mailosi fifitini handiredede usinkhu wake, ndi mailosi fifitini handiredede mbali zonse zonse, ndi maparadiso a Mulungu atamangidwa monse kuzungulira Mzinda umenewo; misewu, tinjira! Kawerengeni Chivumbulutso 21 chanu, mukawone ngati izo siziri zolondola. Mukuona, “Iwo sadzasowa kuwala kumeneko, pakuti Mwanawankhosa ndiye Kuwala.” Ndipo pa Mpandowachifumu ukhoza kuwonedwa, atakhala, mailosi fifitini handiredi.

403 Iwo sakuyenda molunjika choima monga *chonchi*. Iwo akupendekeka, ngati piramidi. Ngati zitakhala theka la mtunda, ndiye iwo akhoza kuyenda pafupifupi monga *chonchi*, inu mwaona, kuchokera ku mzinda umodzi kupita kwa wina... tsopano ngati inu mungazindikire, kuchokera ku mbali imodzi ya Mzinda kupita ku ina.

404 Ine ndikhoza kuponyera chinachake chaching'ono apa ngati inu mukufuna kuti ine nditero. Kodi inu munazindikira gulu laling'ono pano? Ndi pafupifupi gawo limenelo, kuzungulira komwe iwo ukuphimba. Georgia, California, ku Saskatchewan; kuchokera ku Kansas, kupita ku gombe la miyala la Maine; ndi kumene kwasonkhanitsidwa. Ndizo pafupifupi zomwe zikuimiridwa apa, pafupifupi mailosi fifitini handirede mbali zonse zonse.

Oh, akuchokera Kummawa ndi Kumadzulo,
 Akuchokera ku dziko lakutali,
 Kudzadya ndi Mfumu yathu; kudzadya...
 (Chiyani? "Munthu sadzakhala moyo ndi
 mkate wokha." Ndi Mkate, Mawu!)...
 kudzadya monga alendo Ake;
 Ndi odala bwanji amwendamnjira awa!

Padziko lapansi, ine ndikuyenera kunena, sindinawawonepo anthu ngati amenewo.

Oh, akuyang'ana nkhope Yake yopatulika
 Yonyezimira ndi Kuwala Kwaumulungu;
 Otenga gawo odalitsika a chisomo Chake,
 Monga ngale mu korona Wake adzawala.
 Oh, Yesu akubwera posachedwa,
 Mavuto athu adzakhala atatha.
 Oh, bwanji ngati Ambuye wathu atabwera
 mphindi ino?

405 Sizikhala motalika. Chirichonse chiri mwangwiro. Mwa malo, Sodomu, amthenga; chirichonse chikukhala chimodzimidzi molondola basi. Mukuona? Izo zikutanthauza chiyani? Tangoganizani, kubwera ku kachisi wina wamng'ono uyu, mailosi fifitini handiredi mbali zonse zonse, kuchokera mu muyeso womwewo.

406 Nchifukwa chiyani Mulungu anaganiza ndi kusamala kwambiri za malo aang'ono amenewo a Palestina, mwaona, pamene iwo angokhala malo aang'ono? Koma kumeneko ndi kumene kachisi akudzaikidwa. Kumeneko ndi kumene Yerusalemu Watsopano adzakhale, kumeneko basi. "Azitona, Phiri la Azitona lidzagawanika, mbali kumanja ndi kumanzere," ndithudi, pamene iwo uzidzakankhira mmwamba kuchokera pansu. Osati, iwo amati, iwo ukukankhira pakati monga *chonchi*. Iwo ukukankhira mmwamba, "Pa tsiku limenelo pamene Iye adzayima mapazi Ake oyera pa Phiri." Zindikirani, pa

Mpandowachifumu Wake, mailosi fifitini handiredi usinkhu wake!

⁴⁰⁷ Kumbukirani, Satana anayesera kuti amuyese Iye, nthawi ina, pamwamba pa phiri. Mukuona?

⁴⁰⁸ Mzinda Watsopano uli ndi maziko thwelofu, monga ife tinadutsamo, mbadwa thwelofu; mikono handiredede ndi forteforo; ndicho chapachifuwa cha Aroni; zipata thwelofu za ngale, dzina la ophunzira thwelofu.

⁴⁰⁹ Yesu wayima, Mwalawapamutu, pa Mpandowachifumu, pamene oyera Ake adzamuveka Iye korona, “Mfumu ya mafumu, Ambuye wa ambuye.” Ndipo Iye ndi Mwalawapamutu.

⁴¹⁰ Ndiribe kachikwama kanga ka mthumba ndi ine. Koma ngati inu mungazindikire mu kachikwama ka mthumba, ngati muli ndi ndalama ya wani dola, iyo ili ndi chisindikizo cha United States; mphungu kumbali imodzi, itagwira mikondo, chizindikiro cha dziko, monga ngati zinali; ndipo kumapeto enawo, iyo ili ndi piramidi, ndi diso lowona zonse pamwamba pake. Mukuona, iwo sankadziwa chimene iwo ankachita. Ndipo pamenepo izo zinalembedwa mu Chilatini, ndipo inu mudzapeza kuti iyo imati, ichi ndi “chisindikizo chachikulu.” Iwo sankadziwa chimene iwo ankachita. Monganso Kayafa sankadziwa kuti anali kunenera.

⁴¹¹ [M'bale Branham akuwonetsera pa bolodi—Mkonzi]. Ndi chimenecho Chisindikizo Chachikulu. Ndi ichi *apa*, mwaona, Mzindawo. Sikabokosi kotambalala chabe monga *chonchi*, mwaona, koma iwo akutsamira mmwamba kuti iwo azikhoza kuwonedwa. Ndipo pa Phiri lopatulika ili la Ambuye, Ambuye adzatsikira pamwamba pa Phiri Lake; ndi Uyu *apa*. Ndi chifukwa chake mwalawapamutu sunavekedwe ndi Enoki. Mukuona? Ndi chifukwa chake Mwalawapamutu ukuyenera kubwera tsopano. Ndipo Phiri lidzakankhidwira mmwamba, ndipo lidzakhala Phiri la Ambuye.

⁴¹² Ndipo mkati *munu* muzidzakhala Owomboledwa. *Izi*, tinjira ndi misewu yayikulu yotakasuka, monga zimakhallira, mapaki, ndi Mtsinje wa Moyo uzidzatenga, uzidzayenda kudutsa mmenemo. Ndipo nyumba iliyonse idzamangidwa ndi golide wowonekera. Ndipo misewu idzapangidwa ndi golide. Ndipo mitengo ya Moyo idzakhala kumeneko, ndipo izidzabala mitundu thwelofu ya zipatso. Ndipo mafumu ndi anthu olemekazeka a padziko lapansi azidzabweretsa ulemu wawo ndi ulemelero mu zipata. Ndipo zipata sizimadzatzekedwa usiku, chifukwa sikudzakhala usiku kumeneko.

Mu Mzinda umenewo mmene
Mwanawankhosa ndiye Kuwala,
Mu Mzindawo mmene usiku sudzafikamo;
Ndiri ndi nyumba kumeneko yopanda
mazunzo komanso chisamaliro,

Oh, ndikupita kumene Mwanawankhosa ndiye
Kuwala.

413 Kodi inu simukuwona kuti matawuni, mizinda, nyumba, zokhalamo, zi—zikuyankhula za izo pakali pano? Zinthu zonse zachirengedwe izi ndi mthunzi.

414 Mutenge mthunzi, uli patali, monga dzanja langa. Pasanakhale a—chabwino...kapena choyipa, pakuyenera kukhala chabwino. Ndipo, inu mwaona, mthunzi umenewo, umawoneka ngati ndiri ndi zala thwelofu, koma ndiye pamene inu mufika pozifikitsa izo pafupi, izo—zimayang'ana mpaka ku chimodzi, ndipo kenako mthunzi umazirala m'manjamo.

415 Ndipo ndizo, nthawi zambiri, anthu amaganiza kuti pali Amulungu atatu kapena foro. Inu mukuyang'ana patali kwambiri mu kukonzanso koyambirira. Mukuona? Tsikani pansi tsopano ndipo, inu mupeza, yang'anani mpaka mutakhala Mmodzi. Ndizo ndendende.

416 Pali Mkwatibwi mmodzi; osati thwelofu, zipembedzo. Koma Mkwatibwi mmodzi, ameneyo ndi Wosankhidwa, mwa aliyense... kuchokera ku—kuchokera ku dziko lapansi amene anakonzedweratu uku, iwo amene angazindikire malo awo mu Ufumu.

417 Pa Mpandowachifumu uwu, tawonani, wautali kwambiri! Mzinda Watsopano; ndi maziko; zipata thwelofu; Yesu, Mwalawapamutu; atumwi, akuweruza; mafuko thwelofu.

418 Piramidi ya Enoki siimapanga mthunzi ngakhale masana. Ndakhalapo mu Igupto, ku mapiramidi. Iyo inakhazikitsidwa mwa jogarafe, ndi mumiyeso ya chithunzi chachikulu cha masamu ichi; mwakuti, ziribe kanthu kumene dzuwa liri, sipamakhala nkomwe mthunzi kuzungulira piramidiyi. Mukuona momwe izo zimakhallira?

419 Ndipo sikudzakhala konse usiku kumeneko. Iye pamwamba pa Phiri, akusefukira pamenepo ndi ulemelero Wake. Kuwala Kwake kwa Ulemelero kudzakhala komweko nthawi zonse. Sikudzakhala usiku kumeneko. Yesu, Mwalawapamutu!

420 Tsopano zindikirani. Chotero, Owomboledwa azidzayenda mu Kuwala. Ife tiyimbe tsopano, "Ife tiyende mu Kuwala, Kuwala kokongola kuja." Pali chinachake mwa ife chikuyitanira momveka. "Wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo." Ndi chifukwa chakuti akuyembekezera. Mukuona? Ndicho chikhumbocho, chimene ife tikumverera.

421 Moonadi, ndi izi...Inu mwakonzeka? Uwu ndi Mzinda umene Abrahamu ankawufunafuna. Mukuona? Pokhala mneneri, iye ankadziwa kuti Mzinda umenewo unali kwinakwake. Baibulo linanena chomwecho. Ndipo iye anasiya mzinda umene iye ankakhalako, ndipo iye anapita uko; taonani kumene iye anapita, ndendende kumene iwo uti udzakakhaleko.

Mukuona? “Iye ankafunafuna Mzinda Umene wowumanga ndi wowupanga anali Mulungu,” mwaona, pokhala mneneri.

⁴²² Yesu anapita kukakonza, ndi manja Auzimu, Mzinda Wauzimu; Womanga Wauzimu, kwa anthu ogulidwa Mwauzimu, kwa anthu okonzedweratu. Iye anapita kukakonzekeka.

⁴²³ Abrahamu ankawufunafuna iwo. “Ndipo anadzinenera kuti iye anali mwendamnjira ndi mlendo, pakuti iye ankafunafuna Mzinda Umene wowumanga ndi wowupanga Wake anali Mulungu.” Mneneri ameneyo, podziwa kuti iwo unali kwinakwake! Yohane anawuwona iwo ukutsika pansi, koma Abrahamu anaganiza kuti iwo ukuyenera kukhala pa dziko lapansi nthawi yomweyo. Bwanji? Iye anakomana ndi Melkizedeki, Mfumu ya iwo, ndipo anamupatsa Iye chakhumi. “Amene analibe bambo, kapena analibe mayi. Iye analibe chiyambi cha moyo kapena mapeto a moyo.” Abrahamu anakomana naye Iye, ndipo iwo anadya mgonero pa malo omwewo amene Mzinda udzamangidwe, Phiri lopatulika la Ambuye, kumene Owomboledwa adzakhaleko. Oh, mai!

⁴²⁴ Nthawi imeneyo musangoima. Ayi, ife tiri mu nthawi; pakapita kanthawi ife tidzapita ku Muyaya.

⁴²⁵ Oh, Phiri loyera! Kudzakhala misewu ya golide woonekera, tinjira; ndi nyumba, ndi mapaki. Ngati mukufuna kuti muwerenge izi, Chivumbulutso 21:18. Mtengo wa Moyo udzakhala kumeneko; zipatso thwelofu zosiyanasiyana, chimodzi mwezi uliwonse, chizidzabalidwa pa iwo. Anthu amene azidzadya zipatso zimenezi, azidzasintha zakudya zawo mwezi uliwonse.

⁴²⁶ Ndipo ndi—ndi kuchokera . . . za ogonjetsa okha. Kodi inu mukudziwa zimenezo? Izo si zazipembedzo.

Inu mukuti, “Inu mukutanthauza zimenezo, M’bale Branham?”

⁴²⁷ Tiyeni titsegule ku Chivumbulutso 2, miniti yokha, ndipo tipeze izo. Chivumbulutso 2:7. Tiyeni tipeze tsopano ngati izo ziri Choonadi kwenikweni kapena ayi. Chivumbulutso 2:7 akuwerengedwa motere.

Ndipo iye amene ali ndi khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu . . .

⁴²⁸ Tsopano, kumbukirani, Iye sakuyankhula kwa Ayuda tsopano. Uwu ndi Mpingo, Wamitundu.

Iye amene ali ndi khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu anena kwa mipingo; Kwa iye amene agonjetsa, ine ndidzampatsa kuti adye za mtengo wa moyo, umene uli pakati pa paradiso wa Mulungu.

⁴²⁹ “Ogonjetsa okha, amene agonjetsa chirombocho, kugonjetsa chiremba chake,” ndicho Chikatolika, Chiprotestanti, chipembedzo, “amene agonjetsa chirombo, chiremba chake,

chirembo cha dzina lake.” “Iye adzakhala ndi ufulu ku Mtengo wa Moyo, kuti akalowe mu zipata momwe palibe chomwe chiri chodetsa chingalowemo.” Mukuona? Taganizani za zimenezo. Tsopano, miniti yokha tsopano, pamene ife tikupita patsogolo pang’ono pokha. Mtengo wa Moyo udzakhala wa ogonjetsa okha.

⁴³⁰ Masamba adzakhala ochiritsira mafuko. Ndiko kuti, mafumu okhala mmenemo, azidzabweretsa ulemu wawo, pamene iwo azidzabweretsa ulemelero wawo ndi kuwuyika iwo pamaso pa Mpando wachifumu wa Mulungu. Monga ngati kunjako, teni. . . mafuko leveni amabweretsedwa, lirilonse la iwo, chakhumi kwa Levi, mwaona. Pamene iwo akubweretsa ulemu wawo mu. . . kuchokera ku dziko lodalitsikalo, mmenemo, iwo adzafikira kuchokera ku Mtengo wa Moyo, kuthyola tsamba lobiriwira. . . kapena tsamba la Mtengo wa Moyo, ndipo iwo azidzatulukira limodzi. Kulibenso nkondo. Chirichonse chiri pa mtendere. Masamba ndi chikumbutso, cha machiritso a fuko.

⁴³¹ Mtengo womwewo, osati monga Adamu, iye. . . Munali Mtengo wa Moyo mmunda wa Edeni, umene iye akanamadyamo ngati iye akanapanda kugwa. Mtengo wa Moyo umenewo umamukumbutsa iye, nthawi zonse, kuti chatsopano chake. . . chinyamata chake chimapitirirabe. Mukuona?

⁴³² Chomwechonso adzatero mafuko. Masamba adzakhala ochiritsira mafuko; zindikirani, osati matenda tsopano. Inu mudzakhala nawo maufulu omwewo amene Adamu anali nawo, monga le- . . . nkhunda ndi tsamba lobiriwira, ndizo zonse. . . mfumu iliyonse ikutenga tsamba.

⁴³³ Zindikirani, Mtsinje wa Moyo, mwina timitsinje tating’ono tambiri tikuupanga iwo. Tsopano, mdziko ili. . .

⁴³⁴ Ine nditseka mu maminiti pang’ono chabe. Mu dziko lino. . . Kapena, ine ndingoyima. *Umo* ndi momwe ndiriri ndi zolemba zochuluka, tsopano pafupifupi masamba sarte. Eya. Penyani.

⁴³⁵ Mu uwu—m’moyo uno, sindinawonepo kanthu koziziritsa monga kukhala m’mapiri ndi kupeza, monga ine ndinalalikira usiku wina, mtsinje umenewo ukutumphuka, gwero lake lopatsa moyo. Iwe ukhoza kukhala utatopa ndi waludzu, kugwera pansu pa mtsinje wabwino; kumusi kumene majeremusi sangakhoze kupitako, kutali komwe mapazi mahandirede pa dziko lapansi, akutumphuka madzi angwirowo, enieni, opatsa moyo. Ife timayamikira zimenezo. Izo ndi zapang’ono. Tsopano, dziko lapansi liri ndi mitsinje yake yambiri yokhala ndi madzi otsitsimutsa. Pamene ukumva ludzu ndipo ukufa, iwe umapeza chakumwa chabwino, chozizira kuchokera mmenemo, icho chima—icho chimakuthandiza iwe kukhala moyo.

⁴³⁶ Koma taonani kumene Uwu ukuchokera. Kuchokera ku Mpandowachifumu, pamenepo ndi pamene iwo umapeza zinthu

zake zopereka Moyo. Umachokera pansi pa Mpandowachifumu wa Mulungu, kumene amakhalako Mulungu.

⁴³⁷ Zonse za izo, zonse za dziko lapansi lino, dziko lapansi lino kuno kumene ife tikukhalamo tsopano; aliyense, kaya ndi Mkristu kapena wachikunja, ali ndi akachisi. Kodi inu munayamba mwaganizapo za zimenezo? Matchalitchi, onse a iwo.

⁴³⁸ Koma Uwu ulibe aliyense. Baibulo linati, “Ndipo munalibe kachisi mmenemo. Koma Ambuye Mulungu ndi Mwanawankhosa ndiye Kachisi wake.” Mwanawankhosa ndi Kuwala. Mwanawankhosa ndi Kachisi. Mwanawankhosa ndi Mpandowachifumu. Mwanawankhosa ndi Moyo. Iye ndi Kachisi ameneya. Mwaona, akachisi onsewa ali ndi chinthu chimene iwo akuchipembedza; koma, mu Mzinda uwu, Iye ndiye chinthucho. Iye ali ndi anthu Ake. Kuwala kwa Mzimu Wake kukusefukira Mzinda wa piramidi.

⁴³⁹ Monga Petro ndi Yohane, pamwamba pa phiri. Kuwala kunaphimba pamwamba pa phiri, ndipo Liwu linayankhula, linati, “Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa.”

⁴⁴⁰ Mu Chivumbulutso 21:3 ndi 4, “Kachisi wa Mulungu ali ndi anthu.” Mulungu wapanga kachisi mwa munthu, pomuwombola iye, pogwiritsa ntchito njira zitatu izi. Tsopano Mulungu akudzawombola dziko lapansi ndi kudzakhala mdziko lapansi, ndi omumvera Ake a padziko lapansi, amene Iye anawabweretsa kuchokera ku dziko lapansi. Ndipo kudzera mu tchimo ilo linagwa, koma a . . . Iye anayenera kulisiya ilo kuti lizipitirira. Koma tsopano Iye anamutuma Yesu kuti adzawombole dziko lakugwalo, limene ife tiri gawo lake. “Palibepo tsitsi limodzi la m’mutu mwanu lidzawonongeke.” Yesu ananena chomwecho. Iye anati, “Ine ndidzaliwukitsa ilo kachiwiri pa tsiku lotsiriza.” Mukuona? Bwanji? Ndinu gawo la dziko lapansi.

⁴⁴¹ Inu munazindikira, ine ndinali ndi nthabwala yaying’ono ya mkazi wanga akundiiza ine kuti ine ndathothoka tsitsi langa. Ndinamuza iye kuti sindinathothoke limodzi la ilo.

Iye anati, “Kodi ilo liri kuti?”

⁴⁴² Ine ndinati, “Kumene ilo linali ndisanalipeze ilo.” Kulikonse kumene ilo linali, chinthu chogwirika; kulikonse kumene ilo liri, ilo likundiyebekezera ine. Mukuona? Uko nkulondola. Ine ndidzapita kwa ilo, tsiku lina.

⁴⁴³ Thupi lakale ili, likuchita makwinya ndipo likugwa, ndi kumafota m’mapewa, ndi kupweteka mmaondo, ndi—ndi kusasa mawu pakhosi. Izo nzabwino. Inu mukhoza kulikwirira ilo mnyanja, koma Lipenga lidzandidzutsa ine! . . .? . . . Inde, bwana. Ife tidzasintha, limodzi la masiku awa. Ine ndi gawo la dziko lino limene lawomboledwa. Inu muli mdziko, koma palibe cha *kosmos*. Inu muli mu dongosolo lina, dongosolo la owomboledwa.

444 Zindikirani, “Kachisi wa Mulungu adzakhala ndi anthu.” Zindikirani, “Zinthu zoyambazo zapita.” Ichi, chinthu ichi, chapita. Izi zikutanthauza kuti Kumwamba kwatsika kudzakhala ndi munthu. Mukuona? Kumwamba ndi dziko lapansi zakumbatirana.

445 Ndendende basi pamene Nkhunda inabwera pa gawo la dziko lapansi, amene anali Yesu; Iye anali fumbi la dziko lapansi, Munthu. Mulungu, akubwera kuchokera ku nyongolosi ya Moyo yaing’ono ija, mwa mphamvu yolenga. Ndipo Magazi aja amene anali mmenemo. . . Moyo umene unali mu Magazi amenewo unakwera kubwerera kwa Mulungu, koma Magazi anawukhira pa dziko lapansi, kuti adzalitenge ilo.

446 Chifukwa cha magazi amene anabweretsedwa, kuchokera ku khungu la nyongolosi yochokera kwa Kaini, mwaona; tsopano Iye akubwereranso ndi mphamvu yolenga monga momwe Iye anachitira Adamu, kumulenga Adamu, apa pali Adamu Wachiwiri. Ndipo kudzera mu khungu losweka limenelo apo, pamene (tchimo) Kaini anaswa khungu la magazi limenelo pa olungama, mwaona, tsopano Khungu la Magazi ili. . . Chifukwa, iye anamupha Abele, koma Abele anabadwa mwakugonana.

447 Koma Mmodzi uyu sanabadwe mwakugonana. “Chinali chirengedwe cha Mulungu, chiyambi chake,” ndipo Iye anawombola dziko lapansi. Ndipo zonse za kasiamu, potashi, petroliyamu, kuwala kwa dziko, zomwe inu munapangidwa nazo, ndi zowomboledwa. “Palibe tsitsi limodzi lomwe lidzavulazidwe. Ndipo ine ndidzaliwukitsa ilo kachiwiri pa tsiku lotsiriza.”

448 Ndiye chiyani? Mulungu akutsika kudzakhala padziko lapansi. Chimene, Iye ndi gawo la ilo, thupi Lake Lomwe. Iye analiwukitsa ilo kwa kulungamitsidwa kwathu, ndipo ife timalungamitsidwa pokhulupirira izo ndi kuvomereza izo. Zindikirani mwa zoyimira, Yesu akudzakhala. . . Mu choyimira, Yesu akudzakhala munthu; Mulungu. . . kapena wokonzedweratu kuti adzatenge malo ake, kuti adzatiwombole ife, kuti adzapangitse zinthu zonsezi kukhala zotheka.

Zindikirani, kunja kwa makoma ake okongola, a Mzinda uwu.

449 Tsopano kodi mwawupeza “Mzindawo”? Mwaona, ndi Phiri loyera. [M’bale Branham akuwonetsera pa bolodi—Mkonzi]. “Palibe chimene chidzavulaze kapena kuwononga mu Phiri Langa loyera lonse, atero Ambuye.” Mzindawo si kabokosi. Iwo ndi Phiri. Ndipo a—mulifupi ndi kutambalala ndi mu utali mwake, ndi zofanana, mwaona; mailosi fifitini handirede mbali *iyi*, mailosi fifitini handirede mbali *iyu*, mailosi fifitini handirede kuzungulira mbali zonse; ndi mailosi fifitini handirede mu litali mwake. Chotero ndi Phiri lalikulu basi, monga piramidi, ndipo Mzindawo uli pa Phiri. Ulemelero!

450 Ndi zimenezotu, ndi amenewo maparadiso a Mulungu, Kuwala kwa dziko, Ufumu wangwiro uja. Osati tsiku la chisanu ndi chiwiri; la Muyayalo! Mukuona? Osati Zakachikwi; Dziko Latsopano! Mukuona?

451 Pamene ilo likudutsa mu Zakachikwi, ilo likudutsa mu njira yake yoyeretsedwa, komabe likuyenera kuwotchedwa. Mukuona? Chimene, Magazi anawawombola anthu, izo zikusonyeza chikumbutso ichi kuti ndicho...mtengo unalipiridwa, zaka sauzande zimenezo. Komano ilo liyenera kutsukidwa ndi Moto; chimodzimodzi monga zinachitikira ndi inu, nthumwi Zake za Mzinda uwu, nthumwi.

452 Chotero ngati mudzafa kapena mudzakhala moyo, izo zidzapanga kusi yana kotani? Ngati Iye angabwere lero, kapena Iye abwera zaka handirede, kapena zaka sauzande, ine ndidzangopuma kufikira kusintha kwanga kutadzabwera.

453 Chotero, mwamuna wokalamba ndi mkazi wokalamba, musakhumudwitsidwe. [M'bale Branham akuwonetsera pa bolodi—Mkonzi]. Ngati inu muli choimirira pamwamba *apa*, mu chikhumbo ichi cha Mulungu; *uyu*, Mulungu; ngati inu muli nacho icho, ngati inu mukuimiridwa *apa*, inu simungathe. . . Inu muli mu Muyaya. Ndipo ngati mwawoloka kuchokera pa tsiku lachiseveni limenelo, kulowa mu lachi eyiti, inu mwakalowa mu Muyaya mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, inu mwaphatikizidwa mu *Ili*. Tsopano, ngati inu mukungodalira pa kugirigisha, kapena kulumpha chokwera ndi chotsika, kapena, “Ine ndimachita *ichi*. Ine ndimasunga tsiku langa la chiseveni. Ine sindimadya nyama,” ndi zinthu monga choncho, zimenezo zidzawonongeka, mulimonse. Mukuona? Koma *Ili* ndi la Umuyaya. Mukuona? Ili ndi la Umuyaya, Phwando lomaliza la phwando la makachisi. Mukuona?

454 Phwando la misasa limakhala phwando lomaliza, phwando la chiseveni. Ife tikupembedza tsopano pansu pa phwando la makachisi, m'badwo wa mpingo wa chiseveni.

455 Mu Zakachikwi, ife tidzakhala pansu pa phwando la makachisi, kachiwiri, mu tsiku la chiseveni.

456 Koma, ndiye, litapita tsiku la chiseveni, ife tidzakhala ndi Msonkhano Woyera, kubwerera ku Umuyaya. Motani? Mwa Mmodzi Wamuyayayo amene anabwera ndi kudzatiwombola ife ndi kutibwezera ife, kutilola ife kuzindikira kuti ife tinali gawo la *Ichi*.

457 Tsopano iwe ungasaziwe bwanji kuti ndiwe gawo? Chifukwa, chakuti, Mawu a ora, lonjezo la tsikuli. Icho ndi chiyani? Kubwezeretsa kubwerera ku tsiku loyamba, loyamba. “Ndipo adzabwezeretsa mitima ya ana kwa atate,” kubweretsa kubwezeretsanso kwa chipentekoste chenicheni, osati zogirigisha; ndipo adzawonetsera Kuwala kwa madzulo,

Mwana yemweyo amene anawonekera mu Kuwala kwa mmawa, monga momwe analonjezera tsikuli. Amen! amen!

⁴⁵⁸ Kodi ife tiri pati, abwenzi, ife tiri kuti? Tikungoyembekezera tsopano kuti tichoke panjirayi, kuti Chivumbulutso 11 akhoze kupangidwa . . . adziwike kwa Ayuda; ndiko kulondola, Mkwatulo ukubwera.

⁴⁵⁹ Penyani, kunjira kwa zipata za makoma, kufalikira pa Dziko Latsopano, mafuko adzakhala mu mtendere Wamuyaya. Tsopano chiyani? Mafumu olemkezeka azidzabweretsa ulemelero wawo mmenemo. Palibe tchimo lingakhale kumeneko. Palibenso akazi odula tsitsi ati adzalowe mu Mzinda umenewo. Ine ndikukutsimikizirani inu zimenezzo. Palibenso mahule ovala zazifupi, achigololo-osuta ndudu, mahule, kapena abodza, opembezeka mafano, chirichonse chimene iwo anali, sadzalowa mu Mzinda umenewo. Ayi, izo zonse zidzakhala zitatha. Tchimo lidzakhala litapita. “Palibe chodetsa chiyero chake chidzalowe mmenemo.” Ndi chimene Iye ananena. “Zonse zapita, kwanthawizonse.”

⁴⁶⁰ Yang’anani mminda yake ndi kuzungulira zipata zake:

Chimbalangondo chidzakhala chodekha,
nkhandwe idzakhala yosawopsya;
Ndipo mkango udzagona panso limodzi ndi
mwanawankhosa;
Ndipo chilombo cha kuthengo,
chizidzatsogozedwa ndi mwana;
Ndidzasinthidwa kuchoka ku cholengedwa
chimene ine ndiri.

⁴⁶¹ Ndi imfa iyi ikugwira ntchito mu thupi langa lachivundi, ukalamba ukulowamo, ine ndidzasinthidwa.

⁴⁶² Inu mwaimvapo nyimboyo? “Chimbalangondo chidzakhala chodekha. Nkhandwe idzakhala yowetedwa.” Iyo siidzalumphira mmwamba, ndi kudzuka ndi kuyesa kukuphani inu. Iyo idzayenda nanu mu njira.

Ndani ati adzalandire izo? Owomboledwa. Iwowo adzakhala ndani?

Zindikirani, ine ndikhoza kungophunzitsa mwa zoyimira tsopano. Mukuona, M’bale Lee.

⁴⁶³ Ndani anatuluka pa dziko latsopano ndi mneneri Nowa? Iwo amene analowa naye mu chombo. Nkulondola uko? Amenewo ndi amene akutuluka pa icho. Mukuona? Iwo amene analowa umo ndi Nowa, mwa uthenga wake, anali iwo amene anatuluka pa dziko latsopano utatha ubatizo wake wa madzi.

⁴⁶⁴ Iye amene akulowa ndi Yesu tsopano. Inu mumalowa bwanji mwa Iye? Mwa Mzimu umodzi; ndipo Iye ndi Mawu. Inu mumadzakhala gawo la Iye. Inu ndi gawo lanji la Iye? Mawu amene akukhala moyo a ora lino, akuzindikira. Inu mudzatuluka

ndi Iye mu Zakachikwi. Ndi pamene inu muzidzatulukira. Zindikirani, osati kam'badwo katsopano. Kowokeredwa!

Inu mukuti, "Oh, M'bale Branham!" Oh!

⁴⁶⁵ Zindikirani, ngati Mulungu anakhoza kumuwukitsa Eliya ndi kumutengera iye mmwamba, zaka twente-faivi handirede zapitazo, kuti adzamusamutsire iye kubwerera ku dziko lapansi kachiwiri, kuti adzakhale mneneri wa Ayuda, ndi mochuluka bwanji momwe Iye angachitire ndi Mkwatibwi!

⁴⁶⁶ Nowa atatuluka mu chombo, zindikirani chimene chinanenedwa kwa Nowa atatuluka mu chigumula, chimodzimidzi monga zinakhilira ndi Adamu poyamba. Iye atatuluka, pa dziko latsopano; anati, "Muchulukane ndipo mulidzadzitse dziko lapansi," kusefukira kutachitika. Zindikirani, "anali oti abalane, alidzadzitse dziko lapansi," monga Adamu poyambirira.

Tsopano inu mukhoza kuwona ndendende apa. Tsopano mvetserani mwacheru kwenikweni.

⁴⁶⁷ Adamu anali woti "achulukane, kulidzazitsa dziko lapansi." Nkulondola uko? Nowa anali woti, zitachitika kuti, (dziko latsopano lawonongedwa), anali woti "achulukane ndipo alidzadzitse dziko lapansi." Mukumvetsa zimenezo? Tsopano kodi inu simukuwona chimene "mbewu" ya serpenti ili? Chinalidzadzitsa dziko lapansi ndi chiyani? Inu mukumvetsa zimenezo? Chabwino. Inu muwona momwe Satana anafikira kwa Eva tsopano. Ndi chifukwa chake imfa yalamulira padziko lapansi kuyambira pamenepo. Ndipo miyamba, dziko lapansi, chirombo, mlengalenga, zonse ndi zotembereredwa ndi Mulungu chifukwa cha izo. Limenelo ndi themberero, chifukwa Satana anafika kwa ilo poyamba.

⁴⁶⁸ Yesu anabwera kuti adzaliwombole ilo kubwerera kwa Atate. Kutu achite izi, Iye anadzakhala gawo la ilo; monga ine ndangadutsamo kumene. Ndipo kuchokera ku fumbi lomwelo (gawo limene Yesu anali, Iyemwini) akuwomboledwa, kudzera mwa Iye zikhumbo zonse za Mulungu zimawomboledwa ndi dziko lapansi.

⁴⁶⁹ Iye anali Mawu oyankhulidwa. Iye amene tinawomboledwa ndi gawo la Iye. Ndiye, ngati inu mungathe kuzindikira! Mukuona?

⁴⁷⁰ Afarisi ankadzinenera kuti anali. Koma, inu mukuona kufotokoza kwanga koyamba, iwo anali kokha aluntha. Iwo sankakhoza kuwazindikira Mawu pamene Iwo anawonetseredwa pamaso pawo pomwe. Iwo anati, "Munthu uyu ndi mzimu woyipa."

⁴⁷¹ Tsopano, lero, ife tikumatchedwa aneneri abodza. Iye tikumatchedwa chinthu chauve chirichonse chimene tingakhoze

kutchulidwa, ndi anthu achipembedzo, mwaona, ndi amuna aakulu ndi aluso. Mwaona, iwo sakumvetsa basi. Mukuona?

⁴⁷² Ubatizo wake wa madzi sunali wokwanira kuliyeretsa ilo; ngakhalenso wawo. Kuyeretsedwa, kwa Magazi, kunalibweretsanso ilo, kudzalitenganso ilo. Koma ubatizo wa Moto unaliyeretsa ilo; monga uwo unachitira ndi Mkwatibwi Wake. Monga kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera.

⁴⁷³ Sanalonjeze konse kuti adzadzutsa mtundu watsopano, monga ine ndanenera, koma Iye analonjeza kuti adzawombola akugwawo. Iwo amene anali—okonzedweratuwo, adzalandira ilo monga Iye analonjezera. Ndipo Iye ndi Mulungu wosasintha; ife tikudziwa zimenezo.

⁴⁷⁴ Kumbukirani, Mulungu anamutenga Eliya, utatha mkwatulo, ndipo anamusanduliza, anamusamutsira iye kubwerera pakati pa anthu, kuti atenge malo ngati mneneri pakati pa anthu ake; posachedwapa Iye adzachita zimenezo. Ndipo wamusunga iye, wamoyo, zaka twente-faivi handirede izi. Iye ali woti adzawonekeranso.

⁴⁷⁵ Zindikirani kachiwiri, Iye anamuukitsa Mose kwa akufa. Manda ake ali kuti? Kodi alipo amene angawapeze iwo? Muwerenge Bukhu la Yuda. Mukuona? Satana... Mngelowamkulu akukangana ndi mngelowamkulu, Satana, anati, kulimba mtima... “Yehova akudzudzule iwe,” akutsutsana pa thupi la Mose. Ndipo apa Petro, Yakobo ndi Yohane anali atayima pamenepo akuyang’ana pa iye, pa Phiri la Chiwalitsiro, komwe uko mdziko limene Phiri likuyenera lidzakwezedwe mmwamba kuti tidzakhalemo. Mukuona?

Ndipo Iye anabwera kuti adzawombole ilo.

⁴⁷⁶ Mwaona, apo panali Mpingo wokwatulidwa pamenepo, woyimiridwa; apo panali iwo amene akugona, atayimiridwa. Kutu? [M’bale Branham akuwonetsera pa bolodi mu ndime zingapo zotsatirazi—Mkonzi]. Mu Mzinda; pamwamba pa phiri. Mukuona?

⁴⁷⁷ Apo panali Petro, Yakobo, ndi Yohane, akuyang’anapo; atatu, mboni. Apo panali Eliya, Mose, ndi Yesu; monga mboni za Kumwamba. Mukuona?

⁴⁷⁸ Ndipo apo panali Mose, wakufa, anali atawukitsidwa. Apo panali Eliya, mkwatulo, anali akanali wamoyo. Ndipo iwo onse anali ataimiridwa pa phiri lopatulika ili.

⁴⁷⁹ Ndipo, Yesu, Muwomboli. Pamene Mulungu, pamwamba pa Iye monga *chonchi*, anamuphimba Iye, anati, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa.”

⁴⁸⁰ Inu mukukumbukira, Yesu anati, pafupifupi tsiku zisanachitike zimenezo, Iye anati, “Indetu ndinena kwa inu, kuti

ena ayima pano tsopano, sadzawona imfa, kufikira atadzawona Ufumu wa Mulungu ukukhazikitsidwa mu mphamvu.”

⁴⁸¹ Icho chinali chiyani? Akufa owukitsidwa ndi oyera okwatulidwa, limodzi, anakwatulidwa limodzi kukakomana ndi Iye mu mlengalenga. Ndi Mulungu akumuphimba Iye, ndi Yesu atayima pamenepo mu mthunzi uwu, akuti, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa, mwa Yemwe Ine ndikondweramo,” dongosolo la Ufumu Watsopano. Oh, m’bale, mlongo!

⁴⁸² Imfa simakusinthani inu. Imfa imangosintha malo anu okhala. Mukuona?

⁴⁸³ Kumbukirani, Samueli, atamwalira ndi kuyikidwa m’manda kwa zaka ziwiri, iye anali mu Paradiso. Ndipo mfiti ya ku Endori inamuyitana iye, ndipo Sauli anamuzindikira iye; ndipo iye anatero, nayenso, ndipo anagwa pa nkhope yake. Iye anali asanasinthe, ngakhale pang’ono. Iye anali akadali Samueli yemweyo, atafa zaka ziwiri, ndipo iye anali akadali mneneri. Iye anati, “Mawa iwe udzagwa ku nkondo, mwana wako pamodzi ndi iwe, ndipo podzafika nthawi ino mawa usiku iwe udzakhala ndi ine.” Ndipo ndicho basi chimene chinachitika.

⁴⁸⁴ Mukuona? Ndipo pamene Mose azidzabwereranso, ndi Eliya, kwa Chivumbulutso 11, iwo adzakhale akadali aneneri. Aleluya!

⁴⁸⁵ Ndipo kutsidyako, mu Dziko, Mzinda umene Mwanawankhosa ali Kuwala, ine ndidzakudziwani inu, M’bale McKinney. Ine ndidzakudziwani inu, anthu anga, ngale zanga mu korona. Pamene iwo azidzabwera kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo, kupita ku Mzinda; pamene mailosi fifitini handiredi mbali zonse zonse, iye adzakhala atakhala pamenepo, ndipo Mzindawu unamangidwa mbali foro zofanana. Pamene inu mudzakhale pamenepo mu Phiri loyera, pamene Mulungu adzakhala pa Phiri, ndi Yesu pa Mpandowachifumu. Ndipo lipenga lagolide likuwomba pamene Yosefe azidzanyamuka, kuti akayende kudutsa mu Paradiso, ndipo ana a Mulungu akugwa pa maondo awo ndi kamamupembedza Iye, akudziwa kuti iwo anali owomboledwa. Mukuona? Ameni! Aleluya!

Nthawi zina ndimapukwa kwathu
Kumwamba,

Ndi ulemelero umene Ine ndidzawuwona
Kumeneko:

Chidzakhala chisangalalo chotani pamene
Mpulumutsi wanga ndidzamuwona,
Mu Mzinda wokongola wagolide umenewo!

Ine ndikupita ku Mzinda wokongola umenewo
Ambuye wakonza . . . [Malo opanda kanthu pa
tepi—Mkonzi].

⁴⁸⁶ Yesaya anati, mu Yesaya 9:6, “Ndipo za mtendere Wake ndi zochulukitsa Zake kumeneko sizidzatha. Ulamuliro udzakhala

pa mapewa Ake; Dzina lake lidzatchedwa Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha. Ndipo ulamuliro udzakhala pa mapewa Ake; ndipo za kukula Kwake ndi za mtendere Wake ziribe malire.” Ngakhale nyama ziri kumeneko. Oh, mai!

Chimbalangondo chidzakhala chofatsa, ndipo
 nkhandwe idzakhala yosawopsya;
 Ndipo mkango udzagona pafupi ndi
 mwanawankhosa,
 Ndipo chilombo cha kuthengo,
 chizidzatsogozedwa ndi mwana;
 Koma ndidzasinthidwa, ine ndidzasinthidwa
 kuchoka ku cholengedwa ichi chimene ine
 ndiri.

⁴⁸⁷ Pamene Tsiku limenelo lidzafika, pakuti ine ndikupita ku Mzinda umenewo. Ndikupita ku Mzinda wokongola umenewo! Ine ndikumverera Mphamvu yowombola mu mtima mwanga monse tsopano.

⁴⁸⁸ Ngati izi siziri chomwecho, ndiye kuti ine ndataya moyo wanga; ndawaphunzitsa ena zinthu zachinyengo. Koma pamene ine ndiyang’ana pansi ndi kuwona kuti lonjezo limene Iye analipanga la tsiku lino, ndi kuliwona Ilo likutsimikiziridwa; ndi kuyang’ana pa osonkhana awa a mailosi fifitini handirede mbali zonse zonse amene akhala apa, Osankhidwa amene ayitanidwa kuchokera ku zipembezdo ndi mafuko ndi tizikhulupiriro ndi zinthu, atasonkhana pamodzi; pamene ine ndiwona Mawu akudzitsimikizira Okha, ine ndimaziwa, kudutsa mthunzi umodzi wa kukayikira, ngale za koronga wanga zidzaposi kuwala chirichonse mu dziko, pa Tsiku limenelo.

⁴⁸⁹ Idzafikapo nthawi! Anthu, ife sitikusonkhana pano kwachabe. Ife tikungoyembekezera nthawi imeneyo. Iyo kwambiri, nthawi yatha kwambiri, koma Yesu mpaka panobe, ali pafupi kwambiri. Ndipo, Ulemelero Wake, ndi wodabwitsa. “Dzina Lake lidzatchedwa Wauphungu.” Mzinda umenewo, kodi inu mukukhaza kuwuwona iwo? Kumeneko ndi kumene Mkwatibwi ndi Mkwati adzakhaleko, ndipo sizidzachitikanso kuti adzatero . . .

⁴⁹⁰ Tsopano, ngati mukuganiza kuti ndi zodabwitsa pamene ife timayenda mahandirede a mailosi kuti tidzakhale pano ndi kumadya pa Mawu Ake, chimene ichi chiri mthunzi chabe, zidzakhala bwanji tikadzakhala mu Mzindawo limodzi ndi Iye! Ndikadzakhala woyandikana nanu, ndi pamene ife tizidzadya za mitengo imeneyo, ndipo tizidzayenda m’misewu imeneyo, pamene tizidzayenda chokwera mmisewu iyo ya golide tikupita ku kasupe, kumwa kuchokera mu kasupe, tikuyenda kulowa mu paradiso wa Mulungu, ndi Angelo akuyendayenda padziko lapansi, akuyimba nyimbo za fuko, oh, lidzakhala Tsiku

lotani limenelo! Izo ndizoyenera zonsezo. Msewu umawoneka wokhotakhota, nthawizina umavuta, koma, oh, zidzakhala zazing'ono kwambiri pamene ine ndidzamuwona Iye, zazing'ono kwambiri. Kodi maina oyipa ndi zinthu zimene iwo anena, kodi izo zidzakhala chiyani pamene ine ndidzamuwona Iye mu kukongola kumeneko, Mzinda wokongola wa Mulungu?

491 Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

Ine ndikupita ku Mzinda wokongola umenewo
 Ambuye wanga wakonzera Ake Omwe;
 Kumene Owomboledwa onse a mibadwo yonse
 Amayimba “Ulemelero!” kuzungulira
 Mpandowachifumu Woyera.
 Nthawizina ndimapukwa kwathu
 Kumwamba,
 Ndi ulemelero wake umene Ine ndidzawuwona
 Kumeneko:
 Chidzakhala chisangalalo chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ndidzamuwona,
 Mu Mzinda wokongola wagolide umenewo!

492 Pa chisumbu cha Patmo, Yohane anawuwona iwo!

493 Wokonedwa Yesu, chiyembekezo ichi, chiyembekezo changa sichinamangidwe pa chirichonse, Ambuye. Umenewo ndi mayi wa mtima wanga; Mzinda umenewo, Mfumu yayikulu. Mulungu, musalole kuti mmodzi adzawonongeke pano, chonde. Mulole ife tiwunikenso miyoyo yathu, lero, Ambuye, tikuyembekezera Kudza kwa Ambuye. Kumene, Owomboledwa onse amenewo, kutali uko mu bwalo lalikulu la masewera mu Roma, kumene Akhristu amenewo anadyedwa ndi mikango, fumbi lidzaphulika tsiku lina!

494 Sipadzakhala manda pa mbali ya phiri la Ulemelero. Palibe zogwirira zitseko zokhala ndi nkhatta yamaliro. Palibe misozi yomwe idzawonekepo. Ayi, ayi. Palibe kapinga wochita kupanga wowunjika. Palibe namondwe amene adzakantha iyo. Zonse zidzakhala zaulemelero pamenepo.

495 Tithandizeni ife, Ambuye. Ngati pali wina pano . . . amene akuyitanidwa ku Mgonero wa Chikwati cha Mwanawankhosa uwu, zaka sauzande izi za ulamuliro wa Zakachikwi, ndipo kenako nkudzalowa mu Mzinda chitatha Tchuthi cha ukwati. Zakachikwi ndi Tchithu cha ukwati chabe. Ndiye Iye, Mkwatibwi, adzamtengera Wake . . . Mkwati adzamtengera Mkwatibwi Wake Kwawo. Ndi Wake. Mkwati Wake; Mkwatibwi Wake. Oh, Iye anapita kukamukonzera Nyumba, popeza Iye watomeredwa.

496 Mulole ife tikhale owona kwa Iye Amene ali Mawu, pakuti Iye ndi Mawu. Mosalabadira momwe ena amayesera kukangana ndi ife, kutitalikitsira ife kutali ndi Iwo; Ambuye, ndikokereni ine pafupi.

Pakuti nthawi zina ndimapukwa kwathu
 Kumwamba,
 Ndi ulemerero wake umene Ine ndidzawuwona
 Kumeneko:
 Chidzakhala chisangalalo chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ndidzamuwona,
 Mu Mzinda wokongola uja wa golide!

⁴⁹⁷ Kwawo kwamtsogolo kwa Mkwati ndi Mkwatibwi! Iye akubwerera... [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]... ku Mgonero wa Chikwati; zidzakhala masiku atatu ndi theka. Kenako nkudzabwerera kachiwiri, mu Zakachikwi, pa tchuthi chathu cha ukwati. Ndipo kenako Iye—Iye adzabweretsa Mzindawo powonekera. Monga mkwati akumtenga mkwatibwi momudzidzimutsa iye, mmene mkwatibwi wamng'onoyo amaima pamenepo modabwitsidwa pamene iye akuyang'ana kwawo kwa mtsogolo! Ndipo mwa chikhulupiro, lero, Ambuye, ife tikuziwona izo kutaliko. Izo zidzakhala pomwe pano pa dziko lapansi. Inu munalonjeza izo.

⁴⁹⁸ Mpingo Wanu udzawomboledwa kwathunthu, limodzi la masiku awa. Ndipo kenako dziko Lanu lidzawomboledwa, zidutswa zina zonse. Koma choyamba Inu munawawombola anthu Anu, matupi awo amene anapangidwa ndi dziko.

⁴⁹⁹ Tithandizeni ife, Mulungu. Ngati alipo mmodzi pano amene sali wotsimikiza ndendende basi za izo, Ambuye, mulole iwo alandire izo pakali pano.

⁵⁰⁰ Ndikudziwa kuti kwakhala motalika komanso kotentha, koma, anthu, sikuti nthawizonse tizikhala titaima pano. Ine sindidzakhala nthawizonse m'busa wanu. Tiyeni titsimikize izo.

“Kodi ilipo njira, M'bale Branham?”

⁵⁰¹ Inde, khalani gawo la Mawu, gawo la Mawu a lero. Sangakhale gawo la Mawu a tsiku la Mose; gawo limenelo linapangidwa, amenewo anali mapazi. Ife tiri ku Mutu tsopano. Uyu ndi Khristu. Osati nthawi ya mikono, mmbuyo mwa Luther, ayi. Ino ndi nthawi ya Mutu. Khristu, Mwalawapamutu, umabwera ku Thupi.

⁵⁰² Ngati inu simukumverera bwino ndendende za izo, kulikonse kumene inu mungathe, mungakweze mmwamba dzanja lanu kuti ine ndithe kuliwona. Aliyense ayike mutu wake pansu. Mulungu akudalitseni inu.

⁵⁰³ Munene kuti, “Ndikumbukireni ine mu pemphero, M'bale Branham. Ndikufuna ndidzakhale kumeneko moyipa kwambiri! Ine—ine sindikufuna kuti ndizakuphonye kumeneko, M'bale Branham. Ine—ine ndikufufuza, ndikuchita chirichonse chimene ndingathe, koma mundipempherere ine tsopano, inu mutero?” Mulungu akudalitseni inu.

504 Pamene mukuganizira za izo tsopano, mungopemphera, muziti, “Mulungu . . .” Izo ziri mu mtima mwanu. Mwaona, ngati inu mukumverera chinachake chikukoka, chikubaya pa mtima wanu, icho ndi chimene icho chiri. Ndi chokhumba chimenecho chikuyesera kudziwonetsera chokha.

Ine ndikupita ku Mzinda wokongola umenewo
 Ambuye wanga wakonzera Ake Omwe;
 Kumene Owomboledwa a mibadwo yonse
 Adzayimba “Ulemelero!” mozungulira
 Mpandowachifumu Woyera.
 Nthawi zina ndimapukwa Kumwamba,
 Ndipo ulemelero ine Kumeneko
 ndidzawuwona:
 Chidzakhala chisangalalo chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ndidzamuwona,
 Mu Mzinda wokongola wagolide umenewo!

505 Atate Akumwamba, titengeni ife tsopano, Ambuye. Mulole M’busa Wamkulu, M’busa Wamkulu Wowombola, M’busa Wamkulu Amene anasiya Ulemelero, podziwa kuti zina za zikhumbo zinatayika pa zigwa zazikulu izo za tchimo, kumene mimbulu ndi—nyama posachedwa zidzadya nkhoa yaying’ono imeneyo; koma Iye anasiya makonde a golide, anatsika pansu pa dziko lapansi ndipo anadzapangidwa mmodzi wa ife, kuti Iye adzathe kulengeza chikondi cha Mulungu kwa ife. Pamenepo Iye anawapeza iwo, ena a iwo mu zipembedzo, ena a iwo m’nyumba ya mbiri yoipa, ena a iwo mmisewu, akhungu, ena a iwo mmipanda ndi msewu wawukulu, koma Iye anamuwombola aliyense amene Atate anamudzodzera Iye kuti adzamuwombole.

506 Ndipo Iye anatilamulira ife, kuti ife tidzakhale gawo ili la Mawu kwa mibadwo yathu. Ndipo ife tikuwona kukonzanso kwakukulu kwa Luther, mu m’badwo umenewo; ndi kwa Wesley; ndi Achipentekoste. Tsopano tikuyang’anira Mwalawapamutu wa Mzinda. O Mulungu, ife tikudziwa m’badwo ndi lonjezo limene ife tapatsidwa la tsiku lino, momwe Izi ziti zidzabwezeretsedwenso. “Kuwala kwa kumadzulo kudzachetsa chipatsocho. Ndipo kudzachitika kuti padzakhala tsiku limene silingakhale usana kapena usiku, likhoza kutchedwa, koma mu nthawi ya kumadzulo kudzakhala Kuwala.”

507 Yemweyo Mwana waulemelero wa Mulungu wodziwonetsera Yekha mu thupi la munthu kuno pa dziko lapansi, kupangitsa lonjezo kudzikhala lokha moyo ndendende, kuchititsidwa khungu ku maso a Afarisi ndi Asaduki ndi Aherode, ndi ena otero.

508 Ndipo lero izo zikubwereza kachiwiri, Mawu akuwonetseredwa basi monga Iwo ankakhalira. Mawu, podziwa chinsinsi cha mtima, ndendende basi momwe izo

zinkakhalira, monga Lemba linanenera, zomwe sizingathe kusweka. Tithandizeni ife, Mulungu, kuti tizindikire izo.

⁵⁰⁹ Athandizeni awa tsopano amene anakweza manja awo. Mulole iwo amange mothinita pang'ono; adziveke okha ndi Uthenga wa mtendere; avale zida zathunthu za Mulungu; akokere chipewa pansu; atenge chishango cha chikhulupiro; aziguba chitsogolo, kuyambira lero mpakana. Perekani izi, Ambuye.

⁵¹⁰ Kanthawi pang'ono chabe, ife tiyitanidwa, kenako Mkwatulo udzabwera. Gulu laling'ono chabe, monga Enoki, lidzatengedwera mmwamba.

⁵¹¹ Kenako, “otsalira a mbewu ya mkazi, amene amasunga malamulo a Mulungu,” Ayuda, “ali ndi umboni wa Yesu Khristu,” Amitundu, adzasakidwa ngati agalu, “ndipo adzapereka moyo wawo chifukwa cha umboni wawo.”

⁵¹² Kenako, mmawa wina wawukulu, kuyambika kwa Zakachikwi, za—Tchuthi cha ukwati chidzayambika.

⁵¹³ “Ndipo kenako akufa onse sanakhale ndi moyo kufikira kutha kwa zaka chikwi.” Kenako, pa mapeto a zaka chikwi, panali Chiweruzo, kusonyeza kuti Hamu anali mu chombocho. Ndipo Hamu akadali mmenemo mwa otsalirawo. Iwo amene anawamva Iwo ndipo anawakana Iwo adzayenera kuti adzaweruzidwe.

⁵¹⁴ Tsopano, perekani izi, Ambuye, kuti ife tisadzaganiziridwe pakati pawo, koma tidzakhale mu kuitaniridwa ku Mgonero wa Ukwati. Pakuti, ife tikumuzindikira Yesu pakati pathu lero. Ife tikupita mmenemo ndi Iye; kuchoka mdziko, kukalowa mwa Iye. Tiloleni ife tiziyenda mu Mzinda umenewo, tituluke limodzi ndi Iye.

⁵¹⁵ Ndikukalamba, Ambuye. Ine ndiribe maulaliki ochuluka oti ndilalikire. Koma ine ndithudi ndikudalira Inu. Ine ndikufunafuna Mzinda umenewo, monga bambo wanga Abrahamu anachitira. Pali Chinachake mwa ine chikunena kuti iwo ukubwera. Ine ndikuyesetsa kulikonse, Ambuye, kuti ndifalitse Kuwala ndi kuwayitanira iwo. Musalole mmodzi wa awa, Ambuye. . .

⁵¹⁶ Mokongola bwanji, kanthawi kapitako, Inu munawululira izo kwa ine. Kuchokera ku mkombelo wa pafupifupi mailosi fifitini handiredede, basi mmodzi *apa* ndi *apo*, akhala limodzi lero, amene anasonkhana pa malo amodzi aang'ono, akuyembekezera Mzinda umenewo kuti uwonekere. Ife tikudzinenera kuti ndife amwendamnjira ndi alendo. Ndife otayidwa. Wachikunja, dziko, limawaseka ndi kuwasereula; zipembezozabungwe zimawanyogodola; koma ife sitimasunthidwa ndi zinthu zimenezo. Mutipange ife gawo la Mawu, Ambuye, osasunthika. “Zidzachitika m'masiku otsiriza.” Mulole ife tikhale ifeyo,

Ambuye, mulole ife tikhale owerengedwa pakati pawo. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

⁵¹⁷ Inu mukukhulupirira zimenezo? Tiyeii tikweze manja athu monga *chonchi*.

Ine ndikupita ku Mzinda wokongola umenewo
 Ambuye wanga wakonzera Ake Omwe;
 Kumene Owomboledwa onse a mibadwo yonse
 Azidzayimba “Ulemelero!” akuzungulira
 Mpandowachifumu Woyera.
 Nthawizina ndimapukwa Kumwamba,
 Ndipo ulemelero Kumeneko ine
 ndidzawuwona:
 Oh, chidzakhala chisangalalo chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ndidzamuwona,
 Mu Mzinda wokongola wagolide umenewo!

⁵¹⁸ Tsopano, ngati ife titi tidzakhale mu Mzinda umenewo limodzi, mungogwirana chanza ndi winawake, ndikuti, “Mulungu akudalitse iwe, mwendamnjira. Iwe ukuchokera kuti? Louisiana, Georgia, Mississippi? Ndine mwendamnjira, nanenso. Ine ndikufunafuna Mzinda umenewo.”

⁵¹⁹ Ine ndikufunafuna Mzinda umenewo, M’bale Neville, cha uko. Ife tikufika cha kumeneko. . . ? . . . M’bale Capps, ine ndikufunafuna Mzinda umenewo, panobe, usikuuno.

Ndipo ulemelero wake Kumeneko ine
 ndidzawuwona:
 Chidzakhala chisangalalo chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ndidzamuwona,
 Mu Mzinda wokongola wagolide umenewo!
 Oh, chimbalangondo chidzakhala chodekha,
 ndipo nkhandwe idzakhala yosawopsya;
 Ndipo mkango uzidzagona pafupi ndi
 mwanawankhosa, oh, eya;
 Ndipo chirombo chochokera . . .
 chizidzatsogozedwa ndi mwana;
 Ndipo ine ndidzasinthidwa, kusinthidwa
 kuchoka ku cholengedwa ichi chimene ine
 ndiri, oh, eya.
 Oh, mudzakhala mtendere mu chigwa kwa ine
 tsiku lina;
 Oh, mudzakhala mtendere mu chigwa kwa
 ine . . . (Chabwino! Eya!)
 Sikudzakhalanso chisoni, sikudzakhalanso
 kukhumudwa, sikudzakhalanso vuto ine
 ndidzaliwone;
 Ndipo mudzakhala mtendere mu chigwa kwa
 ine.

520 Mfumu yathu yosawoneka, mmawa uno, idzawonetseredwa. Ine sindidzamuwona Bill Dauch ali wa usinkhu wa zaka nainte. Inu simudzayang'ana pa ine ngati fifite. Koma ine ndidzasinthidwa, Tsiku limenelo.

Ndipo pamene chirombo cha kuthengo,
chizidzatsogozedwa ndi mwana;
Koma ine ndidzasinthidwa, kusinthidwa
kuchoka ku cholengedwa ichi chimene ine
ndiri.

521 Kodi simudzasangalala? Imvi zidzatha; mapewa okugwa. Koma kukongola, chisavundi, zidzaima mu chifaniziro Chake, dzuwa kuti liwale moposa. Oh, zodabwitsa!

. . . kwa ine, oh, Ambuye, ndikupempherera;
Sikudzakhalanso kukhumudwa,
sikudzakhalanso chisoni, sikudzakhalanso
vuto ine ndidzaliwone;
Ndipo mudzakhala mtendere mu chigwa kwa
ine.

522 Icho ndi chimene tadzera pano. Ndi angati a inu amene mukusowa mphamvu ya ulendowu? Mulungu apereke iyo kwa ife! Ndi angati a inu akudwala mu thupi lanu, asilikali ovulala? Thwelofu, kapena oposerapo. Inu mukukhulupirira Iye ali pano, Mfumu yosawoneka? Zinthu zowoneka; zosawoneka zimawonetseredwa ndi zowoneka. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, thupi logwirika lokha. Tsopano, ngati uwu uli Mzimu Wake umene walalikira izi kudzera mwa ine, Iye achita ntchito zimene Iye anachita pamene Iye anali kuno. Oh, nzodabwitsa bwanji!

Ndikupita ku dziko lolonjezedwalo,
Ndikupita ku dziko lolonjezedwalo;
O ndani ati abwere ndi kupita nane?
Ndikupita ku dziko lolonjezedwalo.

Paliponse mu zigwa zotambalala zonsezo
Kukuwala Tsiku limodzi Lamuyaya;
Kumeneko Mulungu Mwana amalamulira
nthawizonse,
Ndipo amabalalitsira usiku kutali.

Oh, ndikupita ku dziko lolonjezedwalo,
Ndikupita ku dziko lolonjezedwalo;
Oh ndani ati abwere ndi kupita nane?
Ndikupita ku dziko lolonjezedwalo.

523 Faivi handirede akuyenda kukalowa mu mtsinje kutsidyako, tsiku loyamba limene Mngelo wa Ambuye anawonekera, kuti adzatsimikizire, monga Iye anachitira pa Phiri la Sinai, kuti ine ndinali nditakomana naye Iye. Ine ndinalowa mu mtsinjewo, ndipo mahandirede akuyimba nyimbo yomweyo ya ubatizo. Apa Iye anabwera, akutsika, Lawi la Moto lomwe

lija limene mukuliwona pa chithunzi apo; akutsikira pansi, pansi pomwe apa pa mtsinje, ndipo anati, “Monga Yohane M’batizi anatomidwa kuti adzatsogolere kudza Kwake koyamba, Uthenga uwu udzatsogolera Kudza kwachiwiri.” Mukuona? Ndi zimenezotu pamenepo, mwaona.

O ndani ati abwere ndi kupita nane?
Ndikupita ku dziko lolonjezedwalo.

⁵²⁴ Lawi la Moto lomwelo liri pano ndi ife. Kodi inu mukudziwa zimenezo? Iye anatipanga ena a ife chifukwa cha chinthu chimodzi, ndipo ena china. Ngati mungathe, popanda kukayikira kumodzi, mukhulupirire kuti Iye ali mkati mwa chipindachi, ine ndikukhulupirira Iye adzitsimikizira Yekha kwa inu. Kodi izo zikukhutitsani inu? Ngati ine sindifikira kwa aliyense. . . Iyo ikupita kuti ikakwane thuu koloko, koma ngati inu. . . Ndi pang’ono itadutsa wani, kani. Ngati inu mungakhulupirire, muloleni Iye atsikire pa ife! Kodi chikhulupiriro chathu chiri kuti? Mwaona, inu mukuyenera kukhulupirira zimenezo. Ngati inu simukukayikira izo, pang’ono, izo zigwira ntchito.

⁵²⁵ Ine—ine ndikuzindikira Kukhalapo Kwauzimu kwa Umunthu wa Khristu, Amene ali Mawu. Ndipo Baibulo linati, “Mawu ndi. . . amphamvu kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo Iwo amadula mpaka ku mafuta a mmafupa, ndipo amazindikira malingaliro amene—amene ali mu mtima, kuwulula chinsinsi cha mtima.”

⁵²⁶ Taonani. Bwanji, ine sindimazidziwa zinthu zimenezo, zaka zapitazo. Ndipo pamene ine ndinanena izo, osadziwa izo, onani chimene Iye wachita. Iye anati, “Tsopano iwe udziwagwira anthu pa dzanja lawo, ndipo, usaganize kalikonse, izingoyankhula chikhumbo chimene chanenedwa kwa iwe. Kunena kuti ndi chotupa, chirichonse chimene icho chiri.” Kenako anati, “Zidzachitika kuti iwe sumadzasowa kuchita zimenezo.” Mukuona? Mukuona? “Iwo adzazindikira chinthu chomwecho chimene chiri mwa iwo.” Ife takhala nayo mitundu yonse ya zokopera, ife tikudziwa zimenezo, pafupifupi kuti zikanyenge Osankhidwa ngati nkotheke. Muone momwe chinthu chonsecho chikupitira ndi Mawu, ndiye inu mudziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi. Koma, apobe, Yesu akadali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

⁵²⁷ Ndi angati muno amene akudwala, ndipo mukudziwa kuti ine sindikukudziwani inu? Kwezani mmwamba dzanja lanu, ndikuti, “Ine—ine ndikudziwa kuti inu simukundidziwa ine.” O, izo basi, ine ndikuganiza, paliponse. Chinthu chokha chimene inu mukuyenera kuchita ndi kungokhulupirira izo.

Kungo khulupirira, kungo khulupirira,
Zinthu zonse ndi zotheke, kungo khulupirira;
Kungo khulupirira, kungo khulupirira,

Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira.

528 Yesu anati, “Monga zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso kudzakhala pamene Mwana wa munthu adzaululidwa pa dziko lapansi mu tsiku lotsiriza. Pamene Mwana wa munthu ati adzawululidwe, kapena, kudziulula Yekha mu tsiku lotsiriza.” Tsopano, osati masiku akale, masiku apakati; tsiku lotsiriza, mukuona, Iye adzadzulula. Ndipo tsopano ife tiri mmasiku otsiriza. Sodomu akukhala ndendende basi, chirichonse, amthenga, mofanana basi.

529 Chinachitika ndi chiyani kwa a—wotsalira wapang’ono amene anaitanidwa atuluke limodzi ndi gulu la Abrahamu? Panali Mmodzi amene anabwera pakati pawo, mu thupi la munthu; anaimiriridwa mu mnofu wa munthu, akudya ndi iwo, kumwa ndi iwo, chakudya chomwecho chimene iwo ankadya, chirichonse. Iye anayima pakati pawo, anawawuza Uthenga. Kenako Iye anati, “Ine ndidzachita chinthu chachikulu ichi.”

530 Ndipo Abrahamu anapitiriza kuphunzira, “Kodi ndi ichi? Ndakhala ndikufunafuna Mzinda. Kodi Mfumu yake ndi ameneyu?”

531 Ndipo Iye anati, “Nchifukwa chiyani Sarah anakayikira ichi?” Mu hema, kumbuyo kwa Iye.

532 Abrahamu anati, “Ambuye Mulungu, Elohim!” Chifukwa, Iye anazindikira maganizo a Sarah.

533 Yesu anati izo zidzabwereza kachiwiri pamene Iye ati azidzaululidwa mu tsiku lotsiriza, Mwalawapamutu ukubwera mu Thupi. Kuti adzawombole a . . . Amenewo ndi owomboledwa, akubwera kudzatenga Ake Omwe. Iye ali pano ndi ife.

534 Tsopano, pali pafupifupi manja thwelofu okha, kapena opitirira, anakwera mmwamba. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiritsa aliyense wa inu. Kulondola. Ine ndikukhulupirira inu mukutero. Ine sindikukhulupirira kuti munthu akhoza kukhala pamalo ngati awa popanda . . . mu nthawi ya mtundu uwu, ndi chikhalidwe ichi, popanda kudziwa, kuzindikira chinachake.

535 Ine ndikufuna kuti inu mupemphere. Ine ndikufuna kuti inu mutenge chimene chiri cholakwika ndi inu, mu—mu—mu mtima mwanu, mwaona, ndipo mukatero muyambe kupemphera, munene kuti, “Ambuye Yesu, ululani izi. Ndine—ine ndikuyankhula kwa Inu chimene chiri cholakwika ndi ine. Ndipo tsopano Inu mutumize Mzimu Wanu Woyera kwa M’bale Branham, kuti akwaniritse chimene iye ananena kuti ndi Choonadi, mu Uthenga uwu umene iye walankhula lero za Inu, ine ndikudziwa kuti icho chikhala Choonadi. Tsopano, ululirani izo kwa ine, Ambuye. Yankhulani kwa ine.”

536 Tsopano iwo wamwazikana, zikukhala ngati ndi apa ndi pozungulira. Chotero mungopemphera, ndipo

mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse, kuti Mulungu apereka izo.

⁵³⁷ Tsopano ine ndikufuna inu muyang'ane pa ine, ndipo mupemphere. Monga Petro ndi Yohane ananenera, “Yang'anani pa ife.” Iye ankafuna chinachake, ndipo iye wangotsala pang'ono kuchilandira icho. Ndipo inu mukufuna chinachake, ndipo ine ndikukhulupirira kuti inu mwangotsala pang'ono kuchilandira icho. Iye anati, “Mutiyang'ane ife.”

⁵³⁸ Iye anati, “Siliva ndi golide, ine ndiribe aliyense; koma chimene ine ndiri nacho, ndikupatsa iwe.”

⁵³⁹ Tsopano, machiritso, ine ndiribe. Izo zonse ziri mwa Khristu. Koma chimene ine ndiri nacho, mphatso ya Mulungu, ine ndikupatsani inu, chikhulupiriro kuti mumukhulupirire Iye. Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, aliyense wa inu achiritsidwe. Mukhulupirire izo. Mukuona? “Ngati inu mungakhulupirire!”

⁵⁴⁰ Dona wakhala apo, akundiyang'ana ineyo. Iye amalira, maminiti pang'ono apitawo, akupemphera. Ali ndi vuto la chapakhosi limene likumuvutitsa iye. Ine sindikukudziwani inu. Ndinu mlendo kwa ine. Izo nzoona, sichoncho izo. [Mlongoyo akuti, “Uko nkulondola.”—Mkonzi]. Sindinu wochokera kuno. Ndinu wochokera ku Chicago. Akazi a Alexander. Ngati uko nkulondola, gwedezani dzanja lanu. Tsopano bwererani ku Chicago ndipo mukakhale bwino.

⁵⁴¹ Kodi iye anakhudza chiyani? Chinthu chomwecho chimene mkazi wa vuto la magazi anachikhudza, mphonje ya chovala Chake, osati changa.

⁵⁴² Apa pali dona wamng'ono wakhala pansu pomwe pakati pa unyinj, ngati ine ndingakhoze kumupangitsa iye kuti andimvetsetse ine. Inu amene munakweza mutu wanu chambali. Ine sindikukudziwani inu. Ndinu mlendo kwa ine, koma inu mukuvutika ndi vuto la mmimba. Amuna anu akhala pafupi ndi inu. Iye ali ndi chinachake cholakwika ndi khutu lake. Dzina lanu ndi Czap. Ndinu alendo kwa ine. Sindinu ochokera kuno. Ndinu ochokera ku Michigan. Uko nkulondola, gwedezani manja anu. Mubwerere ku Michigan, wabwino. Chikhulupiriro chanu chakupangani inu wamphumphu. “Ngati mungathe kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheka.”

⁵⁴³ Dona wamng'ono apo ali ndi vuto la mmero, wakhala kumbuyo komwe kuno kumapeto, wochokera ku Georgia, wavala zoyera. Bwererani uko, ku Georgia, wabwino. Yesu Khristu wakuchizani inu. Kodi inu mukukhulupirira izo?

⁵⁴⁴ Dona wakhala apoyo, akundiyang'ana ine, kumapeto komwe kwa mpando. Iye ali ndi vuto la chimfine. Iye akakhulupirira izo, Mulungu amuchiza iye. Akazi a Brown, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, Yesu Khristu akupangani. . . Ndinu mlendo kwa ine, koma Iye amakudziwani inu. Uh-huh. Inu

mukukhulupirira zimenezo? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Izo nzoona.

⁵⁴⁵ Wagona apa pa machira awa. Muuzeni iye kuti ayang'ane kuno. Iye wakhala akuvutika, zikupitirirabe. Ngati ndingathe kumuchiza iye, ine ndingachite zimenezo, bwana. Ine sindingathe kuchiritsa. Iye si wochokera kuno; wachokera kutali. Ndiwe wochokera ku Missouri. Mavuto ako ndi amkati. Koma ngati ungakhulupirire ndi mtima wako wonse, ndipo osakayikira, Yesu Khristu akhoza kukuchiza iwe; ndipo iwe ukhoza kubwerera ku Missouri, utachira, ndi kukaperekera umboni wako. Iwe ukukhulupirira zimenezo? Ndiye landira zimenezo, ndipo unyamule machira akowo ndi kumapita kwanu. Yesu Khristu wakuchiza iwe.

⁵⁴⁶ Kodi inu mukukhulupirira? Chimenecho ndi chizindikiro cha Kukhalapo kwa Mfumu Yamuyaya. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo tsopano, ndi mtima wanu wonse? Tsopano, Iye ndithudi wapanga mkombelo, mozungulira kudutsa mchipinda chino. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo ndi mtima wanu wonse? Inu mukukhulupirira kuti inu muli mu Kukhalapo Kwake?

⁵⁴⁷ Tsopano, kodi inu mukukhulupirira ndi kuvomereza kuti ndinu mmodzi wa nthumwi za Ufumu uwu? Kwezani dzanja lanu. Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Ndife wina ndi mzake; ndinu gawo la ine, ndine gawo lanu; ndife tonse gawo la Khristu. Tsopano, pamodzi, tiyeni tiyike manja athu pa wina ndi mzake.

⁵⁴⁸ Pomwe pano, mkazi wa pa machira wadzuka, akuyendayenda, akubwerera kwawo kuti akakhale bwino. Ameni.

⁵⁴⁹ Inu, aliyense, wachiritsidwa, ngati inu muti mukhulupirire izo. Tsopano ikanani manja anu pa wina ndi mzake, ndipo inu ndinu gawo ili la Khristu. Inu mumupempherere munthu amene inu mwamuyika manja anu, basi momwe inu mukufunira kutero.

⁵⁵⁰ Ambuye Yesu, ife tikukuzindikirani Inu pano. Ndinu Mfumu yathu; Inu mukuzidzindikiritsa Nokha pakati pathu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Kukhalapo uku. Ndipo, Ambuye, Inu munati, “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ musakayikire izo; mudzakhulupirire kuti chimene mwanenacho chidzachitika, inu mukhoza kulandira icho, inu mukhoza kukhala nacho chimene inu mwanena.”

⁵⁵¹ Ndiye, pomvera lamulo ili, pomvera Mawu a Mulungu amene sangalephere, ife monga nthumwi Zanu zochokera mailosi fifitini handiredi mbali zonse zonse, mofanana ndi Mzindawo, ife tikunena kwa Satana, mdierekezi wogonjetsedwayo, “Mapeto ako ndi kukawotchedwa. Ife ndi nthumwi zochokera ku Mzinda umene uli wa mbali zinayi zofanana, Mzinda

umene Mwanawankhosa ndiye Kuwala. Ife ndi chikhumbo chofotokozedwa cha Mulungu Wamphamvuzonse, amene Yesu Khristu wamuwombola mwa chisomo Chake.”

⁵⁵² Satana, tuluka, ndipo umusiye munthu wodwala aliyense amene ali muno, mu Dzina la Yesu Khristu. Manja oyera amene awomboledwa, chifukwa iwo akukhulupirira Mawu ndipo ndiwo zikhumbo za ganizo la Mulungu, tsopano manja amenewo ali pa wina ndi mzake. Iwe sungathe kuwagwiranso iwo kenanso. Tuluka, mu Dzina la Yesu Khristu!

⁵⁵³ Tsopano, mu Dzina la Ambuye Yesu, tsopano, Iye ali pano. Mawu Ake akuti Iye ali pano. Kukhalapo kwanu ndi chikhulupiriro chanu zikuyankhula, za, kuti ndinu mmodzi wa nthumwizo. Ngakhale muyeso uliwonse wadera umene ife tingasonyeze, uli chomwecho. Kodi inu mukukhoza kuzindikira kuti ndinu ana aamuna ndi aakazi owomboledwa a Mulungu? Inu mukuzindikira kuti *uko* ndi Kwanu? *Uko* ndi kumene inu mukupita.

⁵⁵⁴ Ndi chifukwa chake inu mwabwera kuno, ndi chifukwa inu mumabwera kwa Khristu, inu mukudya pa Mawu Ake. Ndipo ngati inu mungakhale ndi nthawi ngati iyi, pano, basi podzera mu zikhumbo Zake zofotokozedwa, zidzakhala motani pamene ife tidzabwere mu Kukhalapo Kwake? Oh, zidzakhala zopambana! Aliyense wa inu ali ndi ufulu wochiritsa odwala, kuyika manja anu pa odwala. Mmodzi aliyense wa inu ali ndi ufulu wobatiza.

⁵⁵⁵ Ngati winawake ali pano amene sanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, dziwe ndi lotsegula.

⁵⁵⁶ Imeneyo ndi njira yokhayo imene inu muti mupangire izo, uh-huh, uko nkulondola, ndiko kumvera Mawu aliwonse. Kumbukirani, gawo limodzi laling’ono la Mawu, pachiyambi, linayambitsa tchimo lililonse pa dziko lapansi. Yesu anati, “Aliyense amene ati adzachotse Mawu amodzi kwa Awa, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, sadzalowa.” Dzina lake lachotsedwa mu Bukhu, mwamsanga pamene iye adzachita zimenezo.

⁵⁵⁷ Ndipo palibe malo mu Baibulo pamene aliyense anayamba wabatizidwapo, mu Tchalitchi, mwanjira iliyonse kuposa mu Dzina la Yesu Khristu. Ngati inu simunabatizidwe mwanjira imeneyo, inu kulibwino muchite zimenezo.

⁵⁵⁸ “Oh,” inu mukuti, “izo sizimapanga kusiyana kulikonse.” Izo zinatero kwa Eva.

⁵⁵⁹ Satana anati, “Oh, ndithudi, Mulungu, inu mukumudziwa Mulungu. . .” Koma, Iye anatero. Iye ananena chomwecho.

⁵⁶⁰ Iye anamupatsa Petro mafungulo aku Ufumu, ndipo chimene chinamangidwa pa Pentekoste ndi chomangidwa kwanthawizonse. Ndi chifukwa chake Mkwatibwi anabwera

mu chiwonetsero kenanso, nthawi yachiwiri; pakuyenera kuti pakhale Mpingo woyitanidwa utuluke kuchokera mu tsiku lotsiriza, monga zinachitikira mu tsiku loyamba, chimodzimodzi basi. Mtengo wabwera kuchokera ku mizu yake, mpaka ku Mtengo wa Mkwatibwi, monga iwo unachitira mu nthawi imeneyo; mbambande ya Mulungu kachiwiri, monga ine ndinanenera ma Lamlungu awiri apitawo, kuti itengedwere ku Mzinda.

Mulungu akudalitseni inu. “Ine tsopano ndikukhulupirira.”

⁵⁶¹ Satana wagonjetsedwa. Iye akudziwa. Iye ali padziko lapansi, iye akupita ngati mkango wobangula. Sipatenga nthawi yayitali mpaka iye, oh, iye wathedwa. Iye akudziwa nthawi yake. Iye akupita ngati mkango wobangula.

⁵⁶² Koma, kumbukirani, Kalonga wa Mtendere wayima pafupi; Mmodzi Wamkulu Waumulunguyo. Womanga wa umunthu wanga, Womanga Amene anandimanga ine chimene ine ndiri, Amene anakumangani inu chimene inu muli, ali pano. Ngati Womanga, Amene amadziwa kuyika nyumbayo pamodzi, malo ake oyenera, ndani amadziwa bwinoko kuposa Womangayo? Ndipo Iye ali pano kuti adzatsimikizire, Iyemwini, Iye ali pano.

⁵⁶³ Tsopano izo zikukhazikika pa chikhulupiroo chanu. Khulupirani, mungokhulupirira! Uh-huh.

Ine ndikupita ku Mzinda wokongola uja
 Ambuye wanga wakonzera Ake Omwe;
 Kumene onse Owomboledwa a mibadwo yonse
 Adzayimba “Ulemelero!” kuzungulira
 Mpandowachifumu Woyera;
 Nthawizina ndimapukwa Kumwamba,
 (Pamene izi zonse zikadzatha!)
 Ndipo ulemelero Kumeneko ine
 ndidzawuwona:
 Chidzakhala chisangalalo chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ine ndidzawuwona,
 Mu Mzinda wokongola wagolide uja!

⁵⁶⁴ Kumbukirani, ku tchalitchi, usikuuno, iwo adzakhala akupereka mgonero. Ngati inu muli kuno mu mzinda, komabe, mukufuna kuti mubwere, ife tingakonde kukhala nanu inu. Ndi chikumbutso cha zomwe ife tidzakadye, limodzi la masiku awa, ndi Iye.

⁵⁶⁵ Ine ndimakukondani inu. Sindikudziwa momwe ndingazifotokozere izo. Ine ndikuganiza kuti ndinu mchere wa dziko lapansi. Ndipo ine ndimamva khalidwe lanu pakati pa dziko, ndiye izo zimandipatsa ine chidaliro chochuluka mwa inu.

⁵⁶⁶ Koma, taganizani, gulu laling’ono ili lidzatero, okondana monga momwe timachitira, lidzasweka, limodzi la masiku awa.

Ife tidzalota za izi. Koma ngati mmodzi wa ife adzapezeke kuti wamwalira tisanakumanenso, ife tidza . . .

Ndidzakumana nanu m'mawa, mmphepete
mwa mtsinje wonyezimira,
Pamene zisoni zonse zachoka;
Ndidzakhala ndikuima pafupi ndi zitseko,
pamene zipata zizidzatseguka,
Pamapeto pa tsiku la moyo lalitali, lotopetsa.

Ndidzakumana nanu m'mawa, m'mphepete
mwa mtsinje wonyezimira, (Ine ndatayika
ndiri pakati.)

. . .kumusi ku mtsinje ndipo ndi kudziwana
kwakale kwa mkwatulo kukutsitsimutsidwa;

Ine ndidzakuwonani inu ndiye, ndidzakudziwani inu.

Inu mudzandidziwa ine m'mawa, ndi
kumwetulira kumene ndimavala,
Ine ndidzacomana nanu m'mawa, mu Mzinda,
womangidwa mwamphwamphwa.

⁵⁶⁷ Inu mukuikonda iyo? “Mpaka tidzacomane!” Tsopano tiyeni tiyimirie. *Tenga Dzinalo La Yesu Ndi Iwu*, tipatseni ife poyambira.

⁵⁶⁸ Inu mumamukonda Iye? Kodi Iye si wodabwitsa? Kodi inu mukukhulupirira kuti ichi ndi Choonadi? Kodi inu mwalunjika njira imeneyo, mwa chisomo cha Mulungu? Mpaka tidzafike kumeneko:

Tenga Dzinalo la Yesu ndi iwe,
Ngati Chishango ku msampha uliwonse;
Ndipo pamene mayesero mokuzingani
asonkhana,
Mungopuma Dzina Loyeralo mu pemphero.

Ndizo zonse zoti tizichita, mpaka ife tidzakuwonneninso inu. Chabwino.

Tenga Dzinalo la Yesu ndi iwe,
Mwana wachisoni ndi . . . [Winawake akuti,
“Usikuuno?”—Mkonzi]. (Ayi.)

Idzakusangalatsani ndi kukutonhozani inu,
Litengeni llo kulikonse kumene mupita.

Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha mdziko ndi chisangalalo
cha Kumwamba;

Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha mdziko ndi chisangalalo
cha Kumwamba.

⁵⁶⁹ Tsopano, ine ndachita kulumpha Uthenga wanga. Tsiku lina, Ambuye akalola, ine ndidzabwereranso ndi kudzatenga

“tinjirati,” ndi kudzatitenga ito, mwaona, pamene ife tidzakhale ndi nthawi yochuluka. Inu mwakhala mukukuwa zakuti sitikukhala motalika kokwanira. Ife tatero, lero. Kukutentha. Koma, tsopano, Mulungu akudalitseni inu. Ine ndimakonda kuyimba kumeneko.

⁵⁷⁰ Woyandikana naye pano, ananena, usiku wina pamene iwo anazimitsa chimkuza mawu cha panja, anati, “Ine ndinawukonda Uthenga kwambiri, koma nchifukwa chiyani inu munazimitsa kuyimba kokongola kuja, mwaona, panjapo?” Chotero, woyandikana naye, ngati inu mukumvetsera mmawa uno, ine ndikuganiza ife tiri nawo oyandikana nawo abwino kwambiri amene alipo mu Jeffersonville. Timaimika magalimoto athu patsogolo pa nyumba zawo ndi china chirichonse; iwo samanena kanthu za izo; ife timangopitirira. Chotero, ife tikuwathokoza iwo tsopano.

⁵⁷¹ Oh, ndi wodabwitsa bwanji Iye! Mulungu akhale nanu tsopano.

. . . Dzina, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha mdziko ndi chisangalalo
cha Kumwamba.

Mpaka tidzakumane!

⁵⁷² Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Abusa atibalalitsa ife, mu mphindi zochepe chabe. Mulungu akhale nanu!

. . . tidzakumane pa mapazi a Yesu; (Pa Mzinda
wawukulu, Pampano wachifumu.)
Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!
Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomane. . .



64-0802 Kwawo Kwamtsogolo Kwa Mkwati Wa
Kumwamba Ndi Mkwatibwi Wapadziko Lapansi
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2025 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org